

# MAFUNSO NDI MAYANKHO PA MZIMU WOYERA



Ndipo utatha usiku watha ife tonse tangodzazidwa. Ine ndamva nkhani zabwino lero za ambiri omwe alandira Mzimu Woyera. Ndipo ndife okondwa chifukwa cha izo.

<sup>2</sup> Wokondwa kukhala kuti M'bale Graham ali ndi ife usikuuno, mmodzi wa oyanjana nafe kuno ochokera ku kachisi, m'busa wa mpingo wa chiyero uko ku Utica. Ndipo M'bale Jackson, iye anali kuno usiku watha, ine ndikukhulupirira ilo linali; kapena iye ali mmbuyo umo mwa omvetsera penapake tsopano, wina anatero. Inde, ine ndikumuwona M'bale Jackson mmbuyo mwa omvetsera tsopano. Ndi—ndi M'bale Ruddell, kodi iye ali muno usikuuno? Uyo ndi mmodzi wina wa oyanjana nafe kuno ku “62.” Ndife okondwa kukhala ndi iwo muno. Ndi athu . . . O, M'bale Pat, ndi abale ena onse awa, ndife—ndi uko mwa omvetsera. Ndife okondwa kukhala nanu nonse inu muno usikuuno.

<sup>3</sup> Tsopano, ngati ine ndikanati ndichilungamitse chinthucho, ine ndikanawabweretsa ena a alaliki abwinowa pano kuti adzayankhule kwa inu, chifukwa ine ndasasa mawu basi chifukwa chokhala ndi nthawi yaikulu usiku watha.

<sup>4</sup> Tsopano, mkazi wanga, iye ndi wondikonza wanga; inu mukudziwa, abale, chimene ine ndikuchikamba. Iye anati anthu mmbuyomo usiku watha samakhoza kundimva ine, chifukwa ine ndimayankhulira mu chinthu ichi. Ndipo tsopano, ine ndisanati ndiyambe, ine ndiyesera chinachake. Tsopano, ine ndikudabwa ngati apo ziri bwino. Kodi ziri bwino mwanjira iyo mmbuyomo? Kapena kodi chonchi ziri bwino? Kodi chonchi ziri bwino? Tsopano, Wokondedwa, ndiyo nthawi imodzi ndapeza chimodzi chokutsutsa iwe. Tsopano, iwo akuti umo ndiye ziri bwino. Chabwino. O, mai! Uyo ndi mkazi. Icho ndi chabwino, chifukwa yakhala ili nthawi yaitali kuchokera pomwe ine ndinakhala nacho china. Iye nthawizonse amakhala wolondola.

<sup>5</sup> Chabwino, ife ndithudi tinali ndi—takhala tiri ndi nthawi yaikulu pa msonkhano wa mausiku atatu awo; ine ndinali. Ndipo tsopano, matepi, onse kupatula usiku watha . . . Ine ndinamumbira M'bale Goad ndipo ndinamuuza iye kuti abwere kudzajambula tepi ya pa kachisi. Koma izo zinachitika kuti ine ndamva kuti Billy Paul anali atatenga galimoto yake ndipo atapita, chotero tepiyo siinajambulidwe momwe ine ndikudziwira. Chotero ife tiuphonya umenewo. Ine ndikanakonda ndikanadzaisunga iyo mu tchalitchi

chifukwa cha mpingowu—kwa wina atati—chomwe ife timachikhulupirira.

<sup>6</sup> Tsopano, usikuuno ine ndikuti ndiyankhule pa *Msonkhano Waukulu*, ngati ine ndingakhoze kutsiriza mafunsowa mu nthawi. Ndiyeno, mawa mmawa ndi msonkhano wa machiritso. Ndipo ife tikuti tiwapempherere odwala. Chotero, ife sitingakhoze kupereka—kapena kungopita ndi kukati, “Tsopano, ine ndati ndikutengeni inu, ndi inu, ndi inu.” Izo sizikanati zikhale zabwino. Koma ife tipereka mulu wa makhadi, ndipo penapake potsatira makhadi amenewo, ine ndidzaitanira angapo pa nsanja. Ndiyeno, ngati Mzimu Woyera uyamba kuwulula, ndiye Iwo umapita uko kudutsa mwa omvetsera ndi kukawapeza anthu mwa omvetsera kwa utumiki wa machiritso. Ndiyeno, mawa mmawa, ine ndidzakhala ndikuyankhula, Ambuye akalola, basi tisanayambe msonkhano wa machiritso.

<sup>7</sup> Ine ndikumuwona mkazi wanga akuseka. Wokonedwa, kodi iwe sukukhoza kundimva ine nkomwe? O, iwe ukundimva ine. Chabwino, ziri bwino. Iye amakhala kumbuyo mmbuyo ndipo ngati nkuti—sakukhoza kundimva ine, iye amagwedeza mutu wake, “Iwe . . . Sindikukhoza kukumva iwe, sindikukhoza kukumva iwe.”

<sup>8</sup> Ndiyeno mawa—mawa usiku ndi utumiki wa ulaliki limodzi ndi utumiki wa ubatizo wa madzi. Ndiyeno, mwamsanga pamene ine ndidzatsiriza kulalikira mawa usiku, ife tidzakokera pansi makatani ndi kudzakhala ndi ubatizo wa madzi muno mawa usiku. Ngati Ambuye alola, ngati Ambuye alola, mmawa ine ndikufuna—kapena mawa usiku ine ndikufuna ndidzayankhule pa phunziro: *C—Chizindikiro Chinaperekedwa*. Ndiyeno, ngati ife tidzakhala pano Lachitatu usiku, ngati Ambuye adzandilola ine kuti ndidzakhale pano Lachitatu usiku, ine ndikufuna kuti ndidzayankhule pa phunziro: *Ife Taiwona Nyenyezi Yake Kummawa ndipo Tabwera Kudzampembedza Iye*. Tsopano, ndizo basi usanafike usiku wa Khristimasi.

<sup>9</sup> Ndiyeno, mwamsanga ikatha Khristimasi ndi sabata la tchuthi cha Khristimasi. Apo ndi pamene ife titi tidzatenge makalata onse . . . M’bale Mercier ndi iwo kawirikawiri amawatulutsa onsewo. Ndipo ife tidzawayala iwo onse apo, ndipo ife tidzawapempherera makalata awa ndi kuwapempha Ambuye kuti atitsogolere ife komwe kuli koyenera kudutsa mdziko komwe ife titi tidzapiteko.

<sup>10</sup> Tsopano, Amuna Amalonda Achikhristu ali ndi mndandanda waukulu, tiyenera kukakhala mu Florida mwamsanga ku msonkhano wao. Tidzapita kuchokera uko ku Kingston, ndiye mpaka ku Haiti, ndipo kutsika mpaka ku Puerto Rico, kulowa mu South America, kubwererako podzera mu Mexico.

<sup>11</sup> Koma Ambuye akuwoneka kuti akunditsogolera ine ku Norway. Ine sindikudziwa chifukwa chake. Inu mukulidziwa bukhu laling'ono lotchedwa *Mwamuna Wotumidwa Kuchokera Kwa Mulungu?* Ndi bukhu lalikulu kwambiri lachipembedzo mu Norway. Taganizani za zimenezo, chimene Ambuye achita uko. Ndipo pamene ine ndinali uko, iwo samandilola ine kuyika manja pa odwala. Ine ndinali uko kwa mausiku atatu. Ndipo iwo samandilola ine kuika manja pa odwala. Chotero inu mukuona chimene Mulungu akhoza kuchita. Unyinji unali waukulu kwambiri iwo anachita kutenga apolisi okwera, akavalo, ndi kumawayendetsa anthu achoke mmisewu kuti ine ndikhoze kukafika ku maloko. Ndipo ine sindinayike manja pa odwala. Ine ndimangowapempherera iwo basi; nkuwasiya iwo ayikane manja wina ndi mzake.

<sup>12</sup> Chotero... [Winawake akuyankhula ndi M'bale Branham—Mkonzi.] Eya, ine ndithudi ndidzatero, ndiye Tsopano, mawa mmawa... Tsopano, usikuuno, mwina ife tingolowa mu mafunso awa, chifukwa ife tiri nawo ena abwino kwenikweni. Ndipo ine sindikudziwa utali wake womwe Ambuye ati atisunge ife pa izo. Ndiyeno, mawa mmawa mwina Billy Paul, Gene, kapena Leo, wina, adzakhala pano kuti azidzapereka makadi a pemphero pa eyiti koloko mpaka hafu pasiti eyiti. Tsopano, anthu a kunja kwa tawoni, mundilole ine ndichinenenso icho kuti inu musati muiwale. Ngati inu mukufuna kuti mudzabwere mu mzere, ife ndibwino tidzakhale ndi anthu a kunja kwa mzinda ngati nkotheke.

<sup>13</sup> Tsopano, nthawizina kuno mu tchalitchi ife timafika pa malo amene iwo amati, “Chabwino...” Ife timawatenga anthu a kunja kwa tawoni, kuwabweretsa iwo... Wina amati, “Chabwino, ine sindimadziwa chomwe chinali cholakwika ndi iwo. Iwo mwina amanena chinachake cholakwika.” Ndiye iwe ukatenga anthu mu tawoni; iwo amati, “O, inu mwina mumawadziwa iwo.” Kotero... Ndiye iwo amati—izo zakhala zikunenedwa, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu, ndi makadi a pempherowo.” Chabwino, nanga bwanji awo amene alibe makadi a pemphero. Ndipo zakhala ziri tsiku ndi tsiku pamene izo...

Mukuti chiani? [M'bale Branham akufunsidwa kuti aime mmbuyo kuchoka ku choyankhulira—Mkonzi.] Ndiime patali ndi choyankhulirapochi? Chabwino, inu mukudziwa, ine nthawizonse ndimalalikira pakati pa msewu. Chotero mwina ine ndingozitenga izo monga choncho. Kodi ziri bwino apo? Ziri bwino. Ndizo zabwino. Ine ndikuuzeni inu chomwe chiri. Zoyankhulira kugulu zathu—zathu nzosauka muno, zosauka kwambiri. Ndipo ife sitiri kuyesera kuti tikhale mwabwinoko mulimonse tsopano, chifukwa ife tikufuna kachisi watsopano amangidwe pompano. Ndipo apo ndi pamene ife titi tidzakhale nawo malo ochuluka (mukuona?), ngati ife tingakhoze kubwera

pano ndi kudzawatambasula malo ano mokulitsa pang'ono, ndi kudzayikamo malo ena owonjezera, ndi kukonzekera misonkhano pamene ife titi tidzakhale nayo kuno.

<sup>14</sup> Ndipo tsopano, kumbukirani, mmawa anyamata, mmodzi kapena atatu a iwo adzakhala akupereka makadi pakati pa 8:30—kapena 8:00 ndi 8:30. Izo zikupereka mwayi kwa aliyense kuti adzakhazikike. Ndipo ine ndinali kuyankhula pa za momwe iwo amaperekeram makadi, chifukwa chomwe ife timachitira izo. Nkuti tizisunga dongosolo. Mwaona? Tsopano, nanga bwanji ine ndikanabwera muno, basi monga pakali pano nkuti, “Mulole mkazi *uyu*, mkazi *uyu*, ndi bambo *uyo*, ndi mkazi *uyu* . . .?” Inu mukuona, izo zikanakhala ngati—izo zikanakhala ngati zovuta. Mwaona? Ndiyeno, ngati inu . . . Nthawi zambiri ine ndachitapo izi. Ndipo ngati iwo sali ochuluka kwambiri mmawawu, ine mwina ndikhoza kuchita chinthu chomwecho. Ine ndimati, “Ndi anthu angati muno ali ochokera kunja kwa mzinda omwe ali ndi chinachake cholakwika ndi inu, inu muimirimire.”

<sup>15</sup> M'bale Mercier, inu mubwere kudzandipulumutsa. Inu mudzandithandiza ine? [M'bale Mercier akuyankha—Mkonzi.] O, inu mubwera . . . Iye abwera kudzadzipulumutsa yekha. Ine ndinayankhula kwa bwenzi wanu wamkazi lero. Tsopano, inu muyenera kuti muzikhala wabwino kwenikweni kwa ine. Mwaona? Chabwino. Izo nzabwino. Ine—ine ndikuyamikira kulimbamtima uko M'bale Leo. Pamene izo siziri bwino, tiyeni—tiyeni tizikonze izo bwino monga ife tikudziwira kuzifikitsira izo, mopambana momwe ife tingakhazere.

<sup>16</sup> Chotero tsopano ndiye, timangowafunsa anthu a kunja kwa mzinda kuti akweze mmwamba manja awo omwe ali nacho chinachake cholakwika nawo. Ndiyeno iwe umaima apo, nkukhazikika pa munthu mmodzi mpaka Mzimu Woyera ufike poyamba, ndipo nkuwatenga omvetsera onsewo. Ndi angati akhalapo ali muno pamene iwo anaziwona izo zikuchitidwa munomo? Zedi! Mwaona, mukuona? Chotero ziribe kanthu kuti ziri mbali iti. Ndi basi . . .

<sup>17</sup> Ine ndikufuna kuti inu mukumbukire izi, ndipo ine ndiyesera kuti ndidutse mu izo mmawa kachiwiri. Amitundu, Uthenga umene waperekedwa kwa iwo ndi Uthenga wa chikhulupiriro, osati wa zintchito konse. Mukuona? Ndipo monga ine ndinanenera usiku watha. Pamene Mzimu Woyera unagwa pa Pentekoste, pamene iwo anapita uko kwa Ayuda (Machitidwe 19:5), iwo ankachita kuyika manja pa iwo kuti iwo aulandire Iwo. Ndipo pamene iwo anapita ku Samaria, iwo ankachita kukaika manja pa iwo. Koma pamene iwo anabwera kwa Amitundu ku nyumba ya Kornerio, “Pamene Petro anali akuyankhula mawu awa . . .” Osati kuyika kwa manja.

<sup>18</sup> Pamene msungwana wamng'ono anafa, mwana wamkazi wa Yairo, wansembe, anati, “Bwerani mudzaike manja pa iye,

ndipo iye akhala moyo.” Koma pamene kenturio wachi Roma, Wamitundu, anati, “Ine sindiri woyenera kuti Inu mubwere pansu pa denga langa, yankhulani mawu.” Ndi zomwezo. Mwaona?

<sup>19</sup> Mkazi wachi Surofonisia, Mherene kwenikweni chimene iye anali, pamene iye—pamene Yesu anati kwa iye, anati, “Sizoyenera kwa Ine kuti nditenge mkate wa ana ndi kuupereka kwa agaru.”

Iye anati, “Izo nzoona, Ambuye; koma agaru pansu pa gome amadya nyenyetswa za ana.”

Iye anati, “Chifukwa cha kuyankhula uku, mdierekezi wamusiya mwana wako wamkazi.” Muzinena zinthu zabwino ndiye. Muzinena zinazake zabwino zokhudza winawake. Muziyankhula za Yesu. Muzinena chinachake chomvera, chinachake chenicheni. Ndiyo njira yochotsera adierekezi. Iye sananene konse—Iye sanampempherere konse msungwanayo. Iye sananene konse kanthu kamodzi zokhudzana ndi kuchiritsidwa kwake; Iye anangoti, “Chifukwa cha kuyankhula uku, chifukwa cha kuyankhula uku. . .”

<sup>20</sup> Hattie Wright, tsiku lina, iye sanapemphe kalikonse. Iye anali atangokhala pamenepo, koma iye ananena chinthu choyenera, chimene chinaukondweretsa Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu Woyera unayankhula moyankha nkuti, “Hattie, pempha chirichonse chimene iwe ungafune, chirichonse chimene iwe uli nacho ndipo ukuchifuna. Kafufuze ngati izi ziri zenizeni kapena ayi. Pempha chirichonse (machiritso a mchemwali wake wamng’ono wolumala atakhala apo yense atawunjikika pamodzi; madola zikwi khumi kuti iye asiye kumakakumba pa mapiri awo kumeneko; unyamata ubwezeretsedwe kwa thupi lake logujumulidwa kwambirilo); chirichonse chimene iwe ukufuna kuti upemphe, iwe uchipemphe icho pakali pano. Ngati Iwo subwera ndi kudzakupatsa iwe icho pomwe pano, ndiye ndine mneneri wabodza.” Ndicho—ndicho—ndicho chinachake, sichoncho izo?

<sup>21</sup> Yesu anati, “Nenani kwa phiri ili. . .” Ndipo inu mwamvapo—zokhudza zomwe zakhala zikuchitika; umenewo ndiwo utumiki umene ife tiri kulowamo. Ife tiri patali mu njirayi tsopano. Posachedwa Kudza kwa Ambuye Yesu. Ndipo ife tiyenera kuti tikhale nacho chikhulupiriro chokwatulitsa mu Mpingo umene ungakhoze kusinthidwa mu kamphindi mu kuthwanima kwa diso kuti tizipita, kapena ife sitidzapita. Koma musati mudandaule, iwo udzakakhala ulipo. Iwo udzakakhala ulipo. Ndipo pamene mphamvu ya mpingo *uwu* ikwera, iwo udzawabweretsa abale ake; mphamvu ya mpingo *uwo* ikakwera, udzawabweretsa abale ake; mphamvu ya mpingo *uwo* udzawabweretsa abale enawo; ndiye kudzakhala chiukitsiro cha aliyense. Ndipo ife tikuyang’anira ku zimenezo.

<sup>22</sup> Tsopano, musati muiwale, makadi apemphero mmawa pa 8 koloko mpaka 8:30. Ndiye ine ndidzawafunsa iwo aliwonse omwe alimo, ndiye adzangosiya kupereka makadi, ndi kupitirira kumka mmbuyo, ndi kukakhala pansa (mwaona?), chifukwa iwo adzakhala atapereka onse mwina pofika nthawi imeneyo mulimonse, kapena ochulukana monga omwe ife titi tidzawatenge kuchokera uko penapake. Anyamata adzabwera, kudzasakaniza makadi onsewo pamaso panu pomwe, ndiye ngati inu mukufuna imodzi, inu mukufuna imodzi, kapena choonjezera china chirichonse monga choncho. . . Ndiye pamene ine ndibwera umu, ine basi. . . Paliponse pamene Ambuye ati itana kuchokerapo. . . Ndipo ngati Iye ati, “Usawaitane konse,” Ine sindiwaitana iwo konse (mwaona?), basi chirichonse chomwe chiri.

<sup>23</sup> Ndipo ine ndiri. . . Utumiki umenewo wangotsala pang’ono kuti uzimirire mulimonse; pali chinachake chachikulupo chikubweramo. Kumbukirani, ndi pomwe nthawi iliyonse zakhala zikunenedwa kuchokera pa nsanja ino kapena pa guwa lino, ndipo izo sizinayambe zalepherapo panobe. Inu mukukumbukira utumiki wa dzanja? Mukuona chimene iwo unachita? Malingaliro a mtima, mukuona chimene iwo unachita? Tsopano penyani ichi: kuyankhula Mawu, ndipo muwone chimene Iwo akuchita. Mukuona? Ine ndinakuuzani inu kuno zaka zapitazo—mpingo (ine ndikuyankhula kwa a pa kachisiyu)—zaka zapitazo, zaka zitatu kapena zinai zapitazo, chinachake chinali kukonzekera kuti chiwonekere; icho chikukonzekera kuti chichitike. Ndipo ndi ichi tsopano kulowa mkati momwemu. . . Icho chiri kudziumba chokha apa. Tsopano, ndife oyamikira chifukwa cha izo. O, momwe ife tiri othokozera. Okondwa basi.

<sup>24</sup> Tsopano, ife tiri ndi mafunso ena olimba kwambiri pano, ndipo ife tikufuna kuti tilowe kumene mwa iwo. Winawake anayang’ana pa mabuku onse awa omwe ine ndiri nawo. Ine ndinati, “Chabwino, munthu wanzeru amangosowa limodzi.” Koma ine sindine munthu wanzeru. Ine ndimayenera kuti ndikhale nawo ochulukana a iwo oti ndiziyang’anamo. Chabwino, ili ndi *Diaglott*, ndipo ili ndi Baibulo, ndipo ili ndi lolongosola. Chotero ziri. . . Ife tati tingowapempha Ambuye kuti atithandize ife ndi kutilondolera ife kuti tiwayankhe mafunso awa basi molingana ndi chifuniro Chake Chaumulungu ndi Mawu Ake.

<sup>25</sup> Chotero tsopano, tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kwa mphindi yokha ya pemphero. Ambuye, ife tiri oyamikira kwa Inu kuchokera mu kuya komwe kwa mtima wathu pa zomwe Inu mwatichitira ife mu masiku atatu athawa. O, kuwaona atumiki akusonkhana kumbuyo uko mu chipinda ndi kumagwirana manja, ndi chikhulupiriro chotsitsimutsidwa, ndi—ndi sitepe yatsopano yoti aitenge. Kuitana pa foni. . . Ndipo mitima yathu ikusangalala, ndi anthu akulandira Mzimu Woyera iwo atatha—

kuwaona Mawu Anu, momwe Iwo akufotokozera ndendende sitepe ndi sitepe momwe angalandirire Mzimu Wanu Woyera. Ife tiri othokoza kwambiri chifukwa cha izo, Ambuye.

<sup>26</sup> Inu mukuzipanga zinthu kuphweka kwambiri kwa ife, chifukwa ndife anthu ophweka. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, ku—kuti Inu mutilola ife kwathunthu tizidzipanga tokha nthawizonse kukhala ophweka. Pakuti ndiwo... Ndiwo mtundu umene umadzichepetsa wokha umene uti udzakwezedwe. Ndipo nzeru ya mdziko ndiyo kupusa kwa Mulungu; kuti zinamukondweretsa Mulungu kupyolera mu kupusa kwa kulalikira kuti aziwapulumutsa iwo amene ali otaika.

<sup>27</sup> Ndipo tsopano, Atate, alipo pano omwe ndiri nawo mafunso angapo omwe afunsidwa ochokera mu mitima yodzipereka yomwe yakhudidwa. Ndipo limodzi la iwo litayankhidwa molakwika zikhoza kumuponyera munthuyo njira yolakwika, kuti uponyere kuwala kolakwika pa funso lawo limene likuwasautsa iwo. Chotero Ambuye Mulungu, ine ndikupemphera kuti Mzimu Wanu Woyera usunthire pa ife ndipo uwulule zinthu izi, pakuti zinalembedwa mu Malemba, “Pemphani ndipo inu mudzalandira; ndi funani ndipo inu mudzapeza; gogodani ndipo zidzatsegulidwira kwa inu.” Ndipo ndi chimene ife tikuchita tsopano, Ambuye, kugogoda pa khomo Lanu la chifundo. Titaima mu mthunzi wa chilungamo Chanu Chaumulungu, ife tikuchonderera Magazi a Khristu wa Mulungu ndi kwa Mzimu Woyera.

<sup>28</sup> Ndipo ife sitikubwera usikuuno kungoti chifukwa ife tachokera ku usiku utatu uja wa kulalikira pa Mzimu Woyera, ife tikubwera ndi kuya kwa kulemekeza kwambiri ndi kuonamtima. Ife tikubwera ngati kuti uwu ndi usiku wotsiriza womwe ife titi tidzakhale nawo konse pa dziko lapansi. Ife tikubwera tikukhulupirira kuti Inu muyankha mapemphero athu. Ndipo Ambuye, ife tikukupemphani Inu tsopano kuti mutikhutitse ife ndi Moyo Wanu Wamuyaya. Ndi pa kuyankha kwa Mawu Anu, mulole Mzimu Woyera... O Mulungu, monga ife tinapeza kuti ndi Inumwini pakati pathu, ife tikupemphera kuti Iye aululire kwa ife usikuuno zinthu zomwe ife tikuzikhumba. Ndipo ife tikukhumba kokha kuti miyoyo yathu ikhoze kukhala pa mpumulo, ndi malingaliro athu pa mtendere, ndi kukhala nacho chikhulupiriro mwa Mulungu kuti tiziyenda chamtsogolo kuti tiwatenge madalitso omwe Iye anawalonjeza. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>29</sup> Tsopano, ine ndiri nawo mafunso onse omwe anaperekedwa kwa ine, kupatula limodzi. Ndipo ine ndinamuyankha M'bale wamng'ono Martin yemwe anandifunsa ine funso usiku wadzana, limodzi lokha. Analipo ambiri muno usiku watha, koma awo anali opempha pemphero. Ndipo M'bale Martin anandifunsa ine funso lokhudza Yohane 3:16—kapena Yohane 3,

ine ndikukhulupirira, la, “Kupatula ngati munthu abadwa mwa madzi ndi mwa Mzimu, iye sangakhoze kuwuona Ufumu,” ndipo amafanizitsa izo ndi tepi yomwe ine ndinaitumiza ya Ahebri. Ndipo ine ndinakomana naye iye mu chipinda cha kumbuyo kuno usiku watha, ndipo—ine ndisanakhale nawo mwayi woti ndimuyankhe iye, ndiyeno ine ndinazichita apo, pa phunzirolo.

<sup>30</sup> Tsopano, kodi alipo wina pano yemwe sanali pano usiku watha, tiyeni tiwone manja anu, omwe sanali pano usiku watha. O, ife zedi timakhumba inu mukadakhala ndi ife. Ife tinali ndi nthawi yaulemerero chotero. Mzimu Woyera . . .

<sup>31</sup> Ine mwina, kwa miniti yokha. . . Izi sizipweteka. Izi zikujambulidwa. Ndipo ngati mtumiki aliyense apezeka kuti—kapena munthu yemwe ati apezeke kuti sakugwirizana pa zomwe ine ndikukonzekera kuti ndinene tsopano, kapena ngakhale mu mafunso, ine ndikupempha, m’bale, inu musaganize kuti icho ndi chachilendo, koma kuti—kumbukirani kuti tepi iyi ikupangidwa mu kachisi mwathu muno. Ife tikuphunzitsa kwa anthu athu. Atumiki ochuluka a zikhulupiriro zosiyana akhala pano. Ndipo ine ndikufuna kuti ndilowe mu phunzirolo kachiwiri, pakuti alipo ena a anthu athu omwe sakanakhoza kulowa muno usiku watha amene ine ndikuwawona ali muno usikuuno. Ndipo ine ndikanafuna kuti ndidutsemo mphindi yokha, ngati inu mungandiloleze izo, pa zomwe ine ndinayankhula usiku watha; ndipo izo zinali pa Pentekoste, pa kulandira Mzimu Woyera.

Tsopano, powerenga kuchokera mu *Emphatic Diaglott* ya kumasulira kwa Chigriki, pamene ine ndinali usiku watha, lomwe liri chitsegulire patsogolo panga tsopano. Ndiko kumasulira kwa pachiyambi kuchokera ku Chgriki kupita ku Chingezezi. Ilo silimadzera mwa omasulira ena, ndi—ndi kumasulira kwina, ndi lolunjika basi kuchokera ku Chigriki kupita ku Chingezezi. Tsopano, mawu Achingezezi, nthawi zambiri ali ndi matanthauzo otero kwa iwo, monga ngati ine ndikanati tsopano, *board*. Mukawatenga mawu awo a *board*. Inu mukanati, “Chabwino, iye amatanthauza kuti ife *timamutopetsa* iye.” Ayi! “Iye—iye analipira *gulu* lake.” Ayi! Chabwino, iye. . . “Ndi *bolodi* ili ku mbali ya nyumba.” Chabwino, mukuona? Kapena chirichonse cha izo. . . Alipo mawu anai kapena asanu osiyana angakhoze kugwiritsidwa ntchito; iwe umayenera kuti umvetse chiganizochi. Mawu oti *see*. *See* amatanthauza “kumvetsa,” mu Chingezezi. *Sea* amatanthauza “chikhamu cha madzi.” *See* amatanthauza “kuyang’anapo.” Mwaona? Koma pa kumasulira uku, mawu amene agwiritsidwa ntchito apa, omwe ine ndinawayankhula usiku watha mu Machitidwe mutu wa 2, pamene amati. “Malirime amoto anakhala pa iwo. . .” Tsopano, ine ndikukhumba ndikanangobwerera mmbuyo mphindi yokha. Kodi inu mungakonde kutero, mphindi yokha, ndi kukhala



ngati kuzibwereza izo kwa mphindi ife tisanapite patsogolo paliponse?

<sup>32</sup> Tsopano, tembenezirani, inu mu King James lanu kapena kumasulira kulikonse kumene inu mukuwerenga kuchokeramo...Ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge izo. Ndipo mumvetsere mwatcheru kwenikweni tsopano. Musati mumvetse molakwika. Ochuluka lero, ngakhale mlongo wanga, ambiri a iwo anaimba, anati... Akazi a Morgan... Ambiri a iwo analimo usiku watha. Akazi a Morgan ndi mmodzi wa alongo athu yemwe analepheredwa; ndipo iye anali pa mndandanda wa okufa mu Louisville kwa sikisitini, zaka seventini zapitazo ndi khansara. Ine ndikuganiza iye wakhala kumbuyo muno usiku unonso. Iye sanali kukhoza kumva, iye anati, chifukwa ine ndinali kuyankhula molunjika mu choyankhulira. Ndipo chifukwa cha iwo ine ndikufuna ndidutsenso mu izi kwa mphindi.

<sup>33</sup> Tsopano, ine ndikuwerenga kuchokera ku Lemba ili la Machitidwe 2:

... pamene Tsiku la Pentekoste Linadza Kwathunthu, anali onse mu lingaliro limodzi... (*Tsopano, ine ndikuzikonda izo bwinoko kuposa "chigwirizano chimodzi," chifukwa inu mukhoza kukhala a chigwirizano chimodzi pafupifupi pa phunziro lirilonse, koma pano malingaliro awo anali ofanana.*)... a lingaliro limodzi ndi pa malo omwewo.

Ndipo mwadzidzidzi apo panadza Phokoso lochokera Kumwamba, longa Mphepo ya nkokomo yachiwawa; ndipo iyo inadza Nyumba Yonseyo momwe iwo anali atakhala. (*Osati atagwada, osati akupempha, koma atakhala.*)

... Malirime ogawanika... (*M-a-l-i-r-i-m-e—malirime. Ogawanika kutanthauza "opatukana."*)... Malirime anawonekera kwa iwo, onga Moto, ndipo limodzi... (*"Limodzi," palokha.*)... linadzakhala pa aliyense wa iwo.)

Ndipo iwo onse anadzazidwa... (*"Ndipo," cholumikizira.*)... onse anadzazidwa ndi Mzimu woyera, ndipo *anayamba* kuyankhula *ndi malirime* Ena, momwe Mzimu unkawapatsira iwo zoyankhula.

Tsopano iwo anali *akukhala* mu Yerusalemu, Ayuda, Amuna *odzipereka, ochokera* ku Fuko Lirilonse la pansu pa Kumwamba.

*Pamene* ichi—ndipo Umboni uwu pamene unafalitsidwa, Unyinji unadza palimodzi, ndipo anadodomsedwa, Chifukwa aliyense anamumva—*iyе* akuyankhula mu Chinenero chake Chomwe.

<sup>34</sup> Tsopano zindikirani! Pamene moto unadza, iwo unali malirime; pamene iwo anali akuyankhula, icho chinali chinenero. Tsopano, pali kusiyana kwakukulu pakati pa malirime ndi zinenero. Kwa ife zonsezo ndi zofanana. Koma, mu Chigriki “lirime” zimatanthauza *ili* [M’bale Branham akufotokozera—Mkonzi.] Khutu ndi *ili*. Mukuona? Ilo silimatanthauza chinenero; ilo limatanthauza gawo la thupi lako ilo ndilo lirime. Ngati inu mungazindikire, izo zinamasuliridwa kuti *malirime a moto* chomwe chikutanthauza “monga malirime,” monga ngati chidutswa cha moto, lawi lalitali la moto. Tsopano, penyani kutsimikizirako tsopano. Ndipo aliwonse a malo amenewo tsopano, musati muiwale izo.

<sup>35</sup> Tsopano, ife tikuti tipereke kasewero kakang’ono usikuuno. Ndipo ine ndikuti ndizisiyire izo kwa inu. Tsopano kumbukirani, ngati chirichonse chiri mosiyana, izo ziri kwa inu. Koma njira yokha yomwe wina aliyense angakhoze kupeza konse chirichonse kuchokera kwa Mulungu ndi mwa chikhulupiriro. Ndipo inu musanati . . .

<sup>36</sup> Ine ndiyenera kuti ndizidziwa chimene ine ndikuchita ine ndisanakhale ndi chikhulupiriro mu zomwe ine ndikuzichita. Nchifukwa chiani inu munamukwatira mkazi wanu? Inu munali ndi chikhulupiriro mwa iye. Inu munamuyesa iye, munamupenya iye, munawona komwe iye ankachokera, yemwe iye anali. Ndi momwe liriri Lemba, kwa Mulungu. Ndi zomwe zimapangitsa masomphenya awa, a—Lawi la Moto ili, zinthu zonse izi, chifukwa Mulungu analonjeza izo. Mulungu ananena chomwecho. Ine ndamuyesapo Iye ndi Mawu Ake ndipo ine ndikudziwa kuti Ichi ndi Choonadi. Ndipo inu muzitsatira Mawu Ake. Ndiye ngati pali kusokonezeka penapake, ndiye pali chinachake cholakwika penapake. Chifukwa Mulungu (mvetserani!)—Mulungu sanachite konse kapena sadzagwira konse ntchito mochoka kwa Iyeyekha—kapena motsutsana ndi malamulo Ake omwe. Dzinja silingabwere mu chilimwe, ndipo chilimwe sichingabwere mu dzinja. Masamba sangakhoze kumagwa mu nthawi ya kuphukira ndi kubwereranso kachiwiri mu kugwa. Inu simungakhoze basi kuzipangitsa izo.

<sup>37</sup> Monga ine ndinanenera usiku wathawu za chitsime cha kasupe, kutsirira mbewu zanu. Kapena ngati inu mutaima pano pakati pa tchire, ndipo imo ndi mwakuda bii, ndipo inu mukanati, “O, magetsi opambana, ine ndikudziwa inu muli mmundamu. Tsopano, ine ndataika, sindikudziwa kumene ine ndikupita. Ndipatse kuwala, kuti ine ndikhoze kumawona momwe ndingayendere! Alipo magetsi okwanira kuti uwalitsire mmundawu.” Izo nzoona. Inde, bwana! Alipo magetsi okwanira mu chipinda chino kuti achiwalitse icho popanda ngakhale nyali izo, popanda izo. Koma inu muyenera kuti muwalamulire iwo. Tsopano, inu mukhoza kufuulira kwa iwo mpaka inu osatha kufuulanso, iwo sangakhoze konse kuwalitsa. Koma ngati inu

mutagwira ntchito molingana ndi malamulo a magetsi, ndiye inu mupeza kuwala.

<sup>38</sup> Chabwino, ndi mofanana momwe ziriri ndi Mulungu. Mulungu ndiye Mlengi wamkulu wa miyamba ndi dziko lapansi, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye akadali Mulungu. Koma Iye amagwira ntchito pamene inu mukutsatira malamulo Ake ndi malangizo basi. Abwenzi, ine ndikunena izi: Ine sindinayambe ndaziwonapo izo zitalephera, ndipo sizingatero.

<sup>39</sup> Tsopano, tiyeni tizindikire. Yesu mu Luka 24:49 anali atawatuma atumwi iwo atapulumsidwa kale ndi kuyetsedwa malingana ndi Mawu; kulungamitsidwa pa kukhulupirira pa Ambuye Yesu; kuyetsedwa pa Yohane 17:17 pamene Yesu anati, “Ayeretseni iwo, Atate, kupyolera mu Choonadi. Mawu Anu ndiwo Choonadi.” Ndipo Iye anali Mawu.

<sup>40</sup> Tsopano, anawapatsa iwo mphamvu kuti azichiza odwala, kutulutsa ziwanda, kuukitsa akufa; ndipo iwo anabwerera akusangalala. Ndipo maina awo anali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Inu mukukumbukira momwe ife takhala tikudutsira mu izo tsopano. Koma iwo anali asanatembenuke apabe. Yesu anamuza Petro usiku wa kupachikidwa Kwake uja; Iye anati, “Iwe ukadzakhala utatembenuka, ndiye udzawalimbikitse abale ako.”

<sup>41</sup> Mzimu Woyera ndi womwe... Inu mukukhulupirira kuloza ku Moyo Wamuyaya, koma pamene Mzimu Woyera ubwera Iwo ndiwo Moyo Wamuyaya. Inu mukukhulupirira kuloza ku... Ndinu obalidwa ndi Mzimu pa kuyetsedwa, koma simunabadwe konse ndi Mzimu mpaka Mzimu Woyera utabwera umo. Ndiko kukhoza. Mwana amakhala ndi moyo mu chiberekero cha amake, akatumba aang’ono amadziwongola; ndi moyo. Koma ndi moyo wosiyana pamene iko kapumila mpweya wa moyo mu mphuno zake. Ndi zosiyana. Nchomwe icho chiri, ndi... .

<sup>42</sup> M’bale wanga wokondedwa wa Methodisti, ndi Pilgrim Holiness, ndi Nazarene, ubatizo wa Mzimu Woyera ndi wosiyana ndi kuyetsedwa. Kuyetsedwa ndi kutsuka, komwe kuli kukonzekera kwa Moyo. Koma pamene Mzimu Woyera ubwera, Iwo ndiwo Moyo. Kukonzekera ndi kutsuka chidacho; Mzimu Woyera ndi kuchidzazitsa chidacho. *Kuyetsedwa* kumatanthauza “kutsukidwa ndi kuikidwira pambali kwa utumiki.” Mzimu Woyera ndi kuchiyika icho mu kutumikira. Ndinu chida chimene Mulungu wachitsuka.

<sup>43</sup> Ndipo ife tikupeza kuti Mzimu Woyera ndi Mulungu Mwiniwake mwa inu, Mulungu anali pamwamba pa inu mu Lawi la Moto ndi Mose. Mulungu anali ndi inu mwa Yesu Khristu. Tsopano Mulungu ali mwa inu mwa Mzimu Woyera. Osati amulungu atatu, Mulungu mmodzi akugwira ntchito mu mauidindo atatu.

44 Mulungu kudzichepetsa, kubwera pansi kuchokera pamwamba pa munthu. Iye sankakhoza kumukhudza Iye, chifukwa iye anali atachimwa mmunda wa Edeni ndipo anadzilekanitsa yekha ku chiyanjano Chake. Ndiye nchiani chinachitika? Iye ankachita kumakhala pamwamba pa iye. Magazi a ng'ombe zamphongo ndi mbuzi sakanakhoza kumulola Iye kuti akhale ndi chiyanjano ndi munthu kachiwiri; koma kupyolera mmalamulo ndi malangizo, kuwonetseratu nthawi ino ikudza, pa kupereka nsembe ng'ombe, ndi zina zotero, ndi nkhosa. . . Ndiye pamene Mulungu anabwera pansi nadzakhala mu thupi loyeretsedwa, lobadwa mwa namwali kwa mkazi, kuti Mulungu Mwiniwake. . . Inu mukudziwa zomwe Mulungu anachita? Iye—Iye sankachita kanthu koma basi. . . Iye anazika Hema Wake pakati pa athu. Mulungu ankakhala mu Hema wotchedwa Yesu Khristu. Iye anadzangomanga Hema Wake limodzi nafe, anadzakhala. . . (Ine—ndidzalalikira pa izo mmawa, kotero ndibwino kuti ine ndizisiye izo zokha.) Tsopano, kuti—momwe hema wa Mulungu—kapena anadzakhala ndi ife. . .

45 Ndipo tsopano Mulungu ali mwa ife. Yesu ananena mu Yohane 14, “Mu tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti ine ndiri mwa Atate, Atate ali mwa Ine, ndi Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.” Mulungu mwa ife. Cholinga chake chinali chiani? Kuti adzachite dongosolo Lake.

46 Mulungu anali ndi dongosolo. Iye ankafuna kuti azidzagwira ntchito pakati pa anthu, ndipo Iye anazibweretsa izo mu Lawi la Moto, umene unali Moto wachinsinsi umene unkapachikika pamwamba pa ana a Israeli. Ndiye Moto womwewo unadzawonetseredwa mu thupi la Yesu. Ndipo Iye anati Iye anali Moto umenewo, “Asanakhalepo Abrahamu, INE NDINE.” Iye anali Moto umenewo. Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu, ndipo ine ndikubwerera kwa Mulungu.” Ndipo itachitika imfa Yake, kuikidwa, ndi chiukitsiro, Paulo Woyera anakomana naye Iye pa njira—pamene dzina lake linali likadali Sauli—pa njira yaku Damasiko, ndipo Iye anali apono atabwereranso ku Lawi la Moto ilo. Kuwala kunathimitsa maso ake. Ndiko kulondola.

47 Ndipo pano Iye ali lero, Lawi la Moto lomwelo, Mulungu yemweyo akuchita zizindikiro zomwezo, ntchito zomwezo. Bwanji? Iye akugwira ntchito pakati pa anthu Ake. Iye ali mwa ife. Ine. . . Iye ali ndi inu tsopano, “koma ine ndidzakhala mkati mwanu. Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka ku mapeto a chimaliziro,” mapeto a dziko. Iye adzakhala ali nafe.

48 Tsopano, zindikirani. Yesu anali atawatuma iwo kuti apite uko ku Yerusalemu ndi kukadikira. Mawu oti *tarry* amatanthauza “kudikirira,” samatanthauza kupemphera, amatanthauza “kudikirira.” Iwo sanali otsatira oyenera apabe

kuti azilalikira, chifukwa iwo ankangodziwa chiukitsiro Chake mwa Umunthu Wake, pa kumuwona Iye kunja. Iye—Iye anawalamulira iwo kuti asati azikalalikiranso, kuti asamachite kalikonse mpaka poyamba iwo atadzazidwa ndi Mphamvu yochokera kumwamba.

Ine sindikukhulupirira kuti mlaliki aliyense ali wotumidwa ndi Mulungu kapena kuti akhoza kukhala wodzozedwa molondola... Chifukwa Mulungu ndi wopandamalire. Ndipo chimene Mulungu amachita kamodzi, Iye amachichita nthawizonse. Tsopano, ngati Mulungu sakanati awalole iwo kuti azilalikira mpaka iwo atapita ku Pentekoste ndipo atalandira chowachitikira cha Chipentekoste, palibe munthu, kupatula chikhumbo china chakuya chakechake kapena bungwe lina litamutuma iye, ali ndi ufulu wolowa mu guwa mpaka iye atadzazidwa kaye ndi Mzimu Woyera. Ndizo ndendende kulondola. Chifukwa iye akuwatsogolera iwo mwa lingaliro laluntha la bungwe lina mpaka iye atadzazidwa ndi Mzimu Woyera; ndiyeno, iye akuwapatsa iwo chakudya cha nkhunda; *Mwanawankhosa ndi Nkhunda*, monga ife tinaziyankhula usiku watha.

<sup>49</sup> Tsopano zindikirani. Iye anati, “Pitani uko ku Yerusalemu ndipo mukakhale komweko; muzikangodikirira kumeneko mpaka ine nditatumiza lonjezo la Atate.” Ndiyeno, kodi iwo anachita chiani? Iwo analipo wani handiredi ndi twente a iwo, amuna ndi akazi. Iwo anapita mu chipinda chapamwamba ku kachisi.

Tsopano, linali kuyandikira tsiku la Phwando la Pentekoste, kuchokera ku kuyeretsa kwa malo opatulika, kupha kwa mwanawankhosa wa paskha mpaka—kudza kwa Pentekoste, zomwe zinali zipatso zoyamba za zokolola, chisangalalo, chisangalalo cha Pentekoste. Ndi pa manyumba...

<sup>50</sup> Tsopano, ine ndakhala ndiri mmaiko. Maiko akummawa si kawirikawiri kuti amakhala ndi makwerero opita mmwamba mkati. Makwererowo anali kunja. Kunja kwa kachisi, ife timauzidwa, uko kunali makwerero ankalondolera mpaka mmwamba ku kachipinda kakang’ono patali pomwe, opita mmwamba, ndi mmwamba, ndi mmwamba, mpaka iwe umafika ku kachipinda kakang’ono mmwamba umo, monga chipinda chosungira zinthu pamwamba pa kachisi, mtundu wina wa chipinda chaching’ono, chipinda chapamwamba. Ndipo Baibulo linati iwo anali mkati mmenemo ndipo zitseko zinali zitatsekedwa, chifukwa iwo ankachita mantha ndi Ayuda, chifukwa iwo akanawakhadzula iwo chifukwa chomupembedza Ambuye Yesu, Kayafa wansembe wamkulu, ndi Pontiasi Pilato, ndi iwo atamuika kale Iye ku imfa. Chotero iwo ankati athane nawo onse otchedwa Akhristu. Ndipo zitseko zinali zitatsekedwa, ndipo iwo anali akudikirira.

<sup>51</sup> Tsopano, mu zipinda izo monga icho, munali mopanda mazenera. Mazenera anali zinthu zazing'ono zotchingidwa zokhala ndi zonga zitseko, iwe unkazikoka kuti utsegule. Mu zipinda zimenezo munkakhala nyali zazing'ono za chikoloboi zomwe zinkapachikidwa chozondotsa ndi kumayaka... Ngati inu mungadzafike konse mu California ku Cafeteria ya Clifton, mudzapite ku chipinda cha pansi, ndipo inu mudzakapeza china cha mtundu wofanana, ndi chipinda chapamwambacho. Kodi inu munayamba mwapitamo uko? Ndi angati muno anayamba apitamo uko? Ine ndikuwawona anthu mukugwedeza mitu yanu. Chabwino, inu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba. Chabwino. Mudzapite pansi pamene, ndipo inu mudzakawuona Munda wa Getsemane; inu musanatero, inu mudzakalowe mu zipinda zina zachikale izo. Izo ziri ndendende moona. Uko inu mukapeza nyali yaing'ono ya mafuta a azitona ili ndi chingwe chaching'ono cha ubweya mkati mwake, chikuyaka.

<sup>52</sup> Tsopano, tiyeni tinene kuti iwo anali mmwamba umo, atakwera chozungulira kunja uku. Iwo anakwera umo ndipo anakadzibisa okha, chifukwa iwo ankachita mantha ndi Ayuda. Yesu sanawauze iwo kuti adzapite mu chipinda chapamwamba. Iye anangoti, “Mukadikirire ku Yerusalemu.” Iwo akanakhala pansi apa mu nyumba, nzovuta kuti udziwe zomwe zikanati zichitike. Iwo akanabwera ndi kudzawatenga iwo. Chotero iwo anapita ku kanyumba kachikale mu chipinda cha mmwamba, mmwamba momwe umo mu chipinda cha mdenga, ndipo mmenemo, iwo anatseka chipindacho kuti Ayuda sakanakhoza kufika kwa iwo. Ndipo iwo anakhala mmenemo akudikira kwa masiku khumi.

<sup>53</sup> Tsopano, tsopano, ife tiri mu Machitidwe 1. Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano. Inu mwachigwira chithunzicho? Kunja kwa nyumba makwerero aang'ono anapita mmwamba, ndipo iwo anakalowa mu chipinda chaching'ono ichi. Pansi mu kachisi mkati iwo ali ndi Phwando la Pentekoste. O, uko kunali kukuchitika nthawi yaikulu. Tsopano, pamene tsiku la Pentekoste linadza kwathunthu, iwo anali onse ndi lingaliro limodzi, lingaliro limodzi, akukhulupirira kuti Mulungu anali woti atumiza lonjezo limenelo. Ndipo mulole munthu aliyense muno alowe mu lingaliro lomwelo usikuuno ndipo awone zomwe ziti zichitike. Izo ziyenera kubwereza. Ilo ndi lonjezo chimodzimodzi basi monga iwo anali nalo. Mukuona?

<sup>54</sup> Kodi iwo anali kuchita chiani? Ankatsatira malangizo, ankatsatira m—m—malamulo a Mulungu: “Dikirani mpakana...”

<sup>55</sup> Tsopano, iwo ankachita mantha ndi Ayuda. Tsopano, zikumbukirani izo. Iwo anali kuwaopa Ayuda. Tsopano, zonse mwadzidzidzi uko kunadza phokoso longa mphepo ya nkokomo. Iyo siinali mphepo yankokomo; iyo inali ngati mphepo

yankokomo. Ine ndiwerenga ndemanga mu maminiti pang'ono okha ya womasulira. Ilo linali longa mphepo yankokomo. Mwa kuyankhula kwina, iyo inali mphepo yauzimu (o!), chinachake chimene iwo amakhoza kuchimverera. Mphepoyo inali mkati mwa iwo. Pamenepo panadza—mphepo yankokomo, yonga mphepo yankokomo. Mphepoyo siinali kukukuma, koma inkangomveka monga mphepo ya nkokomo, yonga chinachake chikuti [M'bale Branham akupanga phokoso la mphepo—Mkonzi.] Kodi inu munayamba mwaimverera iyo? O, mai! Yonga nkokomo wa mphepo. Tsopano penyani. Ndipo iyo inadzaza . . . Tsopano, umu anati “onse,” koma mu Chigriki anati “Yonse (wankulu Y-o-n-s-e), Nyumba Yonse,” paliponse mkati umo. Mng'alu uliwonse, ngodya, ndi pamphanga pankanga kuti panali podzaza nayo. Osati kuti, “Nkuti, Abale, kodi inu mukumverera zomwe ine ndikumverera?” Ayi! Iyo inali paliponse, monga mphepo yankokomo. Tsopano penyani. “Apo panadza phokoso longa nkokomo wa mphepo yamphamvu ndipo (cholumikizira. Tsopano muziwapenya “ma ndipo” amenewo. Ngati inu simutero, inu muwapangitsa Iwo kunena china chimene Iwo ali kunena. Mwaona?)—ndipo monga (ndicho chimene chinachitika choyamba chinali phokoso, chinachake chonga n—nkokomo wa mphepo unadza pa iwo)—ndipo (inu mukukumbukira, usiku watha ine ndinapita ku gulosale ndipo ndinakagula mtanda wa mkate ndi nyama ina. Ndi chinachake chomwe chinapita limodzi nacho. Mkate ndi chinthu chimodzi, nyama ndi chinanso. Ndipo nkokomo unali chinthu china chimene chinawakhudza iwo)—ndipo pamenepo panawonekera kwa iwo, (pamaso pawo) malirime—malirime ogawanika.”

<sup>56</sup> Kodi aliyense muno anayamba waonapo *Malamulo Khumi* a Cecil DeMille? Kodi inu munazindikira pamene Malamulowo anali kulembedwa? Momwe iye anazigwirira izo, ine sindimadziwa. Zinalipo zinthu ziwiri kapena zitatu zomwe ine ndinaziwona umo zomwe ine ndinazikonda kwenikweni. Chinthu choyamba ndi kuwala kwa ambara kuja, umo ndi ndendende momwe Iko kumawonekera. Mukuona? Chinthu china chinali pamene Malamulo anali atalembedwa, ndipo izo zitatha, kodi inu munazindikira kuulukira kwina kwa Lawi la Moto lalikulu lija, apo panali malawi aang'ono a moto akuwulukira kwina? Kodi inu munazindikira izo? Tsopano, ndicho chimene ine ndikuganiza kuti ichi chinali pa Pentekoste. Apo panawonekera kwa iwo . . . Koteri iwo anakhoza kukuwona Iko. Iwo sanati, “Apo anagwera mkati mwao.” Koma pamenepo panawonekera kwa iwo malawi (ife tizitcha izo), malirime, ngati lirime monga lirime ili apa, [M'bale Branham akuwonetsera—Mkonzi.], mawonekedwe a lirime, lawi la moto. Tsopano, khutu—monga ine ndinati, khutu ndi khutu; chala ndi chala. Chala sizikutanthauza kuti iwe unazimverera izo; izo zikutanthauza kuti icho chinkawoneka monga chala. Ndipo ngati ilo likanakhala liri khutu, izo sizikanatanthauza

kuti iwo analimva ilo; izo zinkawoneka monga khutu. Uwu unali moto umene unkawoneka monga lirime, osati winawake akuyankhula, moto umene unkawoneka monga lirime.

<sup>57</sup> Tsopano mvetserani. Penyani momwe Chigriki chikuwerengekera pa izo apa:

Ndipo mwadzidzidzi apo panadza Phokoso...longa *Mphepo ya nkokomo wamphamvu...* (Ya 3—ndime ya 3.)

Ndipo Malirime Ogawanika anawonekera kwa iwo,... (*Osati malirime ogawanika anali mkati mwawo, kapena iwo anali kuyankhula ndi lirime logawanika, awo anali malirime ogawanika omwe anawonekera kwa iwo. Tsopano penyani. Iwo sali pa iwo apabe. Ali mu chipinda mmenemo, kuzungulira zungulira umo monga mu mphepo iyi.*)...kwa iwo, monga Moto—Malirime Ogawanika anawonekera kwa iwo,... (Ndizo patsogolo pawo)...onga Moto,... (*Malirime onga moto.*)... ndipo limodzi... (*Lalokha.*)...linadzatera pa wina aliyense wa iwo. (*Osati anapita mkati mwawo; koma anadzatera pa iwo.*)

<sup>58</sup> Tsopano, mukuona momwe King James akanati aziponyere izo kumbali: “Ndipo malirime ogawanika anabwera pa iwo, kapena anadzakhala (kodi zikuwerengeka motani mu King James umo?)—anadzakhala pa iwo.” Mukuona? Tsopano, iwo sakanakhoza kupita mmwamba umo ndi kukakhala pansi. Ife tikudziwa izo. Koma mwapachiyambi anati, “Iwo anadzatera pa iwo,” ine ndikukhulupirira; si choncho izo? Mundirole ine ndizipeze izo ndendende moona. Eya! “...anadzatera pa aliyense wa iwo.” Lirime limodzi la moto linadzatera pa aliyense wa iwo. Mukuona apo? Kodi inu mukuzimvetsa izo? Ndicho chinthu chachiwiri chimene chinachitika. Choyamba chinali mphepo, kenako kuwonekera kwa malirime a moto.

<sup>59</sup> Munali mchipinda chaching’ono ichi umu muli nyali zazing’ono za mafuta zikuyaka. Taganizani za iwo atakhala mmwamba umo. Ndipo wina nati, “O!” Iye anayang’ana ponseponse mnyumbayo; iwo anali ponseponse mnyumbayo. Ndiye iwo anati, “Taonani!” Malirime a moto anayamba ku—kubwera kuzungulira mchipindamo. Tsopano penyani. Ndipo pamenepo anawonekera malirime a moto awa.

Tsopano penyani chotsatira:

Ndipo...(*Cholumikizira china; chinachakenso chinachitika.*)...iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera,...(*Chinthu chachiwiri chimene chinachitika.*)

<sup>60</sup> Tsopano taonani, ife tikufuna kuti tizisinthe izo mozungulira nkuti, “Iwo anali ndi malirime a moto, ndipo apa akubwebweta pamenepo; ndiyeno anatuluka panja ndipo anayamba kuyankhula mu lirime losadziwika.” Mulibe chinthu



chotero monga icho mu Malemba, mzanga. Aliyense yemwe amayankhula ndi lirime losadziwika pa kulandira Mzimu Woyera amachita izo mosiyana ndi Baibulo. Ndipo ine ndisonyeza kwa inu mu maminiti pang'ono ndi kutsimikizira kwa inu kuti ine ndimakhulupirira kuyankhula mu malirime osadziwika, koma osati pakulandira Mzimu Woyera. Iyo ndi mphatso ya Mzimu Woyera. Mzimu Woyera ndi Mzimu.

<sup>61</sup> Tsopano penyani. Malirime awa anali mu chipinda monga moto, ndipo iwo anaikidwa pa aliyense. Ndiye iwo anadzazidwa ndi Mzimu Woyera (chinthu chachiwiri), ndipo kenako, iwo atadzazidwa kale ndi Mzimu Woyera, atayankhula ndi malirime, osati ndi malirime, ndi zinenero. Kodi inu mwazindikira izo? Iwo anayamba kuyankhula ndi zinenero zina momwe Mzimu unkawapatsira iwo kuti ayankhule. Tsopano, izi zinamveka konsekonse.

<sup>62</sup> Tsopano penyani. Tsopano, tiyeni titenge kalongosoledwe kachiwiri kuti inu musati muziiwale izi tsopano. Malingana ndi Lemba, mu chipinda chapamwamba akuyembekezera, mwadzidzidzi phokoso longa mphepo yankokomo, yomwe inali pa iwo; umenewo unali Mzimu Woyera. Ndi angati akukhulupirira kuti kumeneko kunali kuwonekerapo kwa Mzimu Woyera? Monga mphepo, mphepo yauzimu. Ndiye iwo anazindikira. Ndipo kuchokera mmenemo munali malirime aang'ono a moto, handiredi ndi twente a iwo, ndipo anayamba kudzakhazikika pansu ndipo anadzakhala pa wina aliyense wa iwo. Chinali chiani icho? Chinali chiani? Lawi la Moto, amene anali Mulungu Mwiniwake akudzigawaniza Iyeyekha pakati pa anthu Ake, kubwera mkati mwa anthu. Yesu anali nacho chinthu chonsecho; Iye anali nao Mzimu Woyera wopanda muyezo; ife timaulandira Iwo mwa muyezo (Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?) chifukwa ndife ana okhazikitsidwa. Moyo Wake—Moyo Wake Wamuyaya unali kubwera mkati. Tsopano, ndi chiani chinachitika? Ndiye iwo onse anadzazidwa ndi Mzimu Woyera.

<sup>63</sup> Tsopano, ine ndikufuna kuti ndikufunsi inu chinachake. Ndi liti pamene mphekeserayo inayamba? Ngati iwo akanati achite kubwera kuchokera mchipinda chapamwamba icho kuti atsike pansu ndi masitepe amenewo ndi kukafika mu mabwalo a nyumba yachifumu—kapena uko mu—ku mabwalo a kachisi, kumene kunali mwinamwake mdadada wa mu mzinda kuchokera, kumene iwo anali, chipinda chammwamba ndi kutsika, mu mabwalo kumene anthu onse anasonkhana palimodzi...Ndipo iwo anabwera kuchokera umo okhala ngati aledzera ndi Mzimu. Pakuti anthu anati, “Amuna awa aledzera vinyo watsopano.” Iwo anali asanawonepo chirichonse chonga izo.

<sup>64</sup> Ndipo aliyense ankayesera kunena kuti, “Mzimu Woyera wabwera. Lonjezo la Mulungu liri pa ine. Ine—ine ndadzazidwa

ndi Mzimu.” Ndipo iye pokhala Mgalilea, mwamuna yemwe iye anali kuyankhula naye, Mluya kapena Mperisi, ankamumva iye mu chinenero chake chomwe.

<sup>65</sup> “Ife tikuwamva bwanji (osati mu lirime losadziwika)—ife tikuwamva bwanji munthu aliyense mu lirime lomwe ife tinabadwira. Ndipo kodi onse awa omwe akuyankhulawa si Agalilea?” Ndipo anali mwina wake akuyankhula Chigalilea...Koma pamene iwo ankawamva iwo, izo zinali mu chinenero chomwe iwo anabadwiramo. Ngati si choncho, ine ndikufuna kuti inu mundifunse ine—mundiyankhe ine funso ili: Zinali motani kuti Petro anaimirira pamene ndipo ankayankhula mu Chigalilea, ndipo gulu lonselo linkamva chimene iye ankanena? Miyoyo zikwi zitanu inadza kwa Khristu apo pomwe ndipotu Petro akuyankhula mu chinenero chimodzi. Zedi! Uyo anali Mulungu akuchita chozizwitsa. Petro, kwa omvetsera omwewo omwe anapangidwa ndi a ku Mesopotamia, ndi alendo, ndi otembenuzidwa, ndi chirichonse ochokera ku dziko lonse lapansi anali ataima pamene...Ndipo Petro anaima ndi kumalalikirira mu chinenero chimodzi, ndipo munthu aliyense ankamumva iye, pakuti zikwi zitanu analapa ndipo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu apo pomwe. Zinali motani zimenezo?

<sup>66</sup> Taonani, abwenzi, ine sindingakhoze kuyembekeza m'bale wanga wa chipembedzo, wa Chipentekoste kuti angazivomereze izo pakali pano. Koma inu muzitsatire izo kudutsa mu Baibulo ndipo mundiuze ine nthawi iliyonse yomwe iwo analandirapo konse Mzimu Woyera nayankhula mu malirime omwe iwo sanali kudziwa chimene iwo anali kuchiyankhula. Ndipo ngati njira yake ili imeneyo yomwe anaulandirira Iwo uko, Mulungu wochita mwayekha...Izo ziyenera kumachitika nthawi iliyonse mwanjira yomweyo.

<sup>67</sup> Tsopano, ine sindingakhoze...Tsopano, kunyumba ya Korne...Ife tikukumbukira, pamene ife tinapita ku Samaria kuja, usiku watha, ife tinakapeza kuti uko kunalibe chinthu chimodzi chinanenedwa chokhudza iwo kumva mu lirime lina lililonse, panalibe zinanenedwa zokhudza izo. Koma pamene iwo anapita ku nyumba ya Kornelio, kumene kunali mafuko atatu osiyana a anthu, iwo anayankhula mu malirime. Ndipo pamene iwo anatero, ngati iwo anatero, iwo anaulandira Iwo, Petro anati, mwanjira yomweyo imene anaulandirira Iwo pachiyambi. Ndipo iwo anadziwa kuti Amitundu anali atalandira chisomo kuchokera kwa Mulungu, chifukwa iwo anali atalandira Mzimu Woyera chimodzimidzi monga iwo anachitira pachiyambi. Ine ndiri nalo funso pano, chinachake pa izo mu maminiti pang'ono. Ine ndikufuna kuti ndiyike maziko, chotero inu mukhoze kuwona zomwe izo ziri.

<sup>68</sup> Tsopano, ine sindingakhoze kuyembekezera anthu omwe aphunzitsidwa mosiyana...Ndipo mveterani kwa

ine, abale anga okonedwa, ofunika, Achipentekoste. Ine sindingakaphunzitse izi kunja. Izi ndi... Ine sindikanachita kanthu koti kayambitse kutsutsana. Koma ngati ife sititenga Choonadi, ndi liti pamene titi tidzayambe? Ife tiyenera kuti tikhale nacho chinachake choti chichitike pano choti chitiwongole ife. Ife tiyenera kuti tipeze chisomo chokwatulitsa pano tsopano. Choonadi chiyenera kutulukirapo.

<sup>69</sup> Akanachita chiani munthu ngati iye akanakhala wogontha, ndi wosayankhula, ndipo akanakhala wosayankhula nkomwe? Kodi iye akanakhoza kulandira Mzimu Woyera? Bwanji ngati iye akanakhala wopanda lirime pa kuyamba pomwe, ndipo munthu wosaukayo akufuna kuti apulumutsidwe? Mukuona? Ndi Mzimu Woyera, ndiwo ubatizo. Ndiyeno, mphatso zonse izi monga kuyankhula mu malirime, kutanthauzira kwa malirime, ziri pambuyo iwe utabwera mu Thupilo mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Pakuti mphatso zimenezo ziri mu Thupi la Khristu.

<sup>70</sup> Tsopano, chifukwa chimene ine ndikuti. . . Tsopano, penyani kuno. Kodi inu mukanyembekeza mpingo wa Katolika, umene unali mpingo woyamba kupanga bungwe mu dziko pambuyo pa atumwi. . . Ndiye mpingo wa Katolika anapanga bungwe, o, zaka mazana angapo pambuyo pa imfa ya mtumwi wotsiriza, mwina sikisi handiredi ndi—zaka pambuyo pa atumwi, pambuyo pa Nicene Council pomwe, pamene makolo a Nicene anabwera palimodzi ndipo anapanga bungwe; ndiye iwo anawuyika mpingo wa konsekonse, umene unali mpingo wa Katolika. Mmenemo iwo anapanga mpingo wa kwa dziko. Ndipo mawu oti *katolika* amatanthauza “konsekonse”; ndiko kulikonse. Iwo. . . Roma—Roma wachikunja anatembenezidwa kukhala Roma waupapa. Ndipo iwo anaikapo papa kuti akhale mutu kuti atenge malo a Petro, chimene iwo ankaganiza ndipo ankanena kuti Yesu anamupatsa mafungulo aku Ufumu. Ndi kuti Papa anali wosalephera, ndipo alipo panobe kwa mpingo wa Katolika. Kut. . . Mawu Ake ali lamulo ndi langizo. Iye ndi papa wosalephera. Izo zinapitirira.

<sup>71</sup> Ndiyeno, chifukwa kuti iwo sanali kugwirizana ndi chiphunzitsa cha Chikatolika ichi, iwo anali kuikidwa ku imfa, kuwotchedwa pa nkhu, ndi china chirichonse. Ife tonse tikuzidziwa izo kupyolera mu zolemba zopatulika za Josephus, ndi *Bukhu la Fox la Ofera*, ndi ochuluka ena opatulika. . . *Two Babylons* la Hislop, ndi—mbirizakale zazikulu. Ndiye, izo—zitatha zaka fifitini handiredi, momwe ife tikudziwira, za Mibadwo ya Mdima, Baibulo linachotsedwa kwa anthu. Ndipo Ilo linali—Ilo linabisidwa ndi ansembe aang’ono, ndi ena otero, ife timamva.

<sup>72</sup> Ndiye zitachitika izo panadza kukonzanso koyamba kumene kunali Marteni Lutera. Ndipo iye anabwera poyera nanena kuti mgonero umene Katolika umautchi thupi—thupi lenileni la Khristu, iwo unali kungoimira thupi la Khristu. Ndipo

iyе anaponyera mgonero pa chotchingira ku guwa, kapena pa masitepe, ndipo anakana kuti aziwutcha iwo thupi lenileni la Khristu, ndipo analalikira, “Olungama azikhala moyo mwa chikhulupiriro.” Tsopano, inu simungakhoze kuyembekeza mpingo wa Katolika kuti uvomerezane ndi iye, ndithudi ayi, pamene mtsogoleri wawo wosalephera atawauza iwo kuti ayi. Chabwino.

<sup>73</sup> Ndiye Marteni Lutera atatha, kulalikira Kulungamitsidwa, Joni Wesile anabwera motsatira akulalikira Kuyetsedwa. Ndipo iye ankalalikira kuti munthu, akatha kulungamitsidwa (zonsezo ndi zabwino)—koma iwe umayenera kuti uyeretsedwe, kutsukidwa, muzu wa zoipa uchotsedwe mwa iwe ndi Magazi a Yesu. Tsopano, inu simungakhoze kuwayembekeza Achilutera kuti azilalikira Kuyetsedwa, chifukwa iwo sati azichita izo.

<sup>74</sup> Wesile atatha kulalikira Kuyetsedwa, ndi ena ochuluka atachoka kwa iwo, chimene chinadzakhala Methodisti ya chi Wesile, ndi Nazerini, ndi ena otero, omwe ankasunga moto chiyakire kupyola mu m’badwo wawo, ndiye potsatira kunadza Pentekoste ndipo anati, “Pakuti, Mzimu Woyera ndiwo ubatizo, ndipo ife timayankhula ndi malirime pamene timaulandira Iwo.” Zedi. Ndiye pamene izo zinabwera apo, inu simukanakhoza kuwayembekeza a Nazareni, ndi Amethodisti Achiwesile, ndi ena otero kuti azikhulupirire izo. Iwo sakanati achite izo. Iwo anazitcha izo mdierekezi. Chabwino. Chinachitika ndi chiani? Iwo anayamba kugwa; Pentekoste inayamba kuwuka. Tsopano iyo yawuka mpaka pa malo pomwe Pentekoste yalandira kugwedzedwa kwake. Iyo yapanga bungwe ndipo yatuluka, sali kulandera china chirichonse. Iwo ali nawo malamulo awo awo ndi malangizo, ndipo izo zikukhazikitsa icho.

<sup>75</sup> Tsopano, pamene Mzimu Woyera ukubwera umo ndi kudzaulula Choonadi cha chirichonse ndi kuzitsimikizira izo ndi Kukhalapo Kwake komwe ndi mwa Mawu Ake, inu simungakhoze kuwayembekeza anthu Achipentekoste kuti aziti, “Ine ndivomerezana nazo izo.” Iwe ukuyenera kuti uziyima wekha monga Lutera anachitira, monga Wesile anachitira, ndi monga ena onse a iwo ankachitira. Iwe uyenera kumaima pa izo chifukwa oralo liri pano. Ndipo ndi chimene chikundipanga ine kukhala bakha wonyansa. Ndi chimene chikundipanga ine kukhala wosiyana.

<sup>76</sup> Ndipo ine sindingakhoze kuyamba monga M’bale wanga wofunika Oral Roberts, ndi Tommy Osborne, Tommy Hicks, ndi iwo, chifukwa mipingo siingagwirizane ndi ine. Iwo amati, “Iye amakhulupirira mu chitetezero chamuyaya. Iye ndi wa Baptisti. Iye samakhulupirira mu kuyankhula mmalirime ngati umboni woyamba wa Mzimu Woyera. Pitani kutali ndi munthu ameneyo!” Mukuona?

<sup>77</sup> Koma bwerani maso ndi maso ndi izo. Yang'anizanani nazo izo. Iwo akhoza kuyang'anizana ndi Achilutera, a—Amethodisti akhoza. Apentekoste akhoza kuyang'anizana ndi Amethodisti. Ine ndikhoza kuyang'anizana ndi Apentekoste nazo. Ndiko kulondola ndendende. Ndi zoon. Nchifukwa chiani ziri choncho? Ife tikuyenda mu Kuwala pamene Iye ali mu Kuwala. Mukuona? Ife tikuyenda chokwera mu Msewuwawukulu wa Mfumu, ndipo zikamafika patali, chisomo chochuluka chikumaperekedwa, mphamvu yochuluka ikumaperekedwa, chazimu chochuluka chikumaperekedwa. Ndipo ndife apo. Ili ndi ora lomwe Mzimu Woyera wabwera pansu mu mawonekedwe a Kuwala monga Iye analiri pachiyambi, Lawi la Moto, ndipo wadziwonetsera Yekha, akuchita zinthu zomwe zomwezo zimene Iye ankazichita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Ndipo Yesu anati, “Inu mumawadziwa bwanji ngati iwo akulondola kapena ayi? Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo. Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndichita nayenso azidzazichita. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.”

<sup>78</sup> Tsopano, abale anga Achipentekoste. Ine ndiri ndi inu. Ndine mmodzi wa inu. Ine ndiri nawo Mzimu Woyera. Ine ndayankhulapo mu malirime, koma ine sindinawalandire iwo pa kulandira Mzimu Woyera. Ine ndiri ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Ine ndinayankhula mu malirime, ndanenera, ndili nazo mphatso za chidziwitso, nzeru, kutanthauzira, ndi chirichonse chikuchitika. Koma ndine womvera ku chirichonse cha zinthu zimenezo, chifukwa tsopano ndine mwana wa Mulungu. Mphamvu, Moto wa Mulungu uli mu moyo wanga; lirime la moto lija limene linadzakhalapo—linabwera mkati mwa ine ndi kuwotchamo chirichonse chimene chinali chosiyana ndi Mulungu, ndipo tsopano ine ndikutsogozedwa ndi Mzimu Wake. Iye angati, “Pita *uko*,” ndipo ine ndimapita. “Pita *uku*”; ine ndimapita. “Yankhula *pano*”; ine ndimayankhula. “Ndipo chita *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*.” Ndi inu apo, monga choncho. . . Iwe ukutsogozedwa ndi Mzimu. Ameneyo ndi Mulungu mwa iwe, akuchita chifuniro Chake. Ziribe kanthu chimene icho chiri, Iye akuchita chifuniro Chake.

<sup>79</sup> Tsopano, mverani. Mundilole ine ndiwone—ndiwerenge pano ife tisanayambe mafunso pa lexicon pano. Tsopano, kuchokera ku Kumasulira kwa ku Vatican, Volume 7, 190—1205:

“Ndi kovuta kuti udziwe ngati linali liwu la *anthu* awo omwe ankayankhula mu *chinenero chachirendo*; kapena zonedwa kapena mphekesera ya kuchitika kwa *mphepo* yauzimu yankokomo *yomwe inalisangalatsa gulu*.”

Iwo sankakhoza kuzimvetsa izo. Tsopano penyani. Kaya apo anali anthu. . .

<sup>80</sup> Ine ndingolongosola. Pano pali gulu la osauka, Agalilea olimba. Ndipo apa iwo ali uko mu msewu. Iwo anali asanawonepo chirichonse chonga izo: manja awo ali mu mlengalenga, akuchokera ku chipinda chapamwamba icho, akutsika makwerero awo, kutuluka kumka uko, atangodzazidwa; iwo anali asanayankhule apobe. Mukuona? Apa iwo anabwera akutsika kudutsa apo. Ndipo tsopano, tiyeni titi, iwo anali kunja uko akuzandima akuzungulira mwa izi. Ndipo anthu anati... Mgriki anathamangira kwa ine nati, Ine ndikuyankhula mu Chigalilea.

Iwe ukuthamangira kwa iye nkuti, “Ndipo chavuta nchiani ndi iwe, Mnyamata?”

<sup>81</sup> “Ine ndadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Mphamvu ya Mulungu inagwera uko mu chipinda icho. Chinachake chinachitika kwa ine. O, Ulemerero kwa Mulungu!”

Ndipo mmodzi wina chakuno, iye anali kuyankhula kwa Mluya, ndipo iye pokhala Mgalilea akunena Chiluya—chinenero cha Chiluya.

<sup>82</sup> Tsopano, iwo sangakhoze kunena, kodi inali mphepo ya nkokomo yomwe inawakokera anthuwo palimodzi pamene unyinjini unabwera palimodzi, kapena kodi kunali kuyankhula mu chinenero chachirendo chimene iwo anali kuyankhula? Tsopano, Baibulo silimatero ndendende... Inu muli nazo zinthu ziwiri zoti muzipenye. Izo zinali... A—akunja anati, “Ziri motani kuti ife tikumumva munthu aliyense mu lirime lathu lomwe ife tinabadwa nalo?” Izo sizinanene kuti iwo anali kuziyankhula izo, koma iwo anali kuzimva izo.

<sup>83</sup> Ndiye gulu lomwelo, anthu omwewo, analongosola ichi. Petro analumphira pa chinachake ndipo anati, “Inu amuna aku Galileya, ndi inu okhala mu Yerusalemu, lolani ichi chidziwike kwa inu (anthu amati iwo analibe chinenero cha Chigalilea)—lolani ichi chidziwike kwa inu ndipo mvetsarani kwa mawu anga (chiani—kodi ndi chinenero chanji chimene iye anali kuchiyankhula, kwa onse awo?); bwanji, awa sanaledzere monga inu mukulingalira, powona kuti ndi ora lachitatu la tsiku, koma ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli: ‘Ndipo zidzafika pochitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga pa mnofu wonse. Ana anu aamuna ndi aakazi azidzanenera.’” Mopitiriza pitiriza iye anapita, ndipo anati, “Inu ndi manja oyipa munamupachika Mwana wa Mulungu wosalakwa. Davide anali atayankhula za Iye... ‘kusasiya moyo Wake mu gehena, ngakhale kuti Iye alole Woyera Wake Uyo kuti awone chivundi.’” Ndipo anati, “Lolani ichi chidziwike kwa inu kuti Mulungu anamupanga Yesu yemweyu yemwe inu munamupachika zonse Ambuye ndi Khristu.” Ndipo pamene iwo anamva izi... Amen! Ndani? Munthu aliyense pansa pa miyamba. Nchiani chinali kuchitika?

Iye sanali kunena, “Tsopano, ine ndiyankhula mu Chigalilea; ine ndiyankhula mu *ichi*; ndipo ine ndiyankhula mu *ichi*. . . ? . . .”

<sup>84</sup> Pamene Petro anali kuyankhula mawu awa, iwo anati, “Amuna ndi abale, kodi ife tingachite chiani kuti tipulumutsidwe?” Ndipo Petro anawapatsa iwo kachitidweko. Ndi momwe izo nthawizonse zimachitikira. Mwaona?

<sup>85</sup> Ndi kusunthira mmwamba, kulimbikira kupita mwa Mulungu, kuyenda kwa pafupi. Inu mukudziwa bwanji? Chabwino tsopano, pamene Lutera analandira Kulungamitsidwa, iye anazitcha izo Mzimu Woyera. Iwo unali. Mulungu anamiza pang’ono pa Iwo mmenemo. Ndiye Iye ananena chiani? Wesile analandira Kuyeretsedwa, ndipo anati, “Mnyamata, pamene iwe ufuula, iwe waulandira Iwo.” Koma ambiri a iwo anafuula amene analibe Iwo. Pamene Pentekoste anayankhula mu malirime—malirime osadziwika, iwo anati, “Mnyamata, iwe uli nawo Iwo.” Koma ambiri a iwo analibe Iwo.

Palibe zinthu zotero zonga zizindikiro izo zodziwira izo. “Njira yokha yomwe iwe umaudziwira mtengo,” Yesu anati, “ndi mwa chipatso chimene iwo umabala,” ntchito za Mzimu, chipatso cha Mzimu. Ndiye pamene inu mumuwona munthu yemwe ali wodzazidwa ndi mphamvu, yemwe ali wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndiye inu mumawona moyo umene uli wosinthika. Inu mumawona zizindikiro izi zikuwatsatira iwo amene akukhulupirirawo: “Mu Dzina Langa iwo azidzatulutsa ziwanda, azidzayankhula ndi malirime atsopano. Ngati njoka idzawaluma iwo, iyo siidzawapweteka iwo. Ngati iwo ati adzakhale ndi chinthu chokupha, nkuchimwa, icho sichikanadzawapha iwo. Iwo azidzaika manja pa odwala, ndipo iwo azidzachira.” Mai! Zizindikiro za mtundu uwu zimawatsatira iwo amene amakhulupirira. Koma inu mumalowamo chotani mmenemo? Mphatso zimenezo ziri mu Thupi. Mumalowamo bwanji mu Thupi? Osati mwa kuyankhula njira yako yoloweramo; koma pobatizidwa kulowa mu Thupi limodzi (1 Akorinto 12:13). Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limenelo ndipo timakhala oyenera mphatso zonse. Ambuye akudalitseni inu.

<sup>86</sup> Tsopano, ngati wina ati ayimve tepi iyi kapena winawake muno angati atsutse, kumbukirani, muzichite izo mwaubwenzi, m’bale, chifukwa ine ndimakukondani inu.

**93. Funso loyamba usikuuno: M’bale Branham, ine ndikuganiza televizioni ndi themberero kwa dziko. Kodi inu mukuganiza chiani za izi?**

<sup>87</sup> Chabwino, yense yemwe analemba ilo, ine ndati ndivomerezane ndi inu. Iwo ayipanga iyo themberero kwa dziko. Iyo ikanakhoza kukhala dalitso kwa dziko, koma iwo aipanga iyo themberero. Chirichonse monga izo, anthu anga okonededwa, ndi chimene iwe umayang’anapo iwemwini. Ngati

televizioni ili themberero, ndiye nyuzipepala ili themberero, ndiye wailesi ili themberero, ndipo nthawi zambiri telefoni ili. Mwaona, mwaona, mwaona, mukuona? Ndi chomwe umapanga kuchokera mwa iyo. Koma pokhala kuti m'bale ananena usiku wina, kuti palibe nkomwe programu iliyonse pa televizioni panonso; pali ndalama zochuluka zambiri. Alaliki osauka omwe amalalikira Uthenga Wathunthu sangakhoze kukwanitsa programu pa televizioni. Chotero ndiye . . . M'bale ananena usiku wina, ine ndikukhulupirira, kapena kwinakwake, "Sasani fumbi pa wailesi yanuyo," kapena winawake, kapena, "Muibwezeretse iyo pa ngodya ndipo muzimvetsera ku maprogramu amenewo." Ndiko kulondola.

<sup>88</sup> Koma, munthu wokonedwa, yense yemwe inu muli, ine ndithudi ndikuvomerezana ndi inu. Iyo yasanduka chimodzi cha zinthu zotemberereka kwa mtundu wa anthu. Mmenemo iwo amatenga ndalama zonse izi zomwe zimayenera kuti zipite ku boma za misonkho, ndi kukaziika izo mu zolengeza pa ndudu zonse izi ndi maprogramu a mowa ndi zinthu zonga izo, ndi kuchotsera pa misonkho ya boma; ndiyeno iwo amabwera ndi kudzawatenga alaliki ndi kuwakokera iwo kubwalo la mulandu kuti akapeze ndalama pang'ono kuchokera kwa iwo. Ine ndikuvomerezana ndi inu, ndi chinthu choyipisitsa. Tsopano, sindicho ayi. . . Inu mukudziwa, ndi chinachake basi chimene iwe umapezamo. Zikomo inu, Mlongo, M'bale, yense yemwe inu muli yemwe munafunsa izo.

**94. Tsopano, pano pali lina labwino. Funso: Alipo malo mu Baibulo onga ngati I Samuele 18:10, amene amati mzimu woipa wochokera kwa Mulungu unachita zinthu. Ine sindiri kumvetsa "mzimu woipa wochokera kwa Mulungu." Chonde tafotokozani izi.**

<sup>89</sup> Chabwino, mwina mwa thandizo la Ambuye, ine ndikhoza. Izi zizikutanthauza kuti Mulungu ndi Mzimu woipa. Koma mzimu uliwonse wa chirichonse ndi womvera kwa Mulungu. Ndipo Iye amapangitsa chirichonse kugwira ntchito molingana ndi zomwe Iye amafuna. Mwaona?

<sup>90</sup> Tsopano, pa funso lanu, inu mukuyankhula za mzimu woipa umene unapita kuchokera kwa Mulungu kuti ukamuzunze Sauli. Iye anali molunda, mmawonekedwe osweka—chikhalidwe, chifukwa, malo oyamba, iye anali atabwerera mmbuyo. Ndipo pamene iwe ubwerera mmbuyo, mzimu woipa—Mulungu amaloleza kuti mzimu woipa uzikuzunza iwe.

<sup>91</sup> Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kwa inu chinachake mu—mu mphindi. Ine ndiri ndi lingaliro lina pa izo pano. Mwaona? Mzimu uliwonse uyenera kukhala womvera kwa Mulungu. Kodi inu mukukumbukira pamene Yehosafati ndi Ahabu anali kupita ku nkondo kuja? Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, apo panali—iwo anakhala ku zipata. Ndipo Yehosafati anali munthu



wolongama, ndipo iye anati (mafumu awiri anakhala apo, ndipo iwo analumikizana mphamvu zawo limodzi)—ndipo chotero iye anati, “Tiyeni tifunsire kwa Ambuye za ngati ife tingati tipite uko kapena ayi.”

<sup>92</sup> Ndipo Ahabu anapita ndipo anakatenga aneneri mazana anai omwe iye anali nawo, onse, ankawasunga iwo nawadyetsa iwo ndi kuwanenepesa ndi chirichonse; iwo anali mumawonekedwe abwino. Ndipo iwo anabwera pamene, ndipo iwo onse analosera ndi mtima umodzi, anati, “Pitani uko, ndipo Mulungu akakupatsani inu chigonjetso. Pitani ku Ramoti-gileadi uko ndipo kumeneko Mulungu akakutengerani inu chinthucho.” Mmodzi wa iwo anadzipangira yekha nyanga ziwiri ndipo anayamba kumazungulira ngati molongosolera, anati, “Ndi nyanga zachitsulo izi, inu mukawakankha iwo mpaka kuwachotsa mu dzikolo; ndi la inu.”

<sup>93</sup> Koma inu mukudziwa, pali chinachake chokhudza munthu wa Mulungu kuti samangopitira zonse izo. Mwaona? Ngati icho sichikumveka bwino ndi Lemba, pali chinachake cholakwika. Wokhulupirira woona aliyense...Kotero Yehosafati anati, “Chabwino, foro handiredi awo akuwoneka bwino. Iwo akuwoneka ngati anthu abwino.”

“O, iwo ali,” mwina mwake Ahabu anatero.

Koma Yehosafati anati, “Kodi inu mulibe mmodzi wina?” Bwanji mmodzi wina pamene inu muli nao foro handiredi mchigwirizano chimodzi? Chifukwa iye ankadziwa kuti panali chinachake chimene sichinkamveka mwabwino basi. Mwaona?

Iye anati, “Inde, ife tiri naye mmodzi wina, mwana wa Imlah, kuntunda kuno,” anati, “koma ine ndimadana naye iye.” Zedi. Inu mungatseke tchalitchi chake nthawi iliyonse inu mungakhoze. Inu mungamthamangitse iye achoke mu dzikolo. Mwaona? Zedi. “ine ndimadana naye iye.”

“Nchifukwa chiani inu mumadana naye iye?”

“Iye nthawizonse amalosera zoipa motsutsana ndi ine.” Ine ndikukhulupirira Yehosafati anadziwa apo pomwe panali—chinachake sichinali bwino.

Kotero iye anati, “Pitani ndipo kamutengeni Mikaya.”

Chotero iwo anapita kukamufuna iye, ndipo apa iye anabwera uko...Kotero pamene iwo anapita uko, iwo anatomiza mthenga ndipo anati, “Tsopano, dikirani miniti. Tsopano, iwo ali ndi Madokotala Azauzimu mazana anai kumeneko. Iwo ndi opambana omwe alipo mu dzikolo, okhala ndi Ph, ma LLD, ndi chirichonse.” Anati, “Tsopano, iwe ukudziwa, iwe munthu wamng’ono wosauka wosaphunzira, iwe suti ukatsutsane ndi alaliki onse awo.”

<sup>94</sup> Imlah ananena izi, kapena ine ndikutanthauza, Mikaya ananena izi: “Ine sindinena kanthu mpaka Mulungu ataika icho

mkamwa mwanga, ndiyeno ine ndinena ndendende chimene Iye wanena.” Ine ndikuzikonda izo. Ine ndikuzikonda izo. Mwa kuyankhula kwina, “Ine ndikhala nawo Mawu.” Ziribe kanthu zomwe ena awo ananena. Iye anati, “Chabwino,” anati, “Ine ndikukuuza iwe. Ngati iwe sukufuna kuti utaidwe kunjani, iwe kulibwino unene chinthu chomwecho.”

Kotero iye anapita uko. Ndipo iye anati, “Kodi ine ndipite uko?”

Iye anati, “Zipitani.” Anati, “Ndipatseni ine usikuwu. Mundilole ine ndikambirane izo ndi Ambuye.” Ine ndikuzikonda izo. Chotero usiku umenewo Ambuye anawonekera kwa iye, ndipo tsiku lotsatira iye anapitako. Ndipo iye anati, pamene iye anali kupita uko, iye anati, “Zipitani; koma ine ndinawona Israeli ngati nkhusa zopanda m’busa, atamwazikana pa mapiri.” O, mai! Izo zinaphwesa mpweya mwa iye.

Ndipo iye anati, “Kodi ine sindinakuuzeni inu? Ine ndimadziwa izo. Umo ndi ndendende momwe iye amachitira nthawizonse, kunena chinachake choipa monditsutsa ine.”

<sup>95</sup> Bwanji? Iye anali kukhala ndi Mawu. Chifukwa? Mneneri asanadze iyeyu, Mawu a Mulungu ochokera kwa Eliya, mneneri weniweni, iye anati, “Chifukwa iwe wakhetsa magazi a munthu wosalakwa Naboti, agalu adzanyambita magazi ako nawenso.” Ndipo anamuuzza iye zoipa. Elisha anali atapita kale Kumwamba. Koma iye ankadziwa kuti Elisha anali ndi Mawu a Mulungu, chotero iye ankakhala ndi Mawu. Ine ndikuzikonda izo. Kukhala ndi Mawu.

<sup>96</sup> Ngati Baibulo linati Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; mphamvu Yake ikadali pano yofanana; Mzimu Woyera ndi wa aliynense yemwe akufuna, mulole iye adze, khalani ndi Mawu. Inde, bwana! Ziribe kanthu zomwe ena onsewo akunena. Kaya ndi odyetsedwa bwino bwanji ndi masukulu angati omwe iwo adutsamo, izo ziribe kanthu kochita ndi izo.

Chotero ndiye iye anati. . . Munthu wamkulu uyu ali ndi nyanga pa mutu wake, mukazikankha izo—dzikolo kulilanda kwa mfumu, iye anayenda mpaka anadzamumenya iye pa kamwa (mlaliki wamng’ono uyu). Iye anazindikira kuti iye anali woyera wodzigudubuza wamng’ono basi chotero palibe kanthu kamene kakanati kanenedwe pa izo, chotero iye anangomubwanyula iye pa kamwa. Iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndikufunse iwe chinachake.” Anati, “Ndi njira iti yomwe Mzimu wa Mulungu unapita pamene Iwo umachoka mwa ine ngati iwe uli nawo Iwo?”

<sup>97</sup> Iye anati, “Iwe ukamvetsa pamene iwe uti ukakhale mu linga kutali uko ngati wogwidwa.” Iye anati, “Ine ndinamuwona Mulungu atakhala pa mpandowachifumu (Ameni! Tsopano mvetserani!), ndipo khamu la Kumwamba linasonkhana momuzungulira Iye.” Nchiani chinali chovuta? Mneneri

wake anali atanena kale zomwe zikanati zidzachitike kwa Ahabu. Mulungu...Uyo sanali Eliya yemwe ananena izo; uyo anali mneneri wodzozedwa. Amenewo anali Mawu a Ambuye, PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndipo Mikaya anati, “Ine ndinaliwona khamu lonse la Kumwamba litasonkhana momuzungulira Mulungu mu msonkhano waukulu. Ndipo iwo anali kuyankhulana wina ndi mzake. Ndipo Ambuye anati, ‘Ndani yemwe Ife tingamutenge kuti apite uko—ndi ndani wa inu yemwe angapite uko ndi kukamunyenga Ahabu, kuti akamutengere iye kunja uko kuti akakwaniritse Mawu a Mulungu, kuti akamupangitse iye kulasidwa? Ndani yemwe Ife tingamupeze kuti apite kumeneko?’”

<sup>98</sup> Chabwino, mmodzi anali kunena *uyu* kapena mmodzi *uyo*. Ndipo patapita kanthawi, mzimu woipa, mzimu wabodza unabwera kuchokera pansu ndipo unati, “Ngati Inu mutangondilola ine. Ndine mzimu wabodza. Ine ndipita uko ndi kukalowa mwa alaliki onse awo, chifukwa iwo alibe Mzimu Woyera; ndipo ine ndiwapangitsa iwo (iwo angokhala anyamata ophunzitsidwa ndi sukulu)—ndipo ine ndipita uko, ndi kukalowa mwa aliyense wa iwo, ndi kukawanyenga iwo, ndi kukawapangitsa iwo kunenera bodza.” Kodi iye ananena zimenezo? Ndipo iye anati, “Ndi momwe ife titi tiwanyengere.” Chotero iye anapita uko.

Iye anati—Mulungu anati, “Iwe uli ndi chilolezo Changa kuti upite.”

<sup>99</sup> Ndipo iye anapita uko ndipo anakalowa mwa aneneri abodza awo, utumiki wophunzitsidwa ku sukulu, ndipo anawapangitsa iwo kunenera bodza. Uwo unali mzimu wabodza ukugwira ntchito kwa chifuniro cha Mulungu. Mundirole ine...Basi chinachake chimene inu mungati onani pano, miniti yokha. Penyani izi. Ine ndikufuna kuti inu mutembenuze ndi ine ku I Akorinto mutu wa 5, ndime yoyamba, miniti yokha. I Akorinto...Ndipo penyani ichi ngati inu mukufuna kuti muwone chinachake, cha Mulungu akupanga chinachake—momwe kuti mizimu yoipa iyo, momwe kuti iyo ima—iyo imayendera...Chabwino, Paulo akuyankhula:

*Ziri kunenedwa mwawamba kuti pali ziwerewere pakati panu, ndipo ziwerewere zotero zomwe ziri... siziri kutchulidwa pakati pa Amitundu... (Kodi inu mukuganiza chiani za izo pakati pa mpingo?)...kuti wina akumakhala ndi mkazi wa abambo ake.*

*Ndipo inu mukudzitukumula, ndipo mulibe... (Tiyeni tiwone. Ine ndikukhulupirira ine ndinatembenuza masamba awiri apa...). Inu muli—Ndipo inu mukudzitukumula, ndipo inu simunati maka muzilirire, izo... (Tsopano, dikirani miniti apa. Ine ndine...Eya, ndiko kulondola. Eya)...kulira... (Ndi choncho)...*

*kudzitukumula, ndipo simunati...mulire, kuti uyo yemwe wachita ichi akhoze kuchotsedwa pakati panu.*

100 Ndine—sindikudziwa. Ine sindikukhulupirira kuti aliyense akanati anene kwa izi kapena kudulapo, koma ine ndikungotetezera pa chimene ine ndimakhulupirira: Ngati munthu adzazidwapo kamodzi ndi Mzimu iye sangakhoze kuwutaya Iwo. Mwaona, mukuona?

*Pakuti Ine ndithudi, monga sindiripo mu thupi, koma ndiripo mu mzimu, ndaweruzza kale, ngati kuti ine ndinalipo, za iye yemwe wachita izo chotere,*

*Mu dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, pamene inu musonkhana pamodzi, ndipo mzimu wanga, ndi mphamvu ya Ambuye Yesu Khristu,*

*Kuti mumupereke woteroyo kwa Satana kuti thupi lake liwonongedwe, kuti mzimu udzakhoze kupulumutsidwa mu tsiku la Ambuye Yesu.*

101 Mulungu, akuwuuzza Mpingo woyera, umene uli Thupi Lake kuno pa dziko lapansi, kuti (tsopano, izi ndi chitachitika Chipangano Chakale, mu Chatsopano)—akumuuzza munthu yemwe anali woipa kwambiri ndi wauve pakati pa anthu kuti iye ankagona ndi mkazi wa abambo ake omwe. Anati, “Chinthu choterocho mu Thupi la Khristu...Inu, Mpingo, mumpereke iye kwa mdierekezi ku chiwonongeko...” Mwaona? Mulungu amalola...Ndipo pamene Iye anali ndi chinachake chimene Iye amayenera kuwona kuti chachitidwa, kuti ayike chikwapu pa winawake, Iye amamasulira mzimu woipa pa iwo chotero kuti umuzanze munthu ameneyo ndi—ndi kuwabweretsanso iwo. Tsopano, ife tikumupeza munthu uyu pambuyo...

102 Ndi lomwe liri vuto ndi mipingo lero. Pamene munthu abwera mu Thupi la Khristu ndi kukhala mmodzi wa ziwalo nayamba kuchita choipa, mmalo moti inu nonse mubwere limodzi ndi kuchita chinthu chomwe chomwechi...Ndipo inu, Branham Tabernacle, muzichita izo. Chifukwa utali wonse womwe inu mukumugwirizira iye, iye ali pansa pa Magazi. Ndipo iye amangopitiriza kumachita zinthu zakale zomwezo mobwereza bwereza nthawi zonse. Inu muzibwera palimodzi ndi kumupereka iye kwa mdierekezi kuti awonongedwe thupi, kuti mzimu wake uli—monga—ukhoze kudzapulumutsidwa mu tsiku la Ambuye. Ndipo muwone chikwapu cha Mulungu chikubweramo. Mumuwone mdierekezi atamugwira iye. Ndiwo mzimu woyipa utamutenga iye.

103 Ndipo mnyamata uyu apa anawongoledwa. Iye anabwerera. Ife tikuzipeza mu I Akorinto pamene iye anadzitsuka kwenikweni pamaso pa Mulungu.

104 Tayang’anani pa Yobu, munthu wamngwiro, munthu wolungama. Ndipo Mulungu analoleza mdierekezi woipa kuti abwere pa iye, ndi kumukwapula iye, ndi china chirichonse kuti

akaupange mzimu wake kukhala wangwiro. Mwaona? Koteru mzimu woipa uli. . . Mulungu amagwiritsa ntchito mizimu yoipa nthawi zambiri kuti achite dongosolo Lake ndi chifuniro Chake.

**95.** Tsopano, pano pali limodzi lomwe liri lomata kwenikweni. Funso (ine ndikuganiza ndi munthu yemweyo, chifukwa iko kukuwoneka ngati kulemba kofanana): **Ngati munthu ayenera kukhala nao Mzimu Woyera kuti akhale—akhale nao Mzimu Woyera kuti atembenuzidwe ndi kuti apite mu mkwatulo, chidzakhala chotani chikhalidwe cha ana omwe anafa asanafike zaka za kuzindikira? Ndipo ndi liti pamene iwo ati adzauke?**

<sup>105</sup> Tsopano, m'bale wanga, mlongo, ine sindingakhoze kukuuzani inu zimenezo. Palibe Lemba pa izo mu Baibulo lomwe ine ndingakhoze kulipeza paliponse. Koma ine ndikhoza kufotokoza maganizo anga. Tsopano, izi zikulimbikitsani inu amene mumakhulupirira mu chisomo cha Mulungu. Inu mukuona, munthuyu akufuna kuti adziwe (lomwe liri funso labwino kwambiri. Mwaona?)—munthuyu akufuna kuti adziwe chiukitsiro chiti—nchiani chiti chidzachitike kwa mwana, kuti ngati zimatengera kuti ukhale nao Mzimu Woyera polinga kuti udzapite mu mkwatulo. . .Monga ine ndanenera, ndiko kulondola. Ndizo zolingana ndi Baibulo. Ndiko kuphunzitsa kwa Lemba. Osati kuti—osati kuti upite Kumwamba. . . Chifukwa anthu odzazidwa ndi Mzimu Woyera ndi a chiukitsiro choyamba, Osankhidwa. Ndi otsalira a iwo. . .Akufa onse sadzakhalanso moyo kwa zaka chikwi. Zitatha Zakachikwi, kenako chiukitsiro chachiwiri, chiweruzo cha ku Mpando Woyera. Mwaona? Ndilo ndendende dongosolo la Baibulo. Koma munthu uyu akufuna kuti adziwe kuti nanga bwanji ana awa. Iwo. . .Mwa kuyankhula kwina, kodi iwo anali nao Mzimu Woyera iwo asanabadwe? Kodi iwo anaulandira Iwo? Tsopano, izo ine sindingakhoze kukuuzani inu.

<sup>106</sup> Koma tsopano, tiyeni ife tinene monga chonchi: Ife tikudziwa kuti ana amene amafa, mosasamala za makolo awo, iwo ali opulumutsidwa. Tsopano, ine sindigwirizana nayo sukulu ya aneneri pa izo. Iwo amati ngati izo zinali—anafa ali ndi kholo lomwe linali lochimwa, kuti mwana ameneyo akanati apite ku gehena, kukavundako; sipakanadzakhalanso kanthu kwa iye. Chabwino, Yesu. . .Yohane anati pamene Yesu anadza, “Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la ndzi.” Ndipo ngati mwana uyo anali munthu wokhalapo, yemwe akanati adzabwere pansu pa ziweruzo za Mulungu, ndipo Yesu anafa kuti achotse tchimo, tchimo lonse linachotsedwa pamaso pa Mulungu pamene Yesu anafera cholinga chimenecho. Machimo anu anakhululukidwa. Machimo anga anakhululukidwa. Ndipo njira yokha yomwe iwe ungakhoze kukhululukidwa konse ndiyo pa kulandira chikhululukiro Chake. Tsopano, mwana sangakhoze kulandira

chikhululukiro chake, chotero iye sanachite kalikonse. Iye sanachite nkomwe kalikonse. Chotero iye ali mwamtheradi waufulu kuti apite Kumwamba.

<sup>107</sup> Koma inu mukuti, “Kodi iwowo adzapita mu mkwatulo?” Tsopano—tsopano, awa ndi mawu anga anga; ili ndi lingaliro langa tsopano. Musati... Ine sindingakhoze kutsimikizira izi ndi Baibulo. Koma yang’anani. Ngati Mulungu, asanaikidwe maziko a dziko, anamdziwa munthu wokhalapo aliyense yemwe akanati adzakhale konse pa dziko lapansi... Kodi inu mukukhulupirira izo? Iye anamdziwa tongole aliyense, utitiri uliwonse, ntchentche iliyonse, Iye anadziwa chirichonse chimene chikanati chidzakhalepo konse pa dziko lapansi. Ngati Iye anazidziwa izo... .

<sup>108</sup> Penyani. Tiyeni titenge mwa chitsanzo, Mose. Pamene Mose anabadwa, iye anali mneneri. Asanakhalepo Yeremia... Mulungu anamuza Yeremia, “Iwe usanaumbidwe nkomwe mu mimba ya amayi ako, iwe usanaumbidwe nkomwe mu mimba yao, Ine ndinakudziwa iwe, ndipo ndinakuyeretsa iwe, ndipo ndinakudzozeratu iwe mneneri kwa mafuko.” Yohane M’batizi, zaka 712 iye asanabadwe, Yesaya anamuwona iye mu masomphenya, anati, “Iye ali liwu la wina wofuula mu chipululu.”

<sup>109</sup> Kukonzeratu kapena kudziwiratu kwa Mulungu kumadziwa zonse za tiana tating’ono (mwaona?), zomwe iwo anali woti adzachite. Ndipo Iye anadziwa kuti iwo akanati adzafe. Iye anadziwa. Palibe kangakhoze kuchitika popanda Mulungu kudziwa za iko. Palibe kanthu kangakhoze kuchitika... Chimodzimodzi monga M’busa Wabwino, momwe Iye amaloweramo... Tsopano, kuti titenge izi mwa Lemba, ine sindikanati Lemba limati *zakuti-n-zakuti*. Ine ndikungozitenga izo kuchokera ku malingaliro anga.

**96.** Tsopano, funso lotsatira ndi lomwe ine ndikuganiza kuti mwinamwake wina anali—chimene ine ndinanena usiku wina. **Tafotokozani za mkazi kuti apulumutsidwe pa kubala ana.**

<sup>110</sup> Mkazi samapulumsidwa pa kubala ana. Koma tiyeni titembenuze tsopano ku 1 Timoteo 2:8 miniti yokha. Ndipo tiyeni tingofufuza chomwe Baibulo limanena zokhudza mwana. Tsopano, ine ndikuzindikira icho ndi chiphunzitso cha Chikatolika, kuti Akatolika amati mkazi amapulumsidwa pa kubala kwa ana, pa kubala ana. Koma tiyeni tisati... Ine sindimakhulupirira zimenezo. 1 Timoteo mutu wa 2, ndipo tiyeni tiyambire pa ndime ya 8, ndi kuwerenga kamphindi kokha tsopano. Chabwino, mveterani.

*Mu kachitidwe kofanana aponso, kuti akazi anu azidzikometsera okha ndi zovala zaulemu... (Ife sitikusowa kufunsa zimenezo, si choncho ife?)*

Tamvetserani kwa izi)...ndi nkhope yamanyazi... (Fyuuu!)...ndi *kudekha*; *osati ndi kumanga tsitsi lake ndi, kapena golide, kapena ngale, kapena zovala zodula*; (Abale, ine ndikukuthandizani inu apa, ine ndikuyembekeza. Zibenenga zonse zatsopano izi tsiku lirilonse kapena pa masiku atatu. Inu mukuona? Izo si monga amakhalira Akhristu.)

*Koma (zomwe ziri zoyenera akazi odzinenera umulungu) ali ndi zintchito zabwino.*

*Mulole akazi anu aziphunzira mwachete ndi kumvera konse.*

*Koma ine sindimalola kuti mkazi aziphunzitsa, kapena kutenga ulamuliro pa...mwamuna, koma kuti azikhala...chete.*

*Pakuti Adamu anapangidwa poyamba, ndipo kenako Eva.*

*...Adamu sananyengedwe, koma mkaziyo pokhala atanyengedwa anali mu cholakwira.*

*Popanda choletsa iye adzapulumutsidwa pa kubala ana, ngati... (Tsopano, Iye sali kuyankhula kwa mkazi wa mdziko, pokhala ndi ana)...ngati iye apitirira mu chikhulupiriro... (Mukuona? Ngati iye apitirira. Iye ali kale... Uyo ndi mkazi yemwe iye akumukamba, mkazi yemwe ali wopulumutsidwa kale. Mukuona?)... ndi chikondi ndi chihero ndi kudekha konse.*

111 Osati pa kukhala ndi ana zikumupanga iye kukhala wopulumutsidwa, koma chifukwa kuti iye akulera ana, akuchita ntchito yake, osati kulera amphaka, agalu, ndi zina zoonjezera kuti zitenge malo a mwana, momwe iwo akuchitira lero, kuzipatsa izo chikondi cha mayi kuti iye azikhoza kumapita ndi kumakathamanga paliponse usiku wonse. Anthu ena amachita zimenezo. Pepani, koma iwo amachita izo. Izo ndi zamwano kwambiri kuti ine ndizinene, koma choonadi ndi choonadi. Mwaona? Iwo samamufuna mwana kuti azimangiriridwa pansu naye. Koma pa kubala ana, ngati iye akupitirira mu chikhulupiriro, chihero, ndi kudekha konse, iye adzapulumutsidwa. Koma *ngati* uyo ali, iwe udzapulumutsidwa nawenso, bola uli wobadwa mwatsopano. Iwe udza—iwe ukhoza kuchiritsidwa *ngati* iweyo ukukhulupirira. Iwe ukhoza kulandira Mzimu Woyera *ngati* iweyo ukukhulupirira Iwo, kukonzekera Iwo, *ngati* inu mwaukonzekera Iwo. Ndipo iye adzapulumutsidwa *ngati* iye apitiriza kumachita zinthu izi (mwaona?), koma osati chifukwa iye ndi mkazi. Chotero uko ndi kulondola, m'bale, mlongo. Si chiphunzitso cha Chikatolika konse. Tsopano, ine ndikufuna...Pano pali lina lomwe liri lomata kwambiri. Ndiye ife tiri nalo linanso. Ine ndikuganiza mwina ife tiri nayo nthawi kwa ilo. Ine ndinangotenga nthawi

yathu. Tsopano, izi zangokhala—izi zangokhala zotsatira za chitsitsimutso. Izi ndi zotsatira za msonkhano, mafunso awa.

**97. Tsopano: M’bale Branham (ndi lotaipidwa), kodi ndi Lemba kuti munthu aziyankhula mu malirime ndi kutanthauzira uthenga wake womwe? Ngati ziri choncho, chonde tafotokozani I Akorinto—kapena Akorinto 14:19 ndiponso Akorinto 14:27.**

<sup>112</sup> Chabwino, tiyeni tipite ku Lemba limenelo ndi kuona chomwe ilo likunena. Ndiyeno ife tiwona ngati ife tikuzisunga izi Mwamalemba. Ife tikufuna kuti nthawizonse tizikhala Mwamalemba. Ndi Akorinto 14. Tsopano, munthuyu akufuna kuti adziwe ngati ziri Mwamalemba kuti munthu azitanthauzira uthenga wake womwe umene iye anauyankhula mu malirime. “Ngati ziri choncho, tafotokozani Akorinto 14:19.” Tiyeni tione, 14 ndi 19. Chabwino, ife tiri apa.

*Komabe mu mipingo ine... kulibwino ndiyankhule mawu asanu ndi kumvetsa kwanga, kuti ndi liwu langa ndikhoze kuphunzitsa ena akenso, kuposa zikwi khumi... mu... malirime osadziwika.*

Tsopano, yotsatira ina ndi ndime ya 27, iwo akufuna kuti ayidziwe.

*Ngati munthu aliyense ayankhula mu lirime losadziwika, mulole izo zikhale ndi awiri, kapena mwa... ochulukitsa mwa atatu, ndipo awo motsatizana; ndi kumulola wina atanthauzire.*

<sup>113</sup> Tsopano, ine ndikutenga zomwe munthuyu akuyesera kuti afikepo (chimene ine ndikufuna—ine ndikuti ndiwerenge chinachake kwa inu kwa mphindi yokha). Koma ine ndikuganiza chimene m’bale kapena mlongo akuyesera kuti afikepo, “Kodi ndi choyenera kuti munthu yemwe akuyankhula mu malirime kutinso atanthauzire uthenga umene iye waunena?” Tsopano, mzanga wofunika wokonedwa, ngati inu mutangowerenga ndime ya 13 mu mutu womwewo, iwo ukuuzani inu:

*Chomwecho mulole iye amene ayankhula mu lirime losadziwika apemphere kuti iyeyo akhoze kutanthauzira.*

<sup>114</sup> Zedi. Iye akhoza kutanthauzira uthenga wake womwe. Tsopano, ngati ife titangoti... Tiyeni tingo... Chabwino, inu... Werengani zonse izo apa, ndipo inu mukhoza kuwona Ziri... Ingowerengani mutu wonsewo. Ndi zabwino kwambiri, kufotokoza izo.

<sup>115</sup> Tsopano, kuyankhula mu malirime... Tsopano, pamene ife tikadali pa izo, ndipo izi pokhala zikujambulidwa, ine ndikufuna kunena kuti ine ndimakhulupirira mochuluka basi kuyankhula mu malirime monga ine ndimakhulupirira mu machiritso Auzimu, ndi—ubatizo wa Mzimu Woyera, kudza kwachiwiri kwa



Khristu, ndi mphamvu ya dziko likudzalo; ine ndimakhulupirira mochuluka basi mu izo momwe ine ndimakhulupirira, koma ine ndimakhulupirira kuyankhula mu malirime kuli ndi malo ake basi monga kudza kwa Khristu kuli ndi malo ake; machiritso Auzimu ali ndi malo ake; chirichonse chiri ndi malo ake.

<sup>116</sup> Tsopano, kwa inu anthu, ine ndiri nawo mwayi woti ndinene izi tsopano, ndipo ine ndikanafuna kuti ndizifotokoze izi. Ndipo ngati ine ndimupweteka aliyense, ine sindikutanthauza kutero. Ine sindikutanthauza kuti ndiyambitse chisokonezo. Koma mvetserani. Chakhala chovuta ndi chiani ndi kuyankhula mu malirime osadziwika ndi anthu Achipentekoste (amene ndiri inemwini; Ine ndine Wachipentekoste. Mwaona?)... Tsopano, lomwe lakhala vuto ndi ili: kuti—iwo samazilemekeza izo. Ndipo chinthu china, iwo amangozilola izo zizipita mwachisawawa. Iwo samabwerera ku Mawu.

<sup>117</sup> Tsopano mvetserani. Njira yake ndi iyi—mulole—umu ndi momwe mpingo wakhazikitsidwira. Tsopano, mu mpingo wa Chipentekoste, ngati ine ndikanamachita ubusa mpingo uno, ine ndikanakuuzani inu momwe ndikanati ndiukhazikitsire iwo (mwaona?), ngati ine ndikanakhala—ndikanati ndikhale pano nthawi yonse kuti ndizichita ubusa pa iwo. Ine ndikanamathandizira ku mphatso iliyonse ya mu Baibulo. Kuwauza okhulupirira choyamba kuti azibatizidwa mu Mzimu Woyera. Ndiyeno, mphatso iliyonse ya I Akorinto 12 ikanati izigwira ntchito mu mpingo wanga, ngati ine ndikanakhala nawo iwo mmenemo, thupi lonse likugwira ntchito.

<sup>118</sup> Tsopano, ngati inu mutazindikira... Osati kupanga ndemanga tsopano. Ndipo kumbukirani, ine sindikanati ndinene mawu amodzi mosiyana—ine ndikanati ndichitire mwano Mzimu Woyera. Ndipo Mulungu akudziwa ine sindikananena izo molakwitsa. Mwaona? Koma ine ndikungonena izi kuti ndiyese kukupatsani inu momwe Lemba likuwonekera ine nditaziphunzira izo tsopano kwa pafupi zaka twente. Ine ndakhala ndikulalikira kwa pafupi zaka sate. Ndipo ine ndadutsa kumene mu chirichonse, kumangokoka basi podutsa; inu mukhoza kulingalira momwe izo zakhallira ziri. Ndi pomuyang'ana munthu aliyense, ndi chiphunzitsa chake, ku dziko lonse. Ndi kumazitenga izo chifukwa ndi chondisangalatsa changa. Ndi chosangalatsa kwa anthu okhalapo pambali pa inemwini. Ine ndiyenera kuchokako kuno. Inu muyenera kuchokako kuno. Ndipo ngati ine ndipita ngati mneneri wabodza, ine ndidzataya moyo wanga womwe ndi kutaya wanu limodzi nane. Chotero ndi zoposa—ndi zoposa mkate wa pa tsiku; ndi zoposa kuchuka; ndi zoposa china chirichonse; ndi moyo kwa ine. Mwaona? Ndipo ine ndikufuna nthawizonse kukhala mwa kuya kwambiri kwa kudzipereka.

<sup>119</sup> Tsopano, inu mukapita mu mpingo wa Chipentekoste, chinthu choyamba... (ine sindikutanthauza onse a iwo. Ena

a iwo ali... ) Nthawi zochuluka iwe ukalowa mu tchalitchi ndi kuyamba kulalikira; pamene iwe ukulalikira, wina amauka ndi kuyankhula mu malirime. Tsopano, munthu wokondeka uyo akhoza kukhala ali mwangwiro wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo uwo ukhoza kukhala uli Mzimu Woyera ukuyankhula kupyolera mwa munthu ameneyo, koma chinthu chake ndi choti, iwo ali osaphunzitsidwa. Ngati utumiki uwu pa nsanja uli kuyankhula pansu pa kudzoza, mzimu wa aneneri umamunvera mneneri. Mwaona? “Mulole zinthu zonse zizichitidwa...” Tsopano, fikani umu mwa Paulo chifukwa chimene iye akunenera kuti “pamene wina ayankhula,” ndi zina zotero... “pamene iye anabwera, izo zinangokhala chisokonezo.”

<sup>120</sup> Tsopano, ine ndakhala ndikupanga kuitanira paguwa, ndipo wina amaima ndipo amayankhula mu malirime. Izo basi... Chabwino, iwe kuli bwino ungosiya kupanga kuitanira pa guwa. Izo zimaletsa iko. Mwaona?

<sup>121</sup> Ndiyeno, chinthu china. Nthawi zambiri anthu amauka ndipo amayankhula mu malirime, ndipo anthu amakhala ndi kumatafula chingamu, akuyang’ana uku ndi uko. Ngati Mulungu ali kuyankhula, khala bata, zimvetsera! Ngati icho chiri Choonadi, ngati umenewo uli Mzimu Woyera ukuyankhula mwa munthu ameneyo, iwe ukhale chete ndi kumamvetsera, khala molemekeza. Kutanthauzirako kukhoza kubwera kwa iwe. Mwaona? Khala bata; zimvetsera kutanthauzira kwake. Tsopano, ngati palibe wotanthauzira mu mpingo, ndiye iwo amayenera kuti azikhala bata mu Thupilo.

<sup>122</sup> Ndiyeno, pamene iwo ayankhula ndi lirime losadziwika, Baibulo linati, mulole iwo akayankhule kwa okha kwa iwo ndi Mulungu. Iye amene amayankhula mu malirime osadziwika amadzilimbikitsa yekha. Tsopano, amenewo ndi malirime osadziwika; ziyankhulo, zinenero ndipo zosiyana. “Izo siziri kanthu,” iye akutero... Koma chimene chimapanga phokoso chiri ndi tanthauzo. Koma inu... Ngati lipenga liwomba, iwe umayenera kudziwa momwe ilo likulirira (...kungoliwomba ilo) kapena iwe sungadziwe momwe ungasadzikonzekere wekha ku nkhondo. Ngati aliyense ayankhula mu malirime, ndi kungoti “tutu”; ndi zonse zomwe ziripo kwa ilo, ndani ati adziwe choti achite. Koma ngati ilo liyamba *tetelite*, izo zikutanthauza “ukani!” Ngati ilo liwomba *mogunda*, izo zikutanthauza “khalani pansu.” Mukuona? Ngati ilo liwomba *mwaukali* izo zikutanthauza “pitani mwamphamvu.” Ilo liyenera kupereka tanthauzo, ndipo osati kungoyankhula kokha. Chotero mu mpingo, ngati mulibe wotanthauzira, koma momwe muli wotanthauzira, ndiye malirime ndi omwe ali a mu mpingo.

<sup>123</sup> Tsopano, ku funso lanu, mzanga wokondeka, lomwe likuti, “Ine kulibwino ndiziyankhula zikwi zisanu... mawu asanu mu, ndi chotero kuti anthu azikhoza kumandimvetisa ine kuposa zikwi zisanu (kapena ena aliwonse ochulukira amene akuwanena)

mu lirime losadziwika.” Izo nzoona. Koma werengani mpaka pansi: “...kupatula ngati izo zikhala mwa vumbulutso kapena mwa kutanthauzira kuti zilimbikitse.” Mwaona? Kuti umangirize.

<sup>124</sup> Tsopano, ine ndingokhala ngati ndikupatseni inu kalingaliro kakang’ono bwanji ngati—chiani...Ngati ine ndinali woti ndichitire ubusa mpingo uno umene ukudzapo, ngati Mulungu akanandiyitana ine kuti ndichite ubusa pa iwo, umu ndi momwe ine ndikanauyendetsera iwo: ine ndikanayesera kuti ndimupeze munthu aliyense mmenemo yemwe ali nayo mphatso. Ndipo ine ndikanati anthu amenewo kuti azikomana pafupi ora misonkhano isanayambe konse, mu chipinda kwa okha. Kumawalola iwo kuti akhale pansi pa Mzimu. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, wina abwera apo yemwe ali nayo mphatso yoyankhula mu malirime. Ndipo iye ayankhula mu malirime. Aliyense atakhala chete. Ndiyeno wina aimirirapo ndi kutanthauzira zomwe iye wanena. Tsopano, izo zisanaperekedwe kwa mpingo, Baibulo limati izo ziyenera kuti ziweruzidwe pakati pa mboni ziwiri kapena zitatu. Tsopano awo ndi amuna omwe ali nako kuzindikira kwa Mzimu (mwaona?), chifukwa nthawi zambiri mphamvu zoipa zimalowa mmenemo. Paulo anayankhula za izo. Komano, mphamvu ya Mulungu ili mmenemonso. Ndiuzeni ine gulu mmene choipa sichimakhalamo. Ndiuzeni ine pamene ana a Mulungu amasonkhana palimodzi kumene Satana samakhala pakati pa iwo. Ndi chirichonse. Chotero musamachitire tsinya pa izo. Mukuona? Satana ali paliponse. Tsopano, ndi ife pano. Wina akuyankhula mu malirime. Tsopano, alipo atatu amene ali apo omwe ali nao Mzimu wa kuzindikira. Ndipo wina anayankhula mu malirime napereka uthengawo. Tsopano, izo sizingakhoze kukhala kubwereza Lemba, chifukwa Mulungu samagwiritsa ntchito kubwereza kwachabe, ndipo Iye anatiuza ife kuti tisamatero. Mwaona? Chotero si zimenezo. Ndi uthenga wa kwa mpingo.

<sup>125</sup> Ife takhalapo nazo zinthu ziwiri mu chitsitsimutso ichi mpaka pano. Penyani chomwe chirichonse cha izo chinali—mwangwiro, mpaka pa dontho. Mwaona? Zinasunthira mkati. Mwamuna mmodzi anaimirira, ndipo anayankhula mu malirime, ndipo anapereka kutanthauzira, ndipo anatembenukira mmbuyo chozungulira, ndipo anadzautsimikizira uthenga umenewo umene unangopitapowo. Mmodzi wina anauka usiku wina, ndipo ananena mu—pansi pa kudzoza kwa ulosi, ndipo ananena chinachake, asakudziwa chimene iye anali akunena; ndiyeno pa mapeto iye anayankhula kuti, “Wodala ali iye yemwe adza mu Dzina la Ambuye.” Mwamsanga chinachake chinandigwira ine mofulumira kumene ndipo ndinati, “Mwinamwake wodala ali iye yemwe akukhulupirira kuti awa ndi Ambuye amene abwera.”

<sup>126</sup> Mwaona kuma—ndiye Mzimu Woyera unagwa mu chipinda usiku watha. Mwaona? Izo ndi zolimbikitsa. Ine ndinali nditaima apo ndikuyesera kuwauza anthu kuti iwo ayenera kulandira Mzimu Woyera. Ndipo mdierekezi anali atabweramo panali anthupo, kumati, “Musati mumvetsere; khalani duu.”

Mlongo wanga anati, “Bill, ine ndinali wokondwa kwambiri pamene iwe unali kulalikira; ndinamverera ngati ine ndiimirire ndi kulumphakudutsa khoma.”

Ine ndinati, “Dzuka ndipo zilumphak.” Ndizo basi.

Ndipo iye anati, “Koma pamene iwe unayamba kuchita izo,” ndipo anati, “anthu anayamba kufuula,” nati, “ndiye ine ndinangomverera ngati kuti ine ndinali chakale chopanda ntchito.”

<sup>127</sup> Ine ndinati, “Ameneyo ndi mdierekezi. Ameneyo ndi Satana. Pamene iye anabwera umo kudzachita izo,” ine ndinati, “iwe ukanati ungoima basibe.” Ife ndife ansembe kwa Mulungu, tikupanga nsembe zauzimu—kupereka nsembe, zipatso za milomo yathu popereka matamando kwa Dzina Lake. Mwaona?

<sup>128</sup> Tsopano, tsopano, izi ndi zomwe zinachitika. Ndiye Mzimu Woyera unafalikira, chifukwa uko kunangokhala . . . “Wodala ali iye amene akhulupirira.” Mausiku awiri, atatu molunjika ine ndinayesera kuyala izo mmenemo; ndiyeno, Mzimu Woyera unayankhula ndipo unati (pansi pa kudzoza)—unati, “Wodala ali iye amene adza mu Dzina la Ambuye.” Ndipo ine ndisananene chirichonse, ine ndinali nditazinena kale mobwereza. “Wodala ali iye amene akhulupirira kuti Ambuye abwera muno.” Inu mukuona? Ndipo ine ndangokhala ndikuyankhula izi, Mzimu Woyera ndi Mulungu Mwiniwake mkati mwanu. Mwaona? Ndipo iwo anazigwira izo. Mwaona? Ndiyeno Mzimu Woyera unagwera pakati pa anthu. Mukuona momwe Iwo—Iwo umalimbikitsira, ulosi?

<sup>129</sup> Tsopano, pali kusiyana pakati pa ulosi ndi mneneri. Ulosi umapita kuchokera kwa mmodzi kupita kwa wina, koma mneneri amabadwa kuchokera mchikuta ali mneneri. Iwo amakhala ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! Palibe kuwaweruza iwo. Inu simukuwawona iwo pamaso pa Yesaya, kapena Yeremiya, aliyense wa aneneri awo, chifukwa iwo anali ndi PAKUTI ATERO AMBUYE! Koma mzimu wa ulosi pakati pa anthu; iwe umayenera kuti uwupenyese iwo, chifukwa Satana akhoza kuzembera mmenemo. Mwaona? Tsopano. Koma izo ziyenera kumaweruzidwa.

<sup>130</sup> Tsopano, ndife—ife tikuti tikhale ndi chitsitsimutso. Tsopano, penyani izi mwacheru kwambiri kwenikweni tsopano, inu atumiki. Ife tikukonzekera chitsitsimutso. Chabwino. Kapena mwina ife tangokhala ndi msonkhano wachizolowezi wa mpingo. Mpingo wayaka moto. Iwo umayenera uzikhala uli nthawizonse. Chabwino, mwinamwake ife tiri nawo anthu faifi

kapena sikisi omwe ali anthu amphatso; mmodzi amayankhula ndi malirime, awiri kapena mwina atatu amayankhula ndi malirime, anai kapena asanu ndi malirime, ali ndi mphatso ya malirime, amayankhula mu malirime osadziwika. Awiri kapena atatu a iwo amakhoza kutanthauzira. Mwina alipo mmodzi—awiri, kapena atatu a iwo omwe ali nayo mphatso ya nzeru. Chabwino. Iwo onse amakomana, anthu amphatso amenewo. . . Inu. . . Mphatso zimenezo zaperekedwa kwa inu osati kuti muzisewera nazo, osati kuti muziti, “Ulemerero kwa Mulungu, ine ndimayankhula mu malirime! Aleluya!” Muli—muli—muli kudzitsitsa nokha. Izo zinaperekedwa kwa inu kuti muzigwira nazo ntchito. Ndipo gawo lanu mu mpingo lizibwera msonkhano waukulu usanayambe, chifukwa osaphunzitsidwa azikhala ali pakati pathu.

<sup>131</sup> Ndiye inu muzipita mu chipinda, ndipo inu muzikakhala mmenemo, anthu inu palimodzi, chifukwa ndinu ogwirantchito limodzi mu Uthenga. Ndiye inu muzikhala mmenemo. “Ambuye, kodi chiripo chirichonse chimene Inu mukufuna kuti ife tichidziwe usikuuno? Yankhulani kwa ife, o, Atate akumwamba,” mukupereka pemphero, mapembedzero; kuimba nyimbo. Molunjika pansu uzibwera Mzimu, nugwera pa winawake, nayankhula mu malirime. Wina naimirirapo nati, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Ndi chiani icho? Mvetserani. “Pitani mukamuuze M’bale Jones kuti asamuke ku malo kumene iye akukhalako, pakuti mawa madzulo kudzakhala mkuntho uti udzasese ku dziko limenelo; ndipo iwo udzaitenga nyumba yake. Atenge katundu wake ndipo achokeko!”

<sup>132</sup> Tsopano, izo—izo zikumveka bwino. Koma dikirani miniti. Payenera kukhala pali amuna atatu pamenepo omwe ali ndi Mzimu wa kuzindikira. Mmodzi wa iwo akati, “Izo zinali za Ambuye.” Mmodzi wina nkuti, “Izo zinali za Ambuye.” Awo ndi awiri motsutsana ndi atatu—mboni ziwiri kapena zitatu. Chabwino. Iwo azilembe izo pa chidutswa cha pepala. Ndizo zimene Mzimu wanena. Chabwino. Iwo abwerere pa kupemphera, nkumamuthokoza Ambuye.

<sup>133</sup> Pakapita kanthawi, “PAKUTI ATERO AMBUYE (mlosi aimirira)—PAKUTI ATERO AMBUYE, usikuuno, kuchokera ku Mzinda waku New York akhala ali mkazi; iye ali pa machila; iye abwera mu nyumbayi ali pa machila. Iye wamanga mpango wobiliwira kuzungulira mutu wake. Iye akufa ndi khansara. Chimene chinamupangitsa iye kuti akhale motere, Ambuye akumutsutsa iye—nthawi ina iye anaba ndalama kuchokera ku Mpingo Wake pamene iye anali wa usinkhu wa zaka sikisitini. Kamuuzeni M’bale Branham kuti amuuze iye zinthu zimenezi. PAKUTI ATERO AMBUYE, ngati iye akazikonza izo, iye achiritsidwa.” Dikirani miniti. Izo zikumveka bwino kwambiri, koma dikirani miniti. Inu mulemba dzina lanu pa pepala ili, wozindikira? Kodi inu mulemba dzina lanu?

<sup>134</sup> “Izo zinali za Ambuye.” Wina nati, “Izo zinali za Ambuye.” Ndiye—ndiye inu muzilembe zimenezo, “PAKUTI ATERO AMBUYE, usikuuno pakhala mkazi yemwe ati abwere muno, chinthu *chakuti*, *chakuti*.” Iye amene ali ndi mzimu wakuzindikira, awiri kapena atatu a iwo alembepo dzina lawo kwa izo. Mauthenga onse awa aperekedwa. Chabwino.

<sup>135</sup> Ndiye pakapita kanthawi iwo ayamba kumva belu likulira. Mpingo wayamba kusonkhana. Ndiye iwo abweretsa mauthenga awa, kuwaika iwo pomwepa pa desiki. Pano pomwe ndi pamene izo zimayenera kuti zizikhala zitaikidwa. Ine ndiri kwinakwake ndikuyenera, kupemphera. Pakapita kanthawi ine ndizitulukako nyimbo zitatha kuimbidwa. Mpingo wonse uli mu dongosolo, anthu akubwera, akukhala, akusinkhasinkha, akupemphera; ndicho chimene inu mukuyenera kuti muzichita. Osati kubwera ku tchalitchi ndi kumayankhulana wina ndi mzake, muzibwera ku tchalitchi kuti mudzayankhulane ndi Mulungu. Muzikakhala ndi chiyanjano chanu kunja uko. Mwaona? Ife tikuchita chiyanjano ndi Mulungu tsopano. Ndiwo ife timabwera kuno kumayankhula, chirichonse mwakachetechete, molemekeza, Mzimu ukuyendayenda. Wa limba kubwera ku limba pafupi maminiti faifi utumiki wa nyimbo usanayambe, kuyamba mokoma kwenikweni:

Pa mtanda Mpulumutsi anafa,  
Ponditsuka tchimo ndinalira, . . .

Kapena nyimbo ina yabwino yokoma, mwakachetechete kwenikweni. Izo zimabweretsa Kukhalapo kwa Mzimu Woyera mu msonkhano. Mwaona? Chabwino.

<sup>136</sup> Anthu atakhala mmenemo. Ena a iwo ali kwenikweni—akuyamba kulira ndi kumabwera ku guwa, nkumalapa msonkhano usanayambe nkomwe. Mzimu Woyera uli pamenepo. Mwaona? Mpingo uli mu kusautsika. Akhristu akupemphera; iwo ali pa malo awo. Iwo sikuti angokhala apo akutafuna chingamu, kumati, “Hei, Liddie, tandipatsa ine zopaka mmilomo zakozo; ine ndikufuna. . .Iwe ukudziwa. Iwe ukudziwa. Ine ndikusowa. . .Iwe ukudziwa, tsiku lina pamene ine ndinali kumusi uko ndikugula, ine ndikukuuza iwe, ine ndinali pafupi kuti ndikuponde pa zala zako. Kodi ine ndinayamba ndaziwonapo zoterozo. . .Kodi iwe ukuganiza chiani za izo?” O, chifundo! Ndiye nkuitcha iyo nyumba ya Mulungu. Bwanji, ndi zopanda ulemu. Thupi la Khristu kubwera palimodzi. Apo ife tinakhala.

Bambo atakhala chapafupi, “Ndikuti, inu mukudziwa pamene ife tinapita uko, izi *zakuti-n-zakuti* ndi *zakuti-n-zakuti-n-zakuti*. . .” Izo ndi zabwino muli kunjja, koma mkati muno ndi mnyumba ya Mulungu.

<sup>137</sup> Muzibwera muno mwakupemphera; muzitenga malo anu. Ine ndikukamba tsopano, osati kwa mipingo yanuyo, abale.

Ine sindikudziwa zomwe inu mumachita; ine ndikukamba kwa kachisi uyu. Ine ndikuyankhula kwa khomo langa lakuseri lomwe. Mwaona? Ndiko kulondola.

<sup>138</sup> Tsopano, pamene inu mubwera muno monga choncho, ndiye chinthu choyamba inu mukudziwa, m’busa amatuluka umo. Iye ali mwatsopano. Iye samasowa kuti azidzayankha *izi, izo*, ndi *zinazo*. Iye akubwera kumene kuchokera mu—mame a utumiki wake. Iye wakhala ali pansu pa mphamvu ya Mzimu Woyera. Iye akudzalowa kumene komwe malirime ochuluka a moto asonkhana palimodzi. Ali pafupi lawi tsopano (mwaona?), ili likuyendayenda apo. Iye akutulukira kuno, nadzatenga *izi*. “Uthenga wochokera kwa mpingo: ‘PAKUTI ATERO AMBUYE, M’bale Jones asamuke ku nyumba yake. Mawa madzulo pa 2 koloko mkuntho udzasesa dziko laolo. Atenge zinthu zake ndipo achokeko.’” M’bale Jones akuzimwa zimenezo. Chabwino. Izo zasungidwa. “PAKUTI ATERO AMBUYE, kukhala kuli mkazi dzina lake *Wakuti-n-wakuti* ati abwere muno usikuuno, ndipo izo zinali—iye wachita *zakuti-n-zakuti*.” (Momwe ine ndanenera kumene, onani, monga choncho.) Chabwino, izo ziri pamenepa. Ndi zimenezo. Iwo ali nao kale malo awo tsopano mu mpingo. Chabwino.

<sup>139</sup> Ndiye iye akuutenga uthengawo. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iye akuyamba kulalikira. Palibe kanthu kosokoneza; izo zachitika kale. Tsopano, ife tikupita patsogolo, ife tikulalikira uthenga.

<sup>140</sup> Ndipo patapita kanthawi pamene... Chinthu choyamba inu mukudziwa pamene uthenga watha, mzere wa machiritso ukuyamba. Apa pakubwera mkazi. Winawake anayankhula mu malirime ndipo anati iye abwera. Mwaona? Aliyense wa ife akudziwa chimene chiti chichitike. Aliyense wa ife akuzidziwa izo. Mukuona momwe chikhulupiro chikuyambira kumangika ndi malirime a moto awo ataima pa inu tsopano. Iwo ukuyamba kusonkhanira palimodzi. Bwanji, iyo ndi ntchito yotsirizidwa kale; ndi zomwezo.

Mkazi ameneyo...ine nditi, “Akazi a *Akuti-ndi-akuti*, mwachokera ku Mzinda wa New York, muli muno. . . .” Mwaona?

“O, izo nzolondola. Inu munadziwa bwanji izo?”

“Uwo ndi uthenga wochokera kwa Ambuye kwa mpingo. Pamene inu munali a usinkhu wa zaka sikisitini, kodi inu simunali pa malo *akuti*, *akuti* ndipo munachita—munatenga ndalama zina kuchokera ku mpingo, ndipo munaziba izo, ndipo munapita kwina, ndipo munakagula zovala zatsopano ndi izo?”

“O, uko nkulondola. Uko ndi kulondola.”

“Izo ndi ndendende zomwe Mulungu watiuza ife usikuuno kupyolera mwa M’bale *Wakuti-n-wakuti*, anayankhula ndi malirime; M’bale *Wakuti-n-wakuti* anatanthauzira; M’bale

*Wakuti-n-wakuti* kuno ananena, mwa kuzindikira, anati izo zinali zochokera kwa Ambuye. Ndipo izo nzoona.”

“Inde!”

“Ndiye, PAKUTI ATERO AMBUYE, pitani mukazikonze izo, ndipo muthana nayo khansara yanuyo.”

141 M'bale Jones akupita kwawo, akukatenga ngolo, akubwerera uko, akutenga mipando yake, ndi kuchokako uko. Pa 2 koloko mawa madzulo [M'bale Branham akupanga phokoso kuti afotokozere—Mkonzi.] chikuchokapo chinthu chonsecho. Mwaona? Ndiye mpingo ukulemekeza . . . “Zikomo inu, Ambuye Yesu, chifukwa cha ubwino Wanu.” Tsopano, izo ndi zomwe ziri, kumangiriza, kwa mpingo.

142 Tsopano, nanga bwanji ngati izo sizichitika iwo atanena kale izo. Ndiye inu muli ndi mzimu woipa pakati panu. Inu simukuchifuna chinthu choipa icho. Iwe ungafunirenji chinachake choipa pamene—miyamba yadzaza ndi zenizeni za Chipentekoste? Musati muzitenga choloweza mmalo chakale chochokera kwa mdierekezi. Pezani chinachake chenicheni. Mulungu ali nazo izo kwa inu. Ndiye inu musati muzikhala ndi misonkhano inanso, ndi kuika chirichonse pamenepa, mpaka Mulungu atatsimikizira kale kuti inu mukulondola, chifukwa ndinu wotheadizira kwa mpingo mu ntchito ya Uthenga. Tsopano, inu mukumvetsa zomwe izo ziri?

143 Ndipo malirime, malirime osadziwika . . . Palibe munthu iye—amadziwa chimene iye akuchikamba. Iye amayankhula; koma phokoso lililonse liri ndi tanthauzo. Izo ziri ndi tanthauzo [M'bale Branham akuwomba manja ake—Mkonzi.] “Guluku, guluku, guluku!” izo ziri—ndi—ndi chinenero kwinakwake.

144 Pamene ine ndinali mu Afrika, ine sindinali kukhulupirira konse izo, koma chirichonse chimene chinkapanga phokoso chinali ndi mtundu wina wa tanthauzo kwa icho. Baibulo linati palibe phokoso lopanda kufunikira, lopanda tanthauzo. Phokoso lililonse limene limapangidwa limakhala ndi tanthauzo lina kwa chinachake. Mwakuti, ine ndimawamva anthu akuti . . . ine ndikuti, “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.”

145 Mmodzi wa iwo amati [M'bale Branham akupanga phokoso la wotanthauzira wachi Afrika—Mkonzi.]. Wina amati [M'bale Branham akufotokozerananso—Mkonzi.]. Ndipo zimenezo zinali, “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.” Mwaona? Izo zinali . . . Ndipo izo nkusamatanthauza kanthu kwa ine, koma kwa iwo icho chinali chinenero chimodzimidzi basi monga ine ndikuyankhulira kwa inu. Pamene wotanthauzira wa chi Zulu, chi Xhosa, chi Basuto, ndi chirichonse, chomwe chimadza motsatira, chirichonse chimene chinali kunenedwa, aliyense ankachimva. Ndipo zinthu izi zimene inu mumawamva anthu awa akungoyankhula, ndi kumaganiza kuti ndi zochuluka za



kubwebweta, uko sikuli; izo ziri nalo tanthauzo. Chotero ife tiyenera kuti tizizilemekeza izo, tiziziyika izo mu malo ake.

<sup>146</sup> Tsopano, mwina pakhala palibe uthenga. Tsopano, msonkhano watha; kuitanira pa guwa kuli kupangidwa. Ndipo pakapita kanthawi winawake (pakhala palibe uthenga kumbuyo uko)—winawake akuimirira mwamsanga pamene iwo apeza mwayi wotero. Mzimu Woyera...Tsopano, Baibulo linati, “Ngati palibe wotanthauzira, msiyeni iye akhale bata.” Ziribe kanthu kuti akuvutika bwanji kuyesera kuti ayankhule, khala bata.

<sup>147</sup> Ukati, “Ine sindingakhoze kuchita izo.” Baibulo linati iwe ukhoza. Mwaona? Chotero kuti—izo ndi zokhazikika. Mukuona? Msiyeni iye akhale bata.

<sup>148</sup> Ndiye, pamene iwo, mwayi ukabwera pamene chirichonse chiri mu dongosolo, ndiye ngati Mzimu Woyera ulumphira pa iye kuti apereke uthenga, ndiye upereke iwo. Ndizo ndendende zomwe inu muyenera kumazichita. Ndiye kutanthauzira kumabwera, nkuti, “Muli mkazi mkati muno dzina lake ndi Sally Jones (ine ndikuyembekeza mkazi sali muno amene ali ndi dzina limenelo, koma...)—Sally Jones. (Mwaona?) Mumuuze iye kuti uno ndi usiku wotsiriza wa kuitanidwa kwake. Akonze zinthu ndi Mulungu chifukwa iye ali ndi nthawi yaifupi kuti akhale kuno.” Tsopano, Sally Jones angathamangire ku guwa mwamsanga basi monga iye angakhoze kukafikira uko (mwaona?), chifukwa uko ndi kuitanidwa kwake kotsiriza. Mukuona? Ndiko kupereka uthenga, kapena kutsimikizira, kapena chinachake.

<sup>149</sup> Uwo ndi mpingo wa Chipentekoste ukugwira ntchito. Palibe mwayi woti mizimu yoipa ilowereremo, chifukwa uli kale...Baibulo likupereka mwandendende, “Mulole izo zikhale motsatizana, ndipo izo mwa atatu; ndipo muzilola awiri kapena ochulukirapo aweruze.” Umenewo ndiwo mpingo. Koma kodi ife tafika nazo pati izo lero? Kudumphira mmwamba, kupitiriza, kuseka ndi kumapitirira pamene wina akuyankhula mu malirime; wina kumayang’ana, kumayankhula za chinachakenso ndi kumachulukana chozungulirapo; m’busa kumachita chinachake; kapena ena kumachulukana chozungulirapo. Komatu, izo sizabwino. Mwina m’busa akulalikira, ndipo winawake nkuimirira ndi kumamusokoneza iye mu...Mwina kumawerenga Baibulo ndipo winawake... Kumawerenga Baibulo, ndipo wina kumbuyo uko akuyankhula mmalirime. O, ayi! Mukuona? Mlaliki ataima akulalikira mu guwa, winawake nkuima ndi kumamusokoneza iye, poyankhula mu malirime. Izo zonse nzabwino. Ine sindikuti uwo si Mzimu Woyera, koma inu mukuyenera kuti muzidziwa momwe muziugwiritsira ntchito Mzimu Woyera (mukuona?), kuwugwiritsa ntchito Iwo.

Tsopano, ine—ine ndikuyankhula...Kodi inu muli nawo malo a limodzi lina? Ndiye, mawa ndi Lamlungu. Ndiye, ife tidza...Tiyeni tingo...Pano pali limodzi. Ine ndikuganiza ndilo lachisomo kwambiri. Ndipo tsopano, ngati inu nonse mutangopirira nane maminiti pang'ono okha motalikitsa, chonde. Ndiyeno, ndidza...ine ndikufuna inu—ine ndikufuna inu kuti muchimvetse ichi. Ine ndinalisunga ili mwacholinga. Ili ndi limodzi langa lotsiriza.

Tsopano, poyamba, ine ndikuti ndiwerenge zinthu ziwiri zimene munthuyo wazifunsa. Izo ziri pa chidutswa chakale cha pepala, cholembedwa ndi malembedwe okongola. Ndiribe lingaliro la yemwe ali, palibe dzina lalembedwa kwa—kwa lirilonse la iwo.

**98. M'bale Branham, kodi ndi kulondola kuti atumiki azipanga zikoka zazitali pa ndalama mu misonkhano yawo, kumanena kuti Mulungu wawauza iwo kuti ochuluka mwakuti mwa omvetsera akuyenera kupereka mochuluka chotere? Ngati uku kuli kulondola, ine ndikufuna kuti ndidziwe. Kapena ngati ziri zolakwika, ine ndikufuna kuti ndidziwe. Izi zandisokoneza ine moyipa.**

<sup>150</sup> Tsopano, inu mukuona, mzanga, ine ndikuti ndikuuzeni inu, ine ndikuti ndikuuzeni inu chimene ine ndikuganiza. Mukuona? Tsopano, izo sizikutanthauza kuti nzolondola. Ine ndikuganiza ndi zoipa.

<sup>151</sup> Tsopano, ine ndikuganiza izi. Mulungu ananditumiza ine ku ntchitoyi. Ine ndawonapo nthawi yomwe ine ndinkawoneka ngati ine ndikanati ndikhale mwinabe...Ndipo ine—ine ndimakhala ndilibe ndalama konse. Ndipo ine ndimati, “Ingodusitsani mbale ya chopereka.”

Ndipo amanejala amakhoza kubwera ndi kuti, “Taona, Billy, tiri madola zikwi zisanu mu ngongole usikuuno, Mnyamata. Kodi iwe uli nazo ndalama ku Jeffersonville zoti ukailipire iyo?”

<sup>152</sup> Ine nkuti, “Zonse ziri bwino. Mulungu ananditumiza ine kuno, kapena ine sindikanati ndibwere. (Mukuona?) Ingodusitsani mbale ya chopereka.”

Ndipo msonkhano usanathe, wina nkuti, “Inu mukudziwa, Ambuye anachiyika pa mtima wanga kuti ndipereke madola zikwi zisanu ku izi.” Onani, mwaona? Choyamba, khalani otsogozedwa pakuchita izo.

<sup>153</sup> Ine sindimakhulupirira kukokera, ndi kupempha, ndi kupemphetsa ndalama. Ine ndikuganiza ndi chinthu cholakwika. Tsopano, m'bale, ngati inu mumachita izo, musati mundilole ine ndipweteketse kumverera kwanu. Mukuona? Inu—inu mukhoza kukhala nacho chilolezo kuchokera kwa Mulungu chochitira izo. Koma ine ndikuyankhula za mwiniwanga zokha. Ine sindimakhulupirira mu zimenezo.

<sup>154</sup> Tsopano, ine ndadziwapo ngakhale za azitumiki amapita ndi kumati... Ine ndinaima pomwepo, osati kale litali... Tsopano, awa si Achipentekoste, awa ndi... Chabwino, ndi mipingo (mukuona?), mipingo ina. Izo zinali ku msonkhano waukulu wa msasa. Gertie, iwe unali nane, ambiri ena alipo. Ndipo iwo anatenga madzulo onse ku chipembedzo chotchuka—awiri kapena atatu a iwo palimodzi (ndizo zachizolowezi—mipingo yachizolowezi, monga mipingo yathu yamakono kuno mu mzinda, ndi zina zotero) ku msonkhano waukulu—ndipo iwo anatenga madzulo onse, kuima pa nsanja ndi kumawopyeza kuti—kuti Mulungu akanati awononge mbewu zawo, akanati awapatse ana awo kupuwala, ndi zinthu monga choncho, ngati iwo akanati asapereke kwa msonkhano umenewo. Ndizo ndendende zoonza, ndiri ndi Baibulo ili patsogolo panga. Ine ndinati, “Uko ndi kuchitira mwano kwa Mulungu ndi kwa omutsatira Ake.” Ngati Mulungu akutumani inu, Iye akusamalirani inu. Ngati Iye sanakutumeni inu, ndiye mulole chipembedzo chizikusamalirani inu apono. Koma—koma inu... Ngati Mulungu akutumani inu, Iye akusamalirani inu.

### **99. Nanga bwanji za sewero la Khristimasi mu mpingo wa Mzimu Woyera?**

<sup>155</sup> Chabwino, ngati ziri zokhudza Khristu, izo zikhoza kukhala zabwino. Koma ngati ziri zokhudza Santa Claus, ine sindimakhulupirira mwa iye. I—ine ndakula kale—ine ndakula nkuchoka kale kwa izo. Ine sindimakhulupirira mwa Santa Claus konse. Mukuona? Ndipo tinthu tina tating’ono ta Khristimasi tomwe iwo ali nato, ine ndikuganiza ndi zopusa. Ndipo... Koma ine ndikuganiza iwo amuchotisa Khristu yense mu Khristimasi ndi kuikamo Santa Claus mmenemo.

<sup>156</sup> Ndipo Santa Claus ndi nthano yopeka. (Ine sindikupweteketsa kumverera kwanu kulikonse, ine ndikuyembekeza, pokhudza ana.) Koma ine ndikuuzani inu. Kuno osati kale litali, pafupi zaka twente-faifi, sate zapitazo, pamene mtumiki kuno mu mzinda uwu, m’busa wa—wa mpingo winawake waukulu mu mzindawu, yemwe ine ndinkamudziwa bwinobwino, mzanga wa pachifuwa wa ine, iye anadza kwa ine. Ndipo Charlie Bohannon (M’bale Mike, inu mukumukumbukira Charlie Bohannon, mzanga wabwino kwa ine)... Anakhala pamene mu ofesi yake ndipo anati, “ine sindidzawauza konse ana anga kapena zidzukululu zanga kuwauza bodza limenelo kenanso.” Iye anati, “Mnyamata wanga yemwe wamng’ono anadza kwa ine iye atafika kale pafupi usinkhu wa zaka thwelofu, ndi kumayankhula za Santa Claus...” Ndipo iye anati, “Bwanji... Wokonedwa, ine ndiri ndi chinachake choti ndikuuzani inu,” Anati, “Amayi...” Inu mukudziwa, ndipo anapitirira kumamuza iye zomwe iye anzichita.

Ndiye iye atabwerera, anati, “Ndiye, Adadi, kodi Yesu uyu ali chinthu chomwecho?”

157 Muzinena zooni. Santa Claus ndi zobweretsedwa ndi Katolika za munthu, Kriss Kringle kapena Nicholas Woyera, woyera wa Chikatolika wa chi German wokalamba wa zaka zambiri zapitazo yemwe ankapita paliponse kumachita zabwino kwa ana. Ndipo iwo achipitiriza icho ngati mwambo. Koma Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu. Iye ndi weniweni, ndipo Iye alimoyo.

Tsopano, apa pali funso, limodzi lotsiriza, lomwe liri kwambiri. . .

158 Tsopano taonani. Inu mukhoza kusagwirizana nane pa izo. Koma ngati inu simugwirizana nane, kumbukirani, mulole izo zikhale zachibwanawe, mutero inu? Ine ndimakukondani inu, ndipo ine sindikufuna kuti—sindikufuna kuti ndikupweteketseni inu. Ine ndangokhala, Ine ndikufuna kuti ndikhale woonamtima. Ngati ine sindingathe. . . ngati ine ndimuza mnyamata wanga bodza, ndiye ndine wabodza. Mukuona? Ine ndikufuna ndizimuza iye zooni.

159 Tsopano, ine ndikamuza iye za Santa Claus, ine nkuti, “Eya, zedi, alipo Santa Claus. Mudzawaone Adadi pa usiku wa Khrisimasi.” Mukuona? Eya.

160 Inu mukudziwa, tsiku lina ine ndinali kumusi uko, ndipo ine ndinayesera izo pa msungwana wamng’ono kuti ndingoona. Ine ndithudi ndinalipidwa mobwezeredwa dzana ilo. Ine ndinali mu nyumba. Ndipo iwo anali ataima apo, kumusi kuno ku Quaker Maid. Ndipo ine ndinapita uko kuti ndikagule zinthu. Ndipo chotero ife, mkazanga ndi ine, tinali mmenemo. Ndipo uko kunali msungwana wamng’ono kwambiri, sanali wopitirira pafupi usinkhu wa miyezi eyitini, ndipo iye ataima apo, akupita, akuimba, “Dingle Bells, Dingle Bells. . .” Ndipo ine ndinati. . . Mu maimidwe ake aang’ono, inu mukudziwa, atakhala mmbuyo mwa ngolo yaing’ono.

Ine ndinati, “Kodi iwe ukuyembekezera Santa Claus?”

Iye anati, “Ameneyo ndi adadi anga, Bambo.”

Ine ndinati, “Adalitse mtima wako waung’ono, Wokonedwa. Iwe uli ndi nzeru.”

Tsopano, pano pali kokanirira kenikeni, abwenzi. Ndipo mwa ichi. . . Ndiye ine nditseka. O, ndi—ndi Lemba lokoma, koma ndi lobaya kwa munthu aliyense yemwe wowoneka ngati ali. Ndipo ilo landikanirira ine kwa zaka ndi zaka; ndipo kokha mwa chisomo cha Mulungu chokha. . . Ndipo mkazi wanga wofunika, wakhala kumbuyo komwe uko tsopano, pamene iye anamva kuti ine ndinali nalo funso limenelo madzulo ano, iye anati, “Bill, iwe ukaliyankha chotani ilo?” Iye anati, “Ine nthawizonse ndakhala ndikulidabwa ilo mwiniwanga.” Anati, “Ine sindimakhoza kulimvetsa ilo konse.” Ndipo anati. . .

Ine ndinati, “Ubwere uko usikuuno, Wamtimawokoma. Ine ndikachita mwakukhoza kwanga pakuthandizidwa ndi Mulungu.”

**100. M'bale Branham, chonde tafotokozani Ahebri 6:4 mpaka 6.**

<sup>161</sup> Iyo ndi nthawi imodzi yomwe kwenikweni. . . Mwaona, tsopano inu musowa kuti muyang'ane kuno pa chikhulupiriro chathu, chisomo, chitetezero cha okhulupirira, kupirira kwa oyera, chipiriro, kani, cha oyera. Ahebri mutu wa 6, 4 mpaka 6.

Tsopano, mwamsanga pamene izi. . . tikatsiriza izi, ndiye ine ndikuyembekeza kuti Mulungu andithandiza ine kuzipangitsa izo kumveka bwino bwino kwa inu. Ine ndikupepesa, i—ine ndiri ndi Uthenga wanga wa usikuuno; mwina ine ndilalikira chinthu chomwecho mmawawu pa—pa utumiki. Ndiye ine ndikhala ndikupita.

<sup>162</sup> Tsopano, ili ndi lokanirira kwenikweni. Mukuona? Tsopano, inu muyenera kusamalitsa. Tsopano kumbukirani, ife timakhulupirira ndi kuphunzitsa pa mpingo uno, kuti si chirichonse chimabwera kuno ndi kumafuula, chirichonse chimene chimayankhula mu malirime, chirichonse chimene chimagwirana chanza ndi mlaliki, chiri nawo Moyo Wamuyaya. Koma ife timakhulupirira ngati iwe uli nawo Moyo Wamuyaya, ngati Mulungu wakupatsani inu Moyo Wamuyaya, inu muli nawo Iwo kwanthawizonse. Mukuona? Chifukwa onani. Ngati ukanati usakhale, Yesu apezeka ali mphunzitsi wabodza. Mu Yohane Woyera 5:24, Iye anati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine ali nawo Moyo Wosatha, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wachoka ku imfa wapita ku Moyo.” Tsopano, tsutsanani naye Iye. “Onse amene Atate wandipatsa Ine. . . Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate atamukoka iye. (Ine ndikubwereza Lemba.) Onse amene adza. . . Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse omwe Atate Anga wandipatsa Ine adzabwera kwa Ine. (Mukuona?) Ndipo onse omwe abwera kwa Ine, Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wosatha (Yohane Woyera 6), ndipo ndidzamuukitsa iye pa masiku otsiriza.” Awo ndiwo mawu Ake.

<sup>163</sup> Tsopano onani. Ngati ine ndikanakhoza kubwerera ku Aefeso mutu wa 1, Paulo akulalikira. . . Tsopano, Akorinto, wina aliyense anali ndi lirime ndi salmo. Inu mumazindikira mipingo ina inalibe vuto limenelo. Iye sananene kanthu za iyo. Kodi iye anayamba watchulapo konse malirime paliponse mu mpingo wa Aefeso, mpingo wa Roma? Ayi! Iwo anali nawo malirime ndi chirichonse basi monga Akorinto analiri, koma iwo anali ataziyika izo mu dongosolo. Akorinto sankakhoza basi kuziyika izo mu dongosolo. Mukuona? Koma Paulo anapita uko ndipo anakawuyika mpingowo mu dongosolo.

Tsopano, iye. . . Ine ndikukhulupirira, monga Oral Roberts amanenera, “Mulungu ndi Mulungu wabwino.” Kodi inu simukukhulupirira zimenezo?

164 Ndipo inu mukuti, “Chabwino, nanga bwanji Achipentekoste ndi malirimewo ndiye, M’bale Branham?” Ine ndikuganiza iwo ali nawo Mzimu Woyera. Ndithudi iwo ali. Chabwino, bwanji? Taonani. Inu mukukhulupirira kuti Iye ndi Mulungu wabwino? Tomasi anati nthawi ina, “Inu mukudziwa, Ambuye. . .”

Ena onse a iwo ankamukhulupirira Iye. Ankati, “O, ife tikudziwa Iye ndi weniweni!”

“O,” Tomasi anati, “ayi, ayi, ine sindikuzikhulupirira izo. Njira yokha yomwe ine nditi ndikhulupirire izo, ine ndiyenera kuti ndikhale nawo umboni wina. Ine ndisowa kuti ndilowetse zala zanga mu mbali Mwake ndi mu zipsyera za misomali mu manja Ake.”

Iye ndi Mulungu wabwino. Iye anati, “Bwera, Tomasi. Nazi apa.”

“O,” Tomasi anati, “tsopano ine ndikukhulupirira.”

165 Iye anati, “Inde, Tomasi, iwe utandiwona Ine kaye, ndipo utandimverera Ine, ndi kuika dzanja Langa. . . manja ako mu mbali Mwanga, iwe ukukhulupirirano. Koma kukula kwake nkotani kuli kwa mphoto yawo amene sanayambe awona ndipo komabe akukhulupirira.” Iye ndi Mulungu wabwino. Iye amakupatsa iwe chokhumba cha mtima wako, ndithudi. Tiyeni tizingomukhulupirira Iye. Ndiko—ndiko—ndiko kumenya kwa kumupha Satana. Pamene munthu amutenga Mulungu pa Mawu Ake, m’bale, izo zingamuphe Satana nthawi iliyonse. Ndiko kumenya kolimbitsitsa kumene Satana angakhoze kukulandira, pamene munthu amutenga Mulungu pa Mawu Ake. Inde, bwana Monga ine ndinati, “Munthu sadzakhala moyo (Yesu, usiku wina), koma ndi Mawu onse otuluka kuchokera. . .”

166 Tsopano, zindikirani izi. Tsopano ine ndikuti ndiyambire pa ndime yoyamba:

*Chotero posiya zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro; . . .* (Tsopano, chinthu choyamba chimene ine ndikufuna kuti inu muchidziwe: kodi Paulo akuyankhula ndi ndani apa? Aheberi. Iwo akuti, “Aheberi,” pamwamba, Bukhu la Aheberi. Ndi kulondola uko? Ayuda omwe anali atamukana Yesu. . . Mungakhoze inu—inu mukuzigwira izo tsopano? Iye akuyankhula kwa Ayuda, kumawasonyeza iwo mthunzi wa lamulo kukhala choimira cha Khristu. Zinthu zakale zonse zoimira za zatsopano. Tsopano penyani.)

*...posiya zoyambirira za chiphunzitso cha Khristu, tiyeni ife tipitirire mpaka ku ungwiro; . . .*

167 Tsopano, iye wakhala akuyankhula kwa iwo za ziphunzitso. Tiyeni ife tipite ndi kumayankhula za zinthu zaungwiro. Tsopano, inu mumakhallitsidwa angwiro mwa Mulungu pamene inu mwasindikizidwa ndi Mzimu Woyera mpaka tsiku la chiwombolo chanu. “Iye amene ali wobadwa ndi Mulungu (I Yohane) samachita tchimo; pakuti iye sangakhoze kuchimwa, pakuti Mbewu ya Mulungu ikanali mwa iye.”

168 Munthu yemwe ali wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, osati woganizira kuti iye anadzazidwa, koma iye amene ali wobadwa ndi Mzimu wa Mulungu samachita tchimo, pakuti Mbewu ya Mulungu ili mwa iye, ndipo iye sangakhoze kuchimwa. Mukuona? Kodi Baibulo limanena chomwecho? Chotero ndi izo apo. Inu muli. . . Osati zomwe inu mumachita, zomwe, ndi zomwe, osati zomwe dziko limaganiza za inu, ndi zomwe Mulungu amaganiza za inu. Mwaona, mukuona? Inu simungakhoze. . . Ine ndingakhoze bwanji kukhala ndi chilolezo cholembedwa ndi meya wa mzinda, kuti ine ndikhoza kumathamanga mailosi forte pa ora kudutsa mu mzinda, ndipo mpolisi aliyense nkundimanga ine? Ine sindingakhoze. Ine ndingakhoze kuchimwa bwanji pamene pali nsembe pa magari pamaso pa Mulungu mosalekeza, pamene Iye sangakhoze konse kumandiwona ine, pamene pali chotchinga pa—pa. . . patsogolo pa ine ndi Mulungu, chishango cha Magazi; pakuti ndife akufa, ndipo moyo wathu wabisidwa mwa Khristu kupyolera mwa Mulungu, osindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Ungakhoze bwanji mdziko kuchita chirichonse cholakwika pamaso pa Mulungu. “Ngati ife tichimwa mwadala (Aheberi 10) ife titalandira kale chidziwitso cha Choonadi, sipamakhalanso nsembe kwa tchimolo.” Mkati umu ndi zosatheka (mukuona?) kuti uchimwe mwadala.

169 Tsopano, tiyeni tipitirire nazo ndi kuziwerenga. Chabwino.

*...ungwiro; osati kuikanso maziko a—kulapa ku ntchito zakufa, ndi. . . chikhulupiriro cha kwa Mulungu,*

*Za chiphunzitso cha maubatizo, . . . kuika kwa manja, ndi za chiukitsiro cha akufa, ndi. . . chiweruzo chamuyaya.*

*Ndipo izi. . . ife tizichita, ngati Mulungu alola.*

(Tsopano apa ndi pamene iwo anafuna kuti ayambire, kuchokera pa ndime ya 4.) *Pakuti ndi kosatheka kwa iwo. . . amene anawalitsidwapo, ndipo alawa za mphatso yakumwamba, ndipo anapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera,*

*Ndipo analawa nawo za mawu abwino a Mulungu, ndi mphamvu za dziko likudza ilo,*

*Ngati iwo adzagwa, kuti akakonzedwenso—  
kuwakonzanso iwo kachiwiri kuti alape; powona kuti  
iwo akudzipachikira kwa okha Mwana wa Mulungu  
katsopano, ndi kumuika iye ku manyazi apoyera.*

<sup>170</sup> Tsopano, tsopano, izo zikuwoneka mofanana, kuchokera momwe inu mukuziwerengera izo apo, kuti munthu akhoza kulandira Mzimu Woyera, ndiyeno nkubwerera mmbuyo ndi kutayika. Koma ndi zosatheka kuti iye achite izo. Mukuona? Iye sangakhoze kuchita izo. Ngati iye angatero, Khristu ananama. Mukuona? Ndi zosatheka kwa iwo omwe anawalitsidwapo. Tsopano, penyani apa. Kodi iye akuyankhula kwa ndani? Iye akuyankhula kwa Ayuda ammalire awo. Iye sanati konse munthu ali wodzazidwa ndi Mzimu Woyera; iye anati, “Ngati iye analawa Mawu a Mulungu.”

<sup>171</sup> Tsopano, mungondilora ine ndipereke izo mwa fanizo, kotero kuti inu muwone ndipo musaphonye izo tsopano. Tsopano, iye akulembera kwa Ayuda awa. Ena a iwo ndi okhulupirira a mmalire. Mukuona? Iye anati, “Tsopano, ife tizisiya ntchito izi ndipo tipita tikayankhule za ungwiro.” Anati, “Tsopano, ife tayankhula za maubatizo, ndi kuuka kwa akufa, ndi kusanjika kwa manja, ndi chirichonse; koma tiyeni tipitirire nazo tsopano kuti tikayankhule za ungwiro. Tsopano, ife tikuti tiyankhule za pamene inu mubwera mu Mzimu Woyera. Tsopano, inu mwakhala mukutsalira pa msonkhano kwa nthawi yaitali. . .”

<sup>172</sup> Ndipo inu mwawawona anthu amenewo. Iwo amatsalira: iwo sangalowe mkati kapena kuchokapo. Iwo amauyamikira Mzimu Woyera. Iwo amabwera pafupi. Ndipo mwina mwake Mzimu Woyera umachita chinachake ndi, amuna, iwo amaimirira ndi kumafuula, ndi kumalumpha chokwera-ndi-chotsika pansi chifukwa cha izo, koma iwo safuna konse kuti awulandire Iwo iwoeni. Ayi, ayi! Mukuona? Ndipo iwo amati, “O, inde, izo nzabwino. O, ine sindikudziwa za izo tsopano.” Mwaona, mwaona, mukuona? Okhulupirira ammalire. Pafupi kumene mpaka iwo akhoza kulawa Iwo, komabe iwo samaulandira Iwo. Mukuona? Tsopano, iwo amatsalira pozungulira monga choncho motalika kwambiri mpaka pakapita kanthawi iwo amachokako kwathunthu. Ine ndikhoza kuchula maina a ochuluka omwe anali ku kachisiyu, anachita chinthu chomwecho. Kugwa njira yonse kachiwiri, kuti adzikonze okha mwatsopano mwa kulapa, palibepo kulapa kwa iwo. Iwo anangowukwiyitsa Mzimu kuti utalikire kwa iwo. Iwo akhala ali pafupi kwambiri mpaka. . .

<sup>173</sup> Apa, ngati inu mungatembenuze ndi ine (inu mulibe nthawi, ine ndikudziwa, tsopano) koma ngati inu mungatembenuze ku Detoronome mutu wa 1 ndi kuwerenga izo, inu mupeza chinthu chomwecho. Muzilembe izo apo tsopano, Detoronome mutu wa 1. Tsopano, ndipo muyambire pa ndime ya 19 ndi kuwerenga mpaka pa 26. Detoronome. . . Inu mupezapo. . . Tsopano onani. Israeli yense. . . Zomwe anthu amenewo amachita, iwo amafika



ku Kadeshi-barnea. O, ine ndikuwona chinachake! Kachisi uyu, dziko la Chipentekoste lino liri pa Kadeshi-barnea pakali pano. Ndiko kulondola ndendende, M'bale Neville. Ife tiri pa Kadeshi-barnea, mpando wa chiweruzo cha mdziko (unali mpando wachiweruzo).

<sup>174</sup> Ndipo azondi anapita uko. Yoswa ananena apa, “Tsopano, ine ndinatumba azondi,” kapena Mose, kani, “ine ndinatumba azondi, thwelofu, mmodzi wa, munthu mmodzi kuchokera mwa lirilonse la mafuko anu. Ine ndinawatumiza iwo kuti akalizonde dzikolo ndi kubweretsanso uthenga.” Ndi kulondola uko?

Ndipo pamene iwo anabwererako, uko kunali naini kuchokera pa thwelofu anati, “O, ilo ndi dziko labwino, koma o, chifundo, ife sitingakhoze kulitenga ilo. O, mai! Aamori ali kumeneke, ndipo ife tikuwoneka ngati ziwala pambali pa iwo. Iwo ndi amuna okhala ndi zida. Makoma awo ndi aakulu. O, ndizo. . . bwanji, ine ndikukhumba ife tikanafera kuja mu Igupto mmalo moti inu mutibweretse ife kuno.”

<sup>175</sup> Bwanji, ka Kalebu kachikulire ndi Yoswa analumpha pamenepo ndipo anawatontholetsa iwo; anati, “Ndife okhoza moposa kuti tilitenge ilo.” Inde, bwana! Ndi ameneyo apo. Tsopano taonani. Ndi chiani chinachitika? Kalebu ndi Yoswa ankadziwa kuti Mulungu anapereka lonjezo la ilo: “Ine sindikusamala kaya ndi lalikulu bwanji ilo, kaya zotchingazo ndi zochulukira bwanji, kaya ndi zazitali bwanji, kaya ndi zazikulu bwanji, izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Mulungu ananena chomwecho, ndipo ife tikhoza kulitenga ilo.” Ndipo kodi inu mukudziwa kuti iwo anali anthu awiri okha, kuchokera mu mamilioni awiri ndi theka, omwe anawoloka konse kupita mu dzikolo? Chifukwa iwo anagwiritsa chikhulupiriro chawo mu zomwe Mulungu anati kuti ndi Choonadi. Amen!

<sup>176</sup> Kachisi, pakali pano, waima pa Kadeshi-barnea. Taonani, anthu amenewo anali pafupi kwambiri mpaka iwo analawa kumene mphesa zochokera mdzikolo. Iwo anadya mphesazo. Pamene Kalebu ndi iwo anapita uko ndipo anakabweretsako mphesa, anyamata amenewo anakathyolako zina ndi kumadya izo. “O, izo ndi zabwino, koma ife sitingakhoze kuzichita izo.” “Iwo amene analawa ntchito yabwino ya Mulungu, analawapo za Mzimu Woyera, anawona ubwino wa Iwo, analawa za Iwo, analawapo za Mawu a Mulungu. . .” Mukuona izo? Palibe aliyense wa amuna amenewo, palibe mmodzi wa iwo anayamba walolezedwa kuti apite uko. Iwo anawonongeka mu dziko lawo lomwelo, komwe kuno mu chipululu. Iwo sanapiteko konse, komabe iwo anali oyandikira mokwanira kuti alilawe Ilo, koma opanda chisomo chokwanira ndi chikhulupiriro kuti alitenge Ilo. Ndicho chimene izo ziri.

<sup>177</sup> Tsopano. Tsopano tamvetserani kwa munthu wokonedwa uyo yemwe analemba kalata iyi. Tiyeni tingowerenga ndime

yotsatirayo. Penyani miniti yokha. Mpenyeni Paulo. Tsopano tiyeni tiwerenge ya 7:

*Pakuti dziko... limamwa mu mvula yomwe imadza mowirikiza pa ilo, ndi kumeretsa masamba chakudya kwa iwo omwe amalilimira, zimalandira madalitso ochokera kwa Mulungu:*

*Koma izo zomwe zimabala minga ndi nthula zimakanidwa ndipo ziri pafupi ndi kutembereredwa; zomwe mapeto ake ndiwo kuti ziwotchedwe.*

178 Tsopano, mukuona zomwe iye akunena? Tsopano penyani. Panali funso ili apa; tsopano, ndiyeno ife titseka... Chinthu ichi chimakhala ngati chindipha ine kwa zaka.

179 Ine ndinapita ku msonkhano nthawi ina kumene anthu anali kuyankhula mu malirime ku Mishawaka, Indiana. Tsopano, ine ndiri patsogolo pa khamu langa lomwe. Inu mwawamvapo anthu amenewo... mwandimvapo ine ndikunena mbiri ya moyo wanga, ndi za munthu wachikuda yemwe anati, “Ndi uyu pano. Ndi uyu pano.” Tsopano, ine ndinakuuzani izo.

180 Koma zina za izo: Ine ndinawawona amuna awiri. Iwo anali... Mmodzi ankakhoza kupereka uthenga, mmodzi winayo kumatanthauzira izo. Wina akapereka uthenga, ndipo winayo ankatanthauzira iwo. Ndipo m’bale, iwo anali akulondola. Basi izi... ine ndinaganiza, “Ubwino wanga! Ine sindinayambe ndawonapo chirichonse chonga izo.” Ine ndinati, “Ine ndiri pakati pa angelo.” Ine ndinaganiza, ine sindinayambe ndawonapo chirichonse... Wina anali kuyankhula, ndipo winayo...

181 Ndipo ine ndinakhala kumbuyo uko, ngati kamlaliki kachikulire, inu mukudziwa. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]... amuna onsewo nthawiyina ndipo ndinagwirana nawo chanza. Ine ndinali ndisanawawonepo amuna oterowo mu moyo wanga. Iwo ankakhoza kuyankhula uthenga, ndipo winayo ankakhoza kuzitanthauzira izo. Ndipo mai, mai! Izo zinali zodabwitsa! Mmodzi ankakhoza kuyankhula ndipo winayo nkutanthauzira. Onsewo... Ndipo iwo ankanosanduka oyera ngati choko pamene iwo ankaimitsa manja awo mmwamba. Ine ndinaganiza, “O mai, mai, kodi ine ndakhala ndiri kuti moyo wanga wonsewu. Ichi ndicho chinthucho!” Ine ndinati, “Mai, Achipentekoste ali kulondola.” Uko nkulondola ndendende.

182 Ine ndinali ndisanawonepo zochuluka koma basi zomwe zinali za cha komwe kuno, kumene... Mwinamwake akazi angapo ali ndi utumiki kwina wake. Ndipo iwo amakhala akukangana; ndipo wina kumamutcha mzakeyo, “chisa cha akhungubwe,” ndipo, inu mukudziwa, basi monga choncho, kukhala ngati kumakangana wina ndi mzake. Osati kuwanyozetsa akaziwo tsopano kapena chinachake ayi, koma

basi. . . Izo—izo zinali mchikalidwe chofooka. Ngati aliyense wa inu. . . Inu mukukumbukira, M'bale Graham. Inu munali mnyamata wamng'ono chabe pa nthawi imeneyo. Ndipo chotero, umo ndi momwe izo zinaliri.

Ndipo ine ndinamvetsera kwa izo, ndipo ine ndinaganiza, "O, mai, ine ndakumanizana ndi angelo."

<sup>183</sup> Tsiku lina ndikubwera kuzungulira pa ngodya ya nyumbayo, cha mu tsiku lachiwiri, ine ndinakomana naye mmodzi wa amunawo. Ine ndinati, "Inu muli bwanji, Bwana?"

Iye anati, "Iwe uli bwanji?" Iye anati, "Kodi. . . Dzina lako ndiwe ndani?"

Ndipo ine ndinati, "Branham."

Iye anati, "Ukuchokera kuti iweyo? Kuno?"

Ndipo ine ndinati, "Ayi, ndine wochokera ku Jeffersonville."

Iye anati, "Chabwino, izo nzabwino. Kodi ndiwe Wachipentekoste?"

Ine ndinati, "Ayi, bwana, ine sindiri." Ine ndinati, "Ine sindimavomereza basi njira ya Chipentekoste yolandirira Mzimu Woyera," ine ndinati, "komabe," ine ndinati, "ine ndiri kuno kuti ndiphunzire."

<sup>184</sup> Iye anati, "Chabwino, izo nzabwino mwamphamvu." Ndipo ndikuyankhula ndi iye, ndikuwugwira mzimu wake (monga mkazi pa chitsime), iye anali Mkristu weniweni. M'bale, ine ndikutanthauza iye ankamvekera bwino ndithu. Iye anali wabwino. Tsopano, inu nonse. . . Ndi angati omwe mwakhala mulipo mu misonkhano yanga ndipo mwaziwonapo zinthu zimenezo zikuchitika? Inu mukuona? Ndipo bamboyo anali wabwino mwangwiwo. Chotero ndiye, ine—ine ndinaganiza, "Apo! Mai, ndi zodabwitsa bwanji!"

<sup>185</sup> Pafupi usiku umenewo, madzulo nthawiyina, ine ndinakomana naye winayo. Ine ndinati, "Inu muli bwanji, Bwana?"

Iye anati, "Iwe uli bwanji? Dzina lako ndiwe ndani?" Ndipo ine ndinamuza iye. Ndipo iye anati, "Kodi. . . Kodi—ndiwe wa Chipentekoste?"

Ine ndinati, "Ayi, bwana, osati kwenikweni wa Chipentekoste, ine sindikuganiza." Ine ndinati, "Ine ndangobwera kuno kuti ndidzaphunzire."

Iye anati, ine ndinati, iye anati, "Iwe unayamba walandirapo Mzimu Woyera?"

Ine ndinati, "I—ine sindikudziwa." Ine ndinati, "Malingana ndi zonse zomwe inu nonse muli nazo, ine ndikulingalira ine ndiribe."

Ndipo iye anati, "Unayamba wayankhulapo mu malirime?"

Ine ndinati, “Ayi, bwana!”

Iye anati, “Ndiye iwe sunayambe wakhala nawo Iwo.”

<sup>186</sup> Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine—ine ndikulingalira uko nkulondola.” Ine ndinati, “Ine sindikudziwa. Ine ndangokhala ndikulalikira pafupi zaka ziwiri, kucheperapo,” ndipo ine ndinati, “Ine sindikudziwa zochuluka kwambiri za Iwo.” Ine ndinati, “Mwinamwake ine sindikudziwa.” Ine ndinati, “Ine sindikukhoza kuzimvetsa. . .” Chifukwa chimene, ine ndinali kuyesera kuti ndimugwirebe iye apo (mwaona?), kuti ndiugwire uwo. Ndipo pamene ine ndinatero, ngati ine ndinayamba ndakomanapo ndi wachinyengo, apo panali mmodzi wa iwo. Mkazi wake anali wa mutu-wakuda; ndipo iye anali akukhala ndi mkazi wa mutu wa bulondi, anali nao ana awiri ndi iye; ndipo nkumayankhula mu malirime, kumawathanthauzira iwo mwangwiro basi monga izo zikanakhoza kukhalira. Ndipo ine ndinati, “Tsopano, Ambuye, kodi ine ndalowa mu chiyani?” Kuchokera kwa angelo, ine sindimadziwa kuti ndinalowa mu chiani. Ine ndinati, “I—ine—ndine wachikhazikitso; izo ziyenera kukhala Baibulo. Izo ziyenera kukhala molondola. Pali chinachake chalakwika penapake, Ambuye. Izo zingakhale motani?”

<sup>187</sup> Ine ndinapita ku msonkhano usiku umenewo, ndipo Mzimu uwo umakhoza kugwa; ndipo m’bale, iwe umakhoza kuwumverera iwo, kuti Iwo unali Mzimu Woyera. Inde, bwana! Ngati Iwo sunali, Iwo umachitira umboni ndi mzimu wanga kuti Iwo unali Mzimu Woyera. Ndipo ine ndinangokhala mlaliki wamng’ono, ndipo sindinkadziwa momwe, mochuluka za kuuzindikira mzimu. Koma ine ndinali nditakhala apo. Ndipo ine ndikudziwa kuti Mulungu yemweyo amene anandipulumutsa ineyo, uko kunali kumverera kofanana. . . Ndinamverera ngati ndinali kupita kudutsa pa denga, uko kunali kumverera kodabwitsa chotero mu nyumba imeneyo. Ndipo ine ndinaganiza. . .

<sup>188</sup> Pafupi mazana fifitini a iwo kumeneko. Ndipo ine ndinaganiza. “Mai, o mai!” Magulu awiri kapena atatu a iwo anali atakomana palimodzi. Ndipo ine ndinaganiza, “Ndiiti, mai! Zikukhala motani izo? Tsopano, Mzimu waukulu uwo mu chipinda ichi ukugwa monga choncho; ndipo kuno, tayang’anani pa ichi chiri kupitirira umo, amuna awo akuyankhula mu malirime, kutanthauzira, kupereka uthenga mwangwiro—ndipo mmodzi wa iwo wachinyengo ndi winayo munthu weniweni wa Mulungu.” Ndipo ine ndinaganiza, “Tsopano, ndine wosokonezeka yense. Ine sindikudziwa choti ndichite.”

<sup>189</sup> Chabwino, mwamsanga zitachitika izo, mzanga wabwino kwa ine, M’bale Davis (inu mukumudziwa), anayamba kumati ine ndinali chipapeti. Ndicho chidole cha msungwana, inu mukudziwa. Ndipo chotero, ine ndinali wosakwatira, ndipo

chotero ine...Iye anayamba kumapitiriza ndi ine, ndiyeno kumapitiriza, kumakhala ngati kumandinyoza ine.

<sup>190</sup> Ndipo ife tinkakhala ndi zapang'ono...Ndipo amayi anu ndi tonse ife tinkakhala ndi misonkhano yaing'ono ku malo osiyana. Kachisi sanali—sanali akuyenda nthawi imeneyo, ndipo ife tinali kukhala ndi misonkhano yaing'ono mu malo osiyana. Ndipo potsiriza tsiku lina, kachisi atamangidwa kale, zaka zambiri kenako, ine ndinapita uko ku Chigayo cha a Green ku mphanga yanga kuti ndikapemphere, chifukwa M'bale Davis anali atanena zinthu zina zoipa pa ine mu—mu—mu pepala yake. Ine ndinkamukonda iye. Ine sindinkafuna kuti pachitike kanthu kena, ndipo ine—ine ndinapita uko kuti ndikamupempherere iye. Ndipo ine ndinapita uko, ndipo ine ndinakalowa mu mphanga. Ndipo ine ndinakhala mkati mmenemo pafupi masiku awiri. Ndipo ine ndinati, “Ambuye, mukhululukireni iye. Iye—iye sakutanthauza—sakutanthauza izo.” Ndipo ine ndinaganiza, “Inu mukudziwa...” Ine ndinangopezeka ndikuganiza za Lemba.

<sup>191</sup> Ndipo ine ndinatuluka. Ndipo uko kunali chipika (chipika chimenecho chikadali pamenepo, ndinali pa icho osati kale litali) ukamatsika phirilo ndipo pali kanjira kakang'ono kamene kamabwera mozungulira kuchokera ku khwawa. Ndipo ine ndinangokhala pa chipikacho, ndikuyang'ana kudutsa mapiri mmbuyo—kumbuyo uko, ndipo ndinaika Baibulo langa apo monga choncho. Ine ndinaganiza, “Inu mukudziwa...” Ine ndinali ndikuganiza za Lemba: “Wosulamkuwa, iye wandichitira ine zoipa zambiri, ndipo wanena zinthu.” Inu mukudziwa...Ine ndinaganiza, “ine ndikukhulupirira ine ndingozwiwenga izo.” Ine ndinalitsegula Baibulo, ndipo ine ndinati, “Chabwino...” Ndinaipukuta nkhope yanga, ndipo mphepo inawomba, ndipo iyo inalitsegula ilo ku Aheberi 6. “Chabwino,” ine ndinati, “apo si pamene izo ziri.” Ndipo ine ndinaliyika Ilo mmbuyo monga chonchi. Ndipo mphepo inakupiza kachiwiri ndipo inalitsegula Ilo kachiwiri. Ndipo ine ndinati, “Tsopano, izo ndi zachilendo, mphepo kumalikupiza ilo mobwereza monga choncho.” Chotero ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndikukhulupirira ine ndiziwerenge izo.” Ndipo linati:

*Pakuti ndi zosatheka kwa iwo amene anawalitsidwirapo kale,...anapangidwa kukhala ogawana nawo za Mzimu Woyera, ndipo analawa...za Mawu a Mulungu, ndi zinthu za dziko likudzalo.*

Ine ndinaganiza, “Chabwino, ine sindikuwonapo kanthu ndi izo.” Ndinaziwenga izo mpaka mmusi, mutu wonsewo. Munalibe kalikonse umo. Ine ndinati, “Chabwino, ndizo—izo zikukhazikitsa icho kwa izo.” Ndipo ine—ine ndinaziwona izo monga chonchi, ndi mobwereza ilo linapitapo kachiwiri. Ndipo ine ndinalitenga Ilo, ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino,

kodi nchiani izo?” Ine ndinapitiriza kuziwerenga izo, ndi kuziwerenga izo, ndi kuziwerenga izo. Ine ndinati, “Chabwino, ine sindikukhoza kuzimvetsa.” Ndiye ine ndinapitirira . . . Ndipo ine ndinawerenga mpaka pansi:

. . . ziri zosatheka *kwa iwo omwe anawalitsidwapo kale, . . .*

Izo zinafika mpaka pansi pa malo pamene iwo anati:

*Ndipo dziko lapansi . . . limamwa mu mvula yomwe imadza mowirikiza pa ilo, kuti lizibala zomera chakudya kwa iwo omwe amazilimira, limalandira madalitso ochokera kwa Mulungu:*

*Koma izo zomwe zibala minga ndi nthula zimakanidwa, ndi . . . kuyandikira ku themberero; zomwe chiweruzo chake ndi kuti ziwotchedwe.*

<sup>192</sup> Ine ndinati, “Ndikudabwa chomwe izo zikutanthauza?” Ine basi . . . Tsopano, ine sindinali kuganiza za kanthu pamwamba apo. Kumangoganiza izo. Ndipo nthawi yomweyo pamene ine ndinali nditakhala pamenepo, ine ndinkaganiza Ambuye akanati andipatse ine masomphenya okhudza M’bale Davis ndi iwo kumusi uko. Ndipo ine ndinali nditakhala apo; ine ndinayang’ana, ndipo ine ndinawona chinachake chikutembenezika modutsa kumitengoko patsogolo pa ine. Ndipo ilo linali dziko likutembenezika. Ndipo ine ndinawona ilo lonse linali litalimidwa, linkangowoneka ngati kuti linali lonse litatipulidwa konse. Ndipo Mwamuna anapita uko ali ndi—c—chinthu chachikulu kwambiri patsogolo pa Iye chodzaza ndi mbewu, ndipo Iye anali akufesa mbewu njira yonse kudutsa pa dziko lapansi pamene Iye anali kupita. Ndipo Iye anapita kuzungulira kobisika kwa dziko lapansi, ndipo Iye anachoka ku nkhope yanga. Ndipo mwamsanga pamene Iye anachoka ku nkhope yanga, apa panadza bambo wooneka—mwaukathyali, atavala zovala zakuda, akupita chozungulira monga chonchi, akuti [M’bale Branham akupanga phokoso kuti afotokeze—Mkonzi.] akuponya mbewu zoipa [M’bale Branham akubwereza phokosolo—Mkonzi.] Ndipo ine ndinkaziyang’ana izo, ndipo pamene dziko linkapitirira kutembenezika . . .

<sup>193</sup> Patapita kanthawi tirigu anatulukira. Ndipo pamene tirigu anatulukira, kuchokera umo kunabwera mitungwi, nthula, ndi minga, ndi udzu wonunkha, ndi chirichonse chikumera, thengo lamkaka, ndi chirichonse chikumera mu tirigumu. Ndipo izo zonse zinali kumerera palimodzi. Ndipo apo panadza chilala chenicheni, choipa, ndipo tirigu wamng’onooyo anali atatukula mutu wake monga choncho, ndipo mtungwi waung’onowo, ndi nthula, minga, izo zinali zitatukula mitu yawo. Udzu uliwonse kumangoti [M’bale Branham akupanga phokoso la wefufu—Mkonzi.] kumapuma monga choncho. Iwe umakhoza basi kumazimva izo. Ndipo izo zinali kuitanitsa mvula, mvula.

194 Ndipo patapita kanthawi, motsatira kunadza mtambo waukulu kwambiri, ndipo madzi anangokhuthukira pansi. Ndipo pamene iwo anagwera pamenepo, tirigu uja analumphira mmwamba ndi kuyamba kufuula, “Ulemerero, Aleluya, Ambuye Alemekezeke!” Mmwamba unalumphira udzu waung’ono wonunkha ndi kumafuula, “Ulemerero, Ambuye Alemekezeke, Aleluya!” Minga ndi zonse izo, zikuvina mozungulira mmunda wonsewo zikufuula, “Ulemerero, Aleluya, Ambuye alemekezeke!”

Chabwino, ine ndinati, “Ine sindikukhoza kuzimvetsa izo.”

195 Masomphenya anandichokera ine; ndiye ine ndinagwera mmbuyo pa zija kachiwiri: “Nthula zomwe zayandikira kuti zikanidwe” Ndiye ine ndinazimvetsa izo. Yesu anati, “Mvula imagwera pa olungama ndi osalungama.” Munthu akhoza kukhala mu msonkhano, akhoza kuyankhula ndi malirime, akhoza kufuula ndi kumachita chimodzimidzi monga onse amene ali ndi Mzimu Woyera weniweni ndipo nkusakhalabe ali mu Ufumu wa Mulungu. Ndi kulondola ndendende. Kodi Yesu sanati, “Ambiri adzaima mu tsiku limenelo nati, ‘Ambuye, kodi ine sindinatulutse ziwanda mu Dzina Lanu; kodi ine sindinalosere (kulalikira) mu Dzina Lanu; kodi ine sindinachte ntchito zambiri zazikulu mu Dzina Lanu?’” Yesu anati, “Chokani kwa Ine, inu ochita kusaweruzika, ine sindinakudziweni nkomwe inu.” Nanga bwanji zimenezo?

196 Pano pali ndendende chomwe izo zikutanthauza apa. Mwaona? Iwo analawa mvula yabwino yochokera Kumwamba. Koma pakuyamba pomwe, iwo anali olakwika. Pakuyamba pomwe zolinga zawo sizinali zolondola; zokhumba zawo sizinali zolondola. Ndiko, inu simungakhoze kudziwa. Inu mukudziwa, pa kukolola iye anati, “Kodi ine ndipite uko ndi kukazizula zonsezo?”

197 Iye anati, “Zisiyeni izo zikulire palimodzi, ndipo pa tsiku limenelo minga izi ndi nthula zidzawotchedwa palimodzi, ndipo tirigu adzapita ku nkhekwe.” Tsopano, iwe ungasidziwe bwanji kuti minga ndi iti, kapena nthula ndi iti, kapena tirigu ndi uti? “Ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.” Inu mukuona, M’bale, Mlongo, mtengo wabwino sungakhoze kubala chipatso choipa. Ziribe kanthu, penapake potsatira msewuwu, izo zidzakugwirani inu. Kotero, inu muli kufunafuna ubatizo wa Mzimu Woyera . . . Ndine wokondwa yense yemwe analemba iloyo. Mukuona?

198 Tsopano, okhulupirira ammalire awo kumbuyo uko, iwo anali limodzi nawo. Iwo anali atadulidwa ndi mdulidwe wao. Iwo anapita mpaka ku dziko lomwe Mulungu analilonjeza, ku malire komwe a ilo. Anthu ambiri amayenda mpaka ku malire amenewo. Iye amayenda mpaka ku ubatizo wa Mzimu Woyera womwe ndi kuwukana iwo. Iye samafuna kuti awulephere iwo.

Iye amayenda kumene mpaka ku Lemba lomwe la ubatizo mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kutembenezira nsana wake, ndi kukana kuti alephere kuziwona izo.

<sup>199</sup> Mulibe Lemba limodzi mu Baibulo lonse pamene wina aliyense anayamba wabatizidwapo mu dzina la Atate, Mwana, Mzimu Woyera, palibe Lemba limodzi. Mpingo wa Katolika unayambitsa izo, zinatuluka mwa Lutera, mpaka kwa Wesile, ndipo azikoka izo kudutsa mpaka kuno. Kulondola ndendende. Koma dongosolo la Mwamalemba ndi Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Umenewo ndiwo ubatizo wautumwi. Iwe sungakhoze kuchita izo ndi kumakhalabe mu chipembedzo. Ndiko kulondola.

<sup>200</sup> Tsopano, inu mukuona zinthu izo? Ubatizo wa Mzimu Woyera, mpatso za Mzimu, zinthu zomwe Mulungu amazibweretsapo... Chipatso cha Mzimu ndicho chikondi, chimwemwe, kuvutika-motalika (o, inu mukuti, “Koma M’bale Branham, Mulungu adalitsike, ndine wovutika-motalika.” Izo zikuwoneka ngati choncho. Ine ndinapita ku Ohio kuno osati kale litali, ndipo winawake anandifunsa ine, analemba kalata kunoko ndipo anandifunsa ine ngati ine ndimawabatiza anthu mu Dzina la Yesu Khristu. Ine sindinanene konse mawu. Iwo anazipeza izo mulimonse, ndipo azitumiki sikisitini ogwirizana anachokako. Ndiko kuvutika-motalika sichoncho uko!)—kuvutika-motalika, ubwino, kufatsa, kudzichepetsa, kupirira, ndi Mzimu Woyera. Mwaona?

<sup>201</sup> O, M’bale, Mlongo, ndife—ife tiri pa Kadeshi-barnea. Inu mukulawa tsopano. Usiku watha Mzimu Woyera unagwera pa ife, unabwera mwa ife, kulowa monga mphepo yankokomo. Iyo inadzakhala pa ambiri a inu. Lero atumiki akhala akuyendera makomo kuno ndi uko, kumakasanjika manja ndi kumawapempherera iwo omwe akufunafuna Mzimu Woyera. Musati inu mutenge cholowezammalo. Musati muzitenga mtundu wina wa phokoso. Musati inu muzitenga mtundu wina wa kugirigisha. Inu mudikire pamenepo mpaka Mulungu atakuwumbani inu ndipo atakupangani inu cholengedwa chatsopano, atakupangani inu munthu watsopano. Inu mukuulawa Iwo tsopano, kungoulawa Iwo, koma mulole Nkhunda ikutsogolereni inu mpaka ku tebulo, ndi—ndipo Mwanawankhosa ndi Nkhunda zikhale panso limodzi, ndi kumadya kwanthawizonse pa Mawu a Mulungu. Pakuti Iwo adzaima pamene padzakhala kulibe miyamba kapena dziko lapansi; Mawu a Mulungu adzakhala alipobe. Izo ndi zoon.

<sup>202</sup> Chonde musati muziganiza kuti ndine wotengeka. Ngati ine ndakhala ndiri, ine sindimatanthauza kutero. Ngati ine... ine ndikuyembekeza ine ndawayankha mafunso awa; ine ndatero, mwa kupambana kwa kudziwa kwanga.



203 Ndipo chotero, mu Aheberi 6, ngati inu muti muwone, Paulo akuyankhula kwa Ahebri omwe ankati, “Chabwino, ife tipita nanu inu motalika chonchi.” Iwo azibwera. Inu mukuona? Nati, “Tsopano, inu muli. . .” Iwo amene abwera apa ndipo alawa.

204 Ine ndinangopezeka ndikuyang’ana mmbuyo mu chipindamu. Kuti ndikusonyezeni inu umboni wa Mulungu Wamoyo. Ine ndikuyembekeza sindikumupanga munthu uyu kuwonekera. Ine ndinabwera muno ndikuchokera ku msonkhano osati kale litali, ndipo ndinabwera kuno, ndipo ndinalengeza kwa inu kuti mzanga wabwino, bwanawe wa ine, mzanga wosaka naye, bambo yemwe wakhala wabwino kwa ine, munthu yemwe anafikako ku mpingo wanga, ndipo anakhala ali m’bale wanga; ine ndinkamutcha iye Busty. Dzina lake ndi Everett Rodgers; ankakhala ku Milltown. Ndi angati akukumbukira ine nditabwera kuno ndi kudzalengeza izo? Iye anali atagona muno mu chipatala; madokotala anamuchita iye opareshoni, anamutsegula iye, ndipo anali wodzaza ndi khansara iwo anangomusoka iye. Anati, “Iye azilaza pakali pano; mu masabata angapo iye akhala atapita; izo zikhala zonse zomwe ziti zidzakhalepo kwa izo. Iye akhala atatsirizika, ndizo zonse.”

205 Inu mukukumbukira momwe ine ndinaimira kuno pa nsanja, ndinkamupempherera iye? Ndinapita kumusi uko ndipo ndinapita mu chipinda, chinachake chinali chikundidya mu mtima wanga. Ine ndinayenda kulowa mpaka mu chipinda, ndipo mwamsanga pamene ine ndinamutulutsa aliyense kunj chotero ine ndikanakhoza. . . M’bale Everett anali atagona apo. Ndipo inu mukumbukira izi. Ine ndinalowa mkatimo; ine ndinati, “M’bale—M’bale Busty.” (Ine ndinkamutcha iye Busty.)

206 Kale litali pamene ife tinali ndi misonkhano ya ku msitu lamdima kumusi uko, Amethodisti onse awo kumeneko pa phirilo (Gertie, mmodzi wa iwo), anazemberako, ankasuzumira mu msitu wa mpesa kuti awone zomwe ine ndikanati ndinene, ndi monga choncho, kuwopa kuti mpingo wa Methodisti ukanati uwachotse iwo. Ndiyeno, ine ndinapita ndipo ndinali ndi masomphenya kumeneko, ndipo ine ndinawona nyama itawunjikidwa mu chitini. Ine ndinagwira mulu wa nsomba ndipo ndinazimangirira izo pa, ndinaziyika—ndinaziyika izo pa zomangira izi, ndipo ine ndinazimanga zingwezo. Ndipo pamene ine ndinayang’ana. . . Ndipo izo zonse zinali mu masomphenya; ine ndinasiya—ndinalisiya gulu la anthu ataima pansu pa msituwo usiku umenewo ndipo ndinapita pamwamba pa phiri kwa M’bale Wright. Ndipo iwo samakhoza kundipeza nkomwe ine mmawa wotsatira. Ine ndinati, “Musati wina wa inu. . .”

207 Pamene ine ndinali nditaima apo ndikulalikira, apa panadza Kuwala kuja; Lawi la Moto lija linapachikika apa pomwe patsogolo pa ine ndipo linati, “Choka kuno ndipo upite ku tchire; ine ndikayankhula kwa iwe.” Izo zinali pa tsiku lomwelo, tsiku

lotsatira pamene iwo anandipeza ine pa phiri apo. Ndipo ine ndinali ndiri pamwamba apo; ine ndinabisa galimoto yanga mu udzu, ndipo ndinali ndiri pa phirilo ndikupemphera usiku wonse ndi tsiku lonse lotsatira. Ena a iwo anabwera uko, anaipeza galimotoyo ndipo anabwera pamwambapo uko. . . Ilo linali tsiku limene M'bale Graham Snelling, kuno, analandira Mzimu Woyera ndi kuitana kuti alowe mu utumiki.

<sup>208</sup> Pamwamba apo ku mbali ya phiri pamene ine ndinali nditagona apo, ndipo Iye—Iye anandiuza ine zinthu zosiyana zoti ndizichita ndi kuyankhulana kumene ife tinali nako limodzi. Iye anapereka masomphenya oziwona nsomba izi zitamangidwa apo, anati, “Uwu ndiwo mpingo wako waku Milltown.”

Ndipo anai kapena asanu za izo zinagwapo; ndipo ine ndinati, “Ndi ndani uyo?”

Anati, “Mmodzi wa iwo ndi Guy Spencer ndi mkazi wake. Mmodzi winayo ndi Spencer wina uko, ndi awo.” Ndipo Iye anawatchula ena osiyana, omwe akanati adzagweko.

<sup>209</sup> Ine ndinawauza iwo; ine ndinati, “Asati aliyense wa inu adye.” Akazi anga ndi ine sitinali. . . Apo panali ife tisanakwatirane; ndipo iye anapita kwawo kuti akakhale utali wa usiku wonse ndi Mlongo Spencer, mkazi wodabwitsa. Mwamuna wodabwitsa, Guy Spencer ndi bambo wabwino basi yemwe anaimapo mu chikopa cha nsapato. Ndipo iye—ndipo iye anapita kumusi uko, ndipo Opal anati, “Tsopano, taona. . .” Kwa Meda, iye anati, “Tsopano, Meda, ine ndikukhulupirira M'bale Bill.” Iye anati, “Koma pamene Opal akhala ndi njala, iye amayenera kukhala ndi nyama ndi mazira.” Kotero iye anapita uko, ndipo anakakazinga nyama yake ndi mazira, ndipo anakhala pansu kuti azidya izo, ndi kuyamba kunena mdalitso, ndipo anatsamira pa tebulo, akulira, sanakhoze kuzigwira izo. Ndiye iwo anabwera akusaka.

<sup>210</sup> Ndipo pamwamba pa phiri paja tsiku limenelo, Iye anandiuza ine ndendende zomwe zikanati zidzachitike. Iye anati, “Awa achoka, kenako awa achoka.” Koma Iye anali ndi gulu lalikulu la nyama ya nchitini. Iye anati, “Uyisunge iyi kuti idzagwiritsidwe ntchito mtsogolo kwa anthu aku Milltown.” Ndipo usiku wina pamene ine ndinamumva M'bale Creech. . . Iye anali muno usiku watha. Ine sindiri. . . M'bale Creech, kodi inu muli muno usikuuno? Pamene M'bale Creech anabwera kwa ine, anandiyimbira ine, ndipo Mlongo Creech, akulira; bambo ake anali atagona pamenepo. Anati, “M'bale Bill, musati mumuuze iye. Iye akufa.” Anati, “Iye wadyedwa ndi khansara; madokotala anamutsegula iye, ndipo iye wangodzaza ndi khansara monga iye akanakhoza kukhalira.” Ndipo Will Hall (ndipo nonse inu mukumukumbukira iye), pamene dokotala yemweyo anamutsegula iye ndipo iye anali atadzaza ndi khansara. . . Ine ndinayamba kupita kukasaka agologolo mmawa umenewo,

ndipo ine ndinawaona maapulo aja atapachikika mu chipinda. (Inu mukuikumbukira nkhani iyo ya izo?) Ndipo uko bamboyo akadali moyo lero. Izo zakhala ziri zaka zapitazo. Iye ndi M'bale Busty anali abwenzi.

<sup>211</sup> Ndipo ine ndinapita uko ku chipatala, chipatala chatsopano (ine ndaiwala chomwe iwo amachitcha icho, kumeneko mu New Albany)—chipatala chatsopano. Ndipo ine ndinapita uko kuti ndikamuwone Busty; ndipo pamene ine ndinalowa mu chipinda, ine ndinati, “M'bale Busty.”

Iye anati, “M'bale Bill.” Anandigwira dzanja langa ndi dzanja lokalamba lalikulu ilo; msilikali wakale wa Nkhondo Yoyamba ya Dziko Lonse, osati nkunena izo iye alipo, koma ndi mtima wabwino basi wonga uwo womwe unayamba wagunda pansi pa malaya akale a buluu. Iye analigwira dzanja langa. Ine ndakhalapo mu nyumba yake; ndadyapo mu nyumba yake; ndagonapo mu nyumba yake, basi ngati ndinali m'bale wake. Ana ake ndi onse, ndife basi—monga abale amagazi basi. Munthu wabwino.

<sup>212</sup> Ndipo iye...Koma iye sanabwere nao konse Ambuye mwakuya. Iye...ine ndinamubatiza iye mu Dzina la Yesu Khristu. Koma tsiku limenelo pamene mlaliki wa Chimethodisti uja anati, “Aliyense yemwe anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu, chokani pansi pa hema wanga.” Izo zinali zabwino. George Wright ndi iwo anatulukamo. Madzulo amenewo ine ndinapita uko kuti ndikawabatize mu Dzina la Yesu Khristu ku Totten Ford. Gulu lake lonse linalowa mmadzi ndipo linabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Chotero ine ndinali kungopitirira. Izo zinali zabwino. Mulungu akakhala ndi inu, ndani angakhale mokutsutsani inu? Ine sindikudziwa nkomwe komwe munthuyo anapita, chomwe chinachitika kwa iye.

<sup>213</sup> Komabe, ine ndinalowa mu chipatala. Uko kunali Busty atagona pamenepo ali wodzaza ndi khansara, madokotala sakanakhoza ngakhale, sanachite kanthu koma kungomumanganso iye palimodzi. Busty ananena kwa ine; iye anati, “M'bale Bill, izi ziri kwa cholinga. Chinachake chachitika.”

Ine ndinati, “Inde, Busty.” Ndinayamba kuumverera Mzimu umenewo monga choncho nkokomo wamphepo yomwe ine ndakhala ndikuikamba, inu mukudziwa, ikubwera mmenemo.

Iye anati...Pamene ine ndimalowa muno, panali utawaleza pa ngodya iyo, utaima mu ngodya imeneyo. Utawaleza ndi pangano; pangano la Mulungu. Mulungu anapanga pangano ndi ine pa phiri lija tsiku lija. Ndinaika manja anga pa M'bale Busty ndipo ndinamupempherera iye.

Madokotala akuti, “Iye azilalapo. Iye azingotsika pansi. Palibe kanthu koti nkuchita...Iye akhala atapita mu masiku angapo okha.” Ndipo Busty Rodgers...Awo akhala ali masabata

ndi masabata ndi masabata apitawo, ndipo Busty Rodgers, wakhala mmbuyo momwe muno mu mpingowu usikuuno, wathanzi ndi wojintcha monga ine ndinayamba ndamuwonapo iye akuwoneka mmoyo wanga. Taimirira, M'bale Busty. Ndi uyo apo. Tiyeni timupatse Mulungu matamando, aliyense.

Anasonkana mu chipinda,  
 Akupemphera m'Dzina Lake.  
 Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,  
 Mphamvu ya utumiki inadza.  
 Chomwe anawachitira apo,  
 Akuchitirani chomwecho.  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."

Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."  
 (Aleluya!)  
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."

Anthuwa samadzinenera,  
 Kudzitama ndi za mdziko,  
 Onse alandira Pentekoste,  
 Abatizidwa m'Dzina la Yesu.  
 Akuwauza onse kutali,  
 Mphamvu yake ndi yomweyo.  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."

Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
 Ndine wokondwa kuti "ndine mmodzi wawo,"  
 (Aleluya!)  
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."

Bwera m'bale, funa dalitso'li  
 Likutsuka mtima mwako,  
 Liyambitsa mabelu a chimwemwe,  
 Liyatsa moyo wako.  
 O, ukuyaka mu mtima mwanga,  
 Ulemerero ku Dzina Lake.  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."  
 (Tiyeni tiyimbe iyo!)

O, mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."  
 (Aleluya!)  
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
 Ndine wokondwa kuti, "Ndine mmodzi wawo."  
 (Ndi angati ali mmodzi wawo, kwezani dzanja lanu? O, mai! O, momwe ine ndiriri wokondwa kuti ndine mmodzi wawo.)

Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”  
(Aleluya!)

Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

Anali mchipinda chapamwamba,  
Akupemphera mu Dzina Lake.  
Nabatizidwa ndi Mzimu Woyera,  
Mphamvu ya utumiki inadza.

Zomwe anawachitira apo,  
Akuchitirani zomwezo.  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”  
(Aleluya!)

Mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

Tsopano, pamene ife tikuimba kolasi imeneyo kachiwiri, ine ndikufuna aliyense wa inu kuti atembenuke, ndi kugwirana manja ndi winawake pafupi ndi inu, ndi kuti, “Kodi ndinu mmodzi wawo?” Mukuona? Chabwino.

O, mmodzi wawo (ine ndikudziwa inu muli, M'bale...?.?.?.ine ndikudziwa inu muli, M'bale...?.?.?) [M'bale Branham akugwirana chanza ndi iwo apafupi ndi iye—Mkonzi]. . . mmodzi wawo.

O, mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

<sup>214</sup> O, kodi sindinu okondwa ndinu mmodzi wawo. Ndi angati akufuna kuti akhale mmodziyo, kwezani dzanja lanu? Chabwino. Tsopano, ine ndikuti ndikuimbireni inu iyi:

Ndiye bwera m'bale, funa dalitso'li  
Likutsuka mtima mwako,  
Liyimbisa mabelu a chimwemwe,  
Liyatsa moyo wako.

O, ukuyaka mu mtima mwanga,  
Ulemerero ku Dzina Lake.  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

O, mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”  
(Aleluya!)

Mmodzi wawo, mmodzi wawo,  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

<sup>215</sup> Mukukumbukira zomwe msungwana wamng'ono ananena Petro, “Kodi sindiwe mmodzi wa iwo?” Ndine wokondwa kwambiri, sichoncho inu? Inu mukudziwa, Petro ananena pa tsiku la Pentekoste, “Ichi ndi Chija!” Tsopano, ine ndanenapo

nthawizonse, “Ngati *ichi* si Chija. Ndine wokondwa kuti ine ndiri ndi *ichi*, ndikuyembekeza Chijacho kuti chibwere.” Ndiko kulondola. Ine ndikukondwa ndi *ichi*.

Ndine mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”  
O, mmodzi wawo, mmodzi wawo;  
Ndine wokondwa kuti, “Ndine mmodzi wawo.”

<sup>216</sup> O, kodi izi sizodabwitsa, kukhala limodzi mu malo a Mmwambamwamba mwa Khristu Yesu, kuyanjana limodzi ndi Mzimu, kuyanjana pa Mawu, kumayankhula za zinthu zabwino ziri nkudza. Ndi zabwino kwambiri. Ndine wokondwa kwambiri podziwa zimenezo, sichoncho inu? Kodi sindinu okondwa ndinu Mkhristu? Kodi sindinu okondwa machimo anu ali pansi pa Magazi? Iye akhala akubwera limodzi la masiku awa, ndipo ife tidzakhala tikupita ndi Iye. Ndiye taganizani, ukalamba wonse udzagwa kuchoka pa ife; matenda onse, kusautsika konse, moyo wonse wachivundi udzasintha. O, mai! Ine ndikhoza kungoganiza za abale okondedwa achikulire omwe anaima pano. Ine ndikukumbukira... Ndi angati akumukumbukira Rabbi Lawson? Mai, pafupi nonse inu. Ine ndikukhoza kumuwona iye atapachika ndodo yakale ija apa pomwe. Ndipo ine ndimakhala ndiri kumbuyo uko. Iye amakhoza kumaimba nyimbo yaing’ono iyi... (Miniti yokha Teddy, M’bale.) Ine ndiyesera, ndiwone ngati ndingakhoze kupeza kuimba kwa iyo. Ine sindikudziwa.

Likundiyembekeza ine mawa lokondwa,  
Pamene zipata za ngale zidzakankhika  
nkutsegula kwambiri,  
Ndipo pamene ndidzawoloka chotchinga cha  
chisoni *ichi*,  
Ndidzakupama ku mbali inayo.

Tsiku lina kupyola momwe chivundi  
chingadziwire,  
Tsiku lina, Mulungu yekha akudziwa zoti ndi  
kuti ndi liti,  
Magudumu a moyo wachivundi onse adzaima  
nji,  
Ndiye ine ndidzapita kukakhala ku phiri la  
Zioni.

<sup>217</sup> Magudumu aang’ono awa omwe akugudubuzika mkati mwa ife—kuwona, kulawa, kukhudza, kununkhiza, ndi kumva, zokhudzira zazing’ono izi ndi magudumu omwe akugudubuzika mu moyo wachivundi uno, tsiku lina zidzaima nji. Ndiye ine, inemwini, ndi inu, tidzapita kukakhala pa phiri la Zioni. O, ine ndikuzikonda izo, sichoncho inu? Podziwa kuti tiri nacho chitsimikizo chodala icho. Chabwino. Ndi angati akuidziwa nyimbo yathu yakale yobatizira? Tsopano, ife tisintha iyo. Tiyeni titenge nyimbo yathu yobalalikira:

Tenga Dzina la Yesu ndi iwe,  
Mwana wosauka ndi watsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukupatsa iwe  
chithonhozo,  
Tenga ilo kulikonse upita.

Tengani Dzina la Yesu limodzi nanu. Ingochitani izo, pamene inu mukupita. Chabwino, tonse palimodzi tsopano. Musati muiwale, 8 koloko mmawa makadi a pemphero azidzaperekedwa mu msonkhano. Msonkhano udzayamba ili hafu pasiti naini. Ine ndidzakhala ndikulalikira pa 10:00. Msonkhano wa pemphero kwa odwala udzayamba pafupi 11 koloko.

Mawa madzulo, mawa usiku udzakhala uthenga waulaliki ku kachisi. Ndipo mawa usiku, nonse inu omwe mwalapa machimo anu ndipo simunabatizidwe konse, kudzakhala... dziwe lomwe lidzakhala lotsegulidwa; ife tidzakhala tikuwabatiza anthu mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.

Aliyense limodzi tsopano, pamene ife tikuimba pamwamba pa mawu athu. M'bale Busty, inu simukudziwa momwe ine ndiriri wokondwa ndi wothokoza kwa Mulungu. Inu mukudziwa, iye anapita kwa dokotala. Ndipo iwo akundiiza ine kuti adokotala anayang'ana pa iye, ndipo sanali kudziwa basi zoti aganize. Iye sanali kukhulupirira kuti uyo anali mwamuna yemweyo. O, si chinsinsi zomwe Mulungu angakhoze kuchita. Kodi si kulondola uko? Chabwino.

Tenga Dzina (Iyimbeni iyo momveka!) la Yesu,  
Mwana wosaukawe;  
Lidzakusangalatsa iwe,  
Litenge kulikonseko.

Dzinalo (Lofunika!), O ndi lokoma!  
Chiyembekezo cha dziko;  
Dzina lofunika (O, lofunika!), ndi lokoma!  
Chisangalalo cha Kumwamba.

Chabwino. Ine ndikutembenezira msonkhano tsopano kwa abusa. Iwo akhala ali ndi mawu ena, kapena ayankhula kuti winawake atibalalitse ife, chirichonse chimene chiri pa mtima wao.



*Khalidwe Dongosolo ndi Chiphunzitso cha Mpingo*, Bukhu Loyamba  
(Conduct, Order And Doctrine Of The Church, Volume One)

Mauthenga awa a M'bale William Marrion Branham olalikiidwa ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito ndipo anadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Ndipo kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)



## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)